

## ***NDONDOMEKO ZA KUKONZEKERETSA***

### **HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE**

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

@Harvestime International Institute

## ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Ntchito Ka Bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	4
Mau Oyamba.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	7

## NDONDOMEKO ZA KUMEMEZA

1. Kukonzekeretsa kapena Kuphusitsa.....	8
2. Kukonzekeretsa kwa Baibulo.....	19
3. Moto wa Mulungu.....	26
4. Ulemelero wa Mulungu.....	39
5. Zolinga za Ulemelero wa Mulungu.....	52
6. Mmene mungampatsire Mulungu Ulemu.....	58
7. Likasa Likubwera.....	66
8. Kubwenzeretsa Chihema cha Davide.....	74
9. Ofunika. Wolambira.....	80
10. Tingalambire bwanji.....	87
11. Kodi Chitsitsimutso ndi chiyani?.....	9
12. Zitsitsimutso Mu Chipangano Chakale.....	98
13. Mfundo za Mbaibulo za Chitsitsimutso.....	101
14. Wokonzekeretsa.....	105
15. Wokonzekeretsedwa.....	111
16. Mfundo za kulowera.....	115
17. Atatha kugonjetsa.....	121
18. Nthano ya mizinda itatu.....	126
19. Kukonzekera kwa mphatso.....	131
20. Mayankho a mafunso odziyetsa nokha.....	135

## **KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA BUKULI**

### **KAKONZEDWE KA BUKULI**

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

**Zolinga:** Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welangani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

**Vesi Yotsogololera:** Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

**Zopezeka mu Magawo:** Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

**Zophunzira Zowonjezera:** Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

**Mayeso Omaliza:** ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

### **ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POPHUNZIRA PHUNZIROLI**

Mudzafunikira Buku Lopatulika

## NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

### MKUMANO WOYAMBA

**Kutsekulira:** Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

**Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu:** Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene mudzikumana.

**Mayamiko ndi Matamando:** Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

**Gawani Mabuku Kwa Ophunzira:** Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

**Perekani Nchito Yoyamba.** Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene adziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

### MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

**Kutsekulira:** Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

**Kukumbutsira:** Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

**Phunziro:** Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankha kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipereze okha mayankho.

**Mayeso omaliza:** Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

## MAWU OYAMBA

Mawu oti “kumemeza” amatanthauza “kukonzekeretsa anthu kugwira ntchito, kapena kugwiritsa ntchito mphamvu pa ntchito. Pamene “ndondomeko” ndi dongosolo la njira,” yolongosoledwa bwino pofuna kukwaniritsa masomphenya kapena zolinga.

Ndondomeko za dziko pofuna kulimbikitsa limakhazikika pa kunamiza anthu ndi kuba katundu ndi cholinga chofuna kupeza phindu la umbombo ndi kudzikudza. Pofuna “kulimbikitsa” anthu, pempho limapita pa zinthu zimene zosangalatsa thupi kapena kupezeka chifukwa cha zoipa, kuumilizidwa kapena kugwiritsa ntchito mphamvu. Kumemeza kumasiyana, motero kumakhazikika pa mfundo za uzimu ndi kulimbikitsa kumene kumachokera kwa Mulungu osati kwa munthu. Kumemeza kumabweretsa kukhudza kwa ulamuliro wa Mulungu osati zofuna zomwe anthu amakhala nazo kuthupi.

Mu phunziroli muphunzira kusiyana kwa kumemeza ndi kunamiza. Muphunzira maziko a Mbaibulo okhudzana ndi kumeneza ndi kuphunzira mmene moto, ulemerero ndi malambiro a kwa Mulungu zimagwirira ntchito pomemeza anthu a Mulungu. Muphunziranso mfundo za Mbaibulo za chitsitsimutso ndi kuphunzira kufunika kwa kumemeza kumene kumakwaniritsa masomphenya a uzimu.

Muzaonanso mbiri ya Yoswa Mbaibulo, ndi kuona za mmene anamemezera anthu a Mulungu kukatenga dziko la Kanani. Muphunzira za mtundu wa anthu umene Mulungu amaugwiritsa ntchito ngati omemeza, ndi mmene mungalimbikitsire anthu kuchoka kukungokhala ndi kukhala ochitachita.

Muphunziranso mfundo za kulowerera zimene zingagwiritsidwe ntchito kulowa mu dziko, mzinda, kapena mudzi wa Mulungu. Muphunziranso zimene mungachite mutakumana ndi chiwa chochilikizidwa ndi mmene mungakumanire ndi ziphona za ku uzimu mdziko.

Phunziroli likuonetsa njira zolongosoledwa bwino za kumemeza okhulupiria (kugwiritsa ntchito kuthekera kwawo pofuna kukwaniritsa zolinga zawo za kholora la uzimu. Phunziroli ndi gawo la Harvestime International Institute okonzedwa ndi cholinga chokonzekeretsa okhulupirira kuti agwiritsidwe ntchito ndi Mulungu kuti absinthe chimene akhumbira kuti awonetsere.

Mu bukuli, phunziro limodzi lotchedwa “Kuonaona” ophunzira akutsimikizidwa ndi masomphenya a kholora za uzimu la mmunda limene okhulupirira onse ayitanidwa. Muphunziro lachiwiri la, “Kukhala Wachiwiri,” maphunziro ambiri amakhazikika pa maziko a uzimu amene ndi ofunika kukhala wokolora.

Mu phunziro lachitatu la “Kuchukukitsa,” ophunzira atsimikizidwa ku kuchuluka ku uzimu pamene akuchuluka ndi kugawira ena zimene aphunzira.

Phunziro la chinayi, la “Dongosolo,” limalongosola za kayendetsedwe ka chuma cha uzimu pa chomwe chimadza chifukwa cha kutukuka kwa “[kuchulukana.” Pambali pa phunziroli, pa mutu wa “Kumemeza” umene umakamba za njira za kumenezera mphamvu za uzimu za Mulungu ndi kulongosola zomwe zimachitika ndi masomphenya a Harvestime kumadera omwe amachita utumiki.

Maphunziro a Harvestime kutsatira limeneli ndi ofunukira onse. Pamene mukuyesera kumemeza popanda maziko, ndiye kuti muli ndi change cha chopanda chidziwitso. Simungamemeze opanda anthu, amene amapangitsa kuti kuchuluka kutheke. Ngati muyesera kumemeza koma opanda dongosolo, mukhoza kukhala ndi ntchito koma yopanda cholinga.

Nthawi zambiri mu chikhristu, timapereka zbwino kwa Mulungu ndi kumaganiza kuti ndi zokwanira. Zabwino zathu sizikwana. Kuchulukana ku uzimu sikokwanira. Ngakhale maziko abwino a chiphunzitso si okwanira. Ndi zoonza kuti tiyenera kupereka zabwino koma tiyenera kuyang’ana kwa Mulungu kuti awonjezera moto wake Woyera, Ulemerero wake ndi kukonzedwanso ku uzimu. Tikuyenera kuphunzira osadalira pa maphunziro athu, zomwe tadutsamo ndi dongosolo lanthu. Koma, tiyenera kudalira pa kukhudza kwa Mulungu pa ntchito ya manja athu. Pamenepo, ngati ife okolora, tidzamemezedwa ku ntchito ya zokolora.

**Ndipo panali munthu mwini cuma amabvala cibakuwa ndi nsaru yabafuta, nasekera, nadyerera masiku onse (Luka 19:16).**

**Ndipo cisomo cace ca Yehova Mulungu wathu cikhale pa ife;  
Ndipo mutikhazikitsire ife nchito ya manja athu;  
Inde, nchito ya manja athu muikhazikitse (Masalmo 90:17)**

## ZOLINGA ZA PHUNZIRO

Pakutha pa phunziroli muyenera:

- Kupereka tanthauzo la kumemeza.
- Kulongosola kusiyana kwa kumemeza ndi kunamiza.
- Kulongosola ubale wa pakati pa kumemeza ndi kufalitsa uthenga.
- Kulemba chidule cha mfundo za Mbaibulo za kumemeza.
- Kulongosola izi zokhudza kumemeza kwa ku uzimu:
  - Moto wa Mulungu
  - Ulemerero wa Mulungu
  - Malambiro a Mulungu
  - Chitsitsimutso chochokera kwa Mulungu
- Kulongosola tanthauzo la kulambira mu Mzimu ndi mchoonadi.
- Kukambirana za mmene tingamulambirire Mulungu.
- Kudziwa mfundo za Mbaibulo za chitsitsimutso.
- Kulongosola za mmene tingamemezere anthu omwe sachita kanthu.
- Kulongosola za mmene tingathanirane ndi zolemphera.
- Kulongosola mfundo za Mbaibulo za kulowerera mu buku la Yoswa.
- Kudziwa zomuyenerereza munthu kukhala womemeza anthu ena.
- Kumemeza mpingo wanu ndi mphatso za mzimu.

## CHAPUTALA CHA 1

### KUKONZEKERETSA KAPENA KUPUTSITSA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “kunamiza.”
- Kupereka tanthauzo la mawu oti “kukonzekeretsa.”
- Kulongosola kusiyana pakati pa kukonzekeretsa ndi kunamiza.
- Kulongosola kusiyana pakati pa munthu wongokhala ndi amene wamemezedwa.
- Kulemba chidule cha ubale wa pakati pa kumemeza ndi kufalitsa uthenga.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Koma Yesu anawaitana, nati, Mudziwa kuti mafumu a anthu amadziyesa okha ambuye ao, ndipo akuru ao amacita ufumu pa iwo. 26Sikudzakhala comweco kwa inu ai; koma amene ali yense akafuna kukhala warnkuru mwa inu, adzakhala mtumiki wanu; 27ndipo amene ali yense akafuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu: 28monga Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la anthu ambiri (Mateyu 20:25-28).**

#### MAWU OYAMBA

Zimanenedwa kuti, “kupambana pa kuchuluka pa ulendo uliwonse kumafanana ndi kuthekera komemeza ndipo kumakhudza kukhala membala wokhazikika pofalitsa zikhulupiriro, zolinga ndi mnzeru.”

Ngati cholinga tifuna kuti chikwaniritsidwe, mukuyenera kuchitapo kanthu. Koma ngati mungolimbana ndi zofuna, ndi zolinga, ndiye kuti muli ndi dongosolo. Ngati mumemeza anthu, ndiye kuti muli ndi chinthu ndipo munthu aliyense amene ali mchinthumu amakhala gawo la kukwaniritsidwa kwa masomphenya.

Kumemeza komwe kumaoneka kunja, kumakhala zotsaitira za kumemeza kwa mkati. Aliyense amalimbikitsidwa kuchita chinthu. Chinthu chofunika mu utumiki wamphamvu ndi kulimbikitsa ndi kumemeza anthu a Mulungu pa ntchito ya utumiki.

#### KUPUTSITSA

Njira za dziko za kumemeza zimakhazikika pa kuputsitsa anthu ndi cholinga chozitamandira. Motero “kunamiza” kumatanthauza “kuchita dongosolo, kutsogolera, kulamulira munthu ndi



cholinga chongofuna kudzitamandira. Munthu amene amanamiza amagwiritsa ntchito anthu ena molakwika ngati “zinthu” ndi cholinga chongofuna kukwaniritsa zinthu.

Pofuna kuputsitsa, kunamiza/kunyengerera, machitachita omemeza anthu amakhazikika pa zinthu zimene zimakhala za kuthupi. Munthu amakopeka kuti ntchito zina zikwaniritsa zolinga, zofuna komanso zokhumba zake. Amaika chidwi chake pa matamando ndi pa chidwi cha anthu ena. Amafunitsitsa kukhala wapamwamba ndi wodziyenerenza. Chidwi chake chimakhala pa chuma ndi katundu. Izi ndi zina mwa zinthu zimene zimakhala zoyambirira za mkati zimene amamemezera nazo pochita zinthu.

Kuputsitsa kumakhazikika pa zosowa. Mtsogolera amaona chosowa ndi kuyamba kuwanyengerera anthu ndi chuma ndi cholinga chofuna kukwaniritsa chosowa. Ngati mwakhazikika pa zosowa, posachedwa mumalamulidwa ndi zosowazo. Anthu amakulamulirani ndi kukunyengererani ndi cholinga chofuna kukwaniritsa zosowa zawo.

Zoona zake, pali kunyengerera kwa mitundu iwiri. Koyamba kumakhala koumiriza kumene kumafuna kugwiritsa ntchito mantha ngati mphamvu yake. Mtundu wina ndi kukoka kumene kumafuna zinthu zakuthupi ndi mphoto. Pamene wokhulupirira akakamizidwa kapena kukokedwa kuti achite ntchito ya ufumu wa Mulungu, ndi zachiziwikire kuti chinachake sichili bwino.

Mu kuputsitsa, anthu amatengedwa ngati a wamba kapena atsogoleri amayamba kuopseza, kulakwira kapena kukamiza zinthu kuti zichitike. Koma Baibulo limachenjedza atsogoleri kuti...

**Ndipo, ambuye inu, muwacitire zomwezo iwowa, nimuleke kuwaopsa; podziwa kuti Ambuye wao ndi wanu ali m'Mwamba, ndipo palibe tsankhu kwa Iye (Aefeso 6:9)**

Mwanjira ina, mukhale nawo iwo amene mukuwatsogolera molingana ndi mmene Mulungu amakhalira ndi inu.

“Ufiti kapena nyanga zikupezeka mu Agalatiya 5:20 ngati imodzi mwa ntchito ya kuthupi. Mu ndimeyi, ufiti sumaimira ntchito zoyipa zokha zochitika ndi afitiwo amene amatsata Satana. Koma umaimiranso kunyengerera kwa kuthupi kwa anthu ndi cholinga chofuna kukwaniritsa zolinga ndi zokhumba zanu.

Yesu anaphunzitsa kuti okhulupirira sayenera kuvomereza njira za makhalidwe a dzikowa ndi utsogoleri:

**Koma Yesu anawaitana, nati, Mudziwa kuti mafumu a anthu amadziyesa okha ambuye ao, ndipo akuru ao amacita ufumu pa iwo.**

**Sikudzakhala comweco kwa inu ai; koma amene ali yense akafuna kukhala warnkuru mwa inu, adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense akafuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu: (Mateyu 20:25-27)**

## **KUKONZEKERETSA**

Okhulupirira sayenera kunamizidwa kapena kukhala onamiza kapena oputsitsa, koma akuyenera kukhala omemezedwa. Mulungu wakhala akuyendera anthu amene amalimbikitsidwa kuntchito. Mumbiri yonse ya Baibulo Mulungu amaitana anthu kuti amemeze kuthupi, ku uzimu ngakhale kuchuma ndi cholinga chofuna kukwaniritsa cholinga ndi zofuna zake.

Choncho “kumemeza” kumatanthauza kukhala wokonzekera kugwira ntchito, kugwiritsa ntchito mphamvu za munthu wina ku ntchito. Pofuna kutambasula, kumemeza ndi chochitika chilichonse chimene anthu a Mulungu amatakasidwa ndi kupitilirabe kukula kufikira apeza gawo lawo lalikula la kukwaniritsa ulaliki wa dziko lonse lapansi.

Kumemeza kwa ku uzimu kumasiyana ndi kunyengerera chifukwa kumakhazikika pa mfundo za Mbaibulo ndipo cholinga chake chimakhala pa Mulungu osoti munthu. Sikumakhazikika pa za kuthupi kapena za munthu yekha ayi. Sikumakhazikika pa utumiki wa zosowa ayi, koma pa lamulo.

Mwachitsanzo, pamene Yesu anayendera thamanda la Betsaida, panali anthu ambiri amene anali opuwala ndi odwala. Koma Yesu anachidza munthu mmodzi yekha. Amakhazikika pa lamulo osati pa chosowa. Izi sizitanthauza kuti analibe chifundo ndi odwala ena aja, koma anatsogozedwa ndi Mulungu kutumikira kwa munthu amene uja.

Ngati mukhazikika pa zosowa mu utumiki, mwachangu muzaopsezedwa ndi zosowa zimene zakuzungulirani. Komalizira, muzizatsogozedwa ndi zosowa. Zosowa za anthu zizalamulira moyo ndi utumiki wanu. Muzanamizidwa ndi izo ndipo mudzakhala onamiza ndi cholinga chofuna kukwaniritsa zosowa zazikulu.

Ngati mukhazikika pa lamulo osati pa zosowa, utumiki wanu amautsogolera ndi Mulungu osati munthu. Muzalimbikitsidwa ndi kumemezedwa ndi mphamvu ya Mulungu osati kunamizidwa ndi anthu ndi zosowa zawo.

## **KUSACHITA KANTHU NDI OMEMEZEDWA**

Mawu otsutsana ndi kumemezedwa ndi kusachita kanthu. Choncho ndi zofunika kwambiri kudziwa kusiyana kwa zinthu ziwirizi ngati mukufuna kulimbikitsa okhulupirira amene sachitachita.

### **MUNTHU WONGOKHALA:**

Kusachita kanthu kumatanthauza kusakhudziwa, kukhala wosiyana, wosasunthika. Izi ndi zina mwa zifukwa zimene anthu amakhallira osachita kanthu, osakhudzidwa ndi osiyana, ndi osakangalika ndi ntchito ya Mulungu:

-Sakhala panso pa ulamuliro wa Ambuye Yesu.

-Sanamvetse tanthauzo la kutumidwa.

-Sadziwa malo awo mu thupi la Khristu.

-Alibe zolinga, masomphenya ndi kopita.

-Alibe masomphenya amodzi. Amaona ali ndi zochita zambiri koma opanda masomphenya a zimene ayenera kuchita, choncho amakhumudwa ndipo sachita kanthu.

-Amakhala okangalika ndi zofuna ndi machitachita a dziko.

-Amaopa kuti chidwi chawo chokangalika chidzperereka mwayi kwa ena.

-Utsogoleri wa ulamuliro umene umachita chilichonse umalepheretsa kupezeka kwawo. Uwu umakhala utumiki wokhazikika pa zofuna za mmalo mwa mwa utumiki wa thupi wa ziwalo zonse za mu ntchito ya Ambuye. Mbusa kapena mtsogoleri wauzimu sayenera kuchita zonse yekha. Akuyenera kukonzekeretsa kapena kulimbikitsa ena thupi pa ntchito ya utumiki.

-Amakhala a kale lawo: Baibulo limachenjeza za kukumbukira mkazi wa Loti. Kuyang'ana mmbuyo kwa zinthu zabwino zakale kapena mmene zinthu zimachitikira kale kumalepheretsa zinthu zochitika za tsopano.

-Amayenda mthupi: Pamene munthu ayenda mthupi, sangakwaniritse zolinga za uzimu. Thupi limekulepheretsani kuchita zimene muyenera kuchita (Aroma 7:15). Nkhawa, magawano, ndi mikangano yosatha ndi zizindikiro zoti munthu akuyenda muthupi. Awa ndi makhalidwe ena amapangitsa anthu kukhala osachita kanthu mu ufumu wa Mulungu.

-Tchimo limalepheretsa kuyenda kwa kudzodza kwa Mulungu, moto wake, ulemerero wake ndi chitsitsimutso. Chifukwa chakuti izi ndi mphamvu zomemeza za uzimu, wokhulupirira amene akhalabe mu uchimo amasemphana ndi zimenezi.

-Kukhumudwa kumabweretsa kukhala chete: Munthu wokhumudwa amasokonezeka mmaganizo, amafuna mphamvu, ulamuliro kuti atuluke mu zimene ali. Amakana udindo wake, mkupezera zifukwa anthu ena pa mavuto awo, ndi kyamba kubwezera. Samakhazikika ndipo amakhala wosamvera.

-Malangaliro oti zingozchitika: ilinso ndi vuto limene limapangitsa anthu a mumpingo kukhala chete. Malingalirowa amangofuna kuti zinthu zingochitika basi.

### **ANTHU ONGOKHALA:**

Munthu wogokhala amalimbikitsa kuti enanso azingokhala. Choncho mpingo wongokhala umagwirizana ndi umene umapezeka pa chibvumbulutso 3:1 ku Sardisi. Amakhala ndi dzina kuti alipo, koma amakhala okufa. Izi ndi zitsanzo za mpingo wongokhala. Kodi mpingo wanu umakhala bwanji?

- Chisamaliro cha mpingo pa zinthu za kuthupi chimakhala chapansi ndipo chimalengeza malingaliro akuti “sindisamala.”
- Pamakhala kudalira kwakukulu pa abusa kapena olembedwa ntchito amene achita ntchito ya utumiki.
- Pamakhala kukhazikika pa zinthu za kale, kukhulupirira kuti zinthu zabwino zakale zinali bwino kusiyana ndi zatsopano.
- Chiwerengero cha anthu mu mpingo chimasowa.
- Mamembala ambiri samachita kanthu mumpingo.
- Chidwi cha anthu ambiri chimakhala pa nyimbo, ana, ndi achinyamata pomwe akuluakulu amakhala chete.
- Nkhani zachuma ndi zimene zimatsogolera zochitika za chikhulupiriro.
- Kulumikizana kumakhala kovuta pakati pa mamembala, abusa ndi olembedwa ntchito.
- Kupezeka kwa anthu ochepa mumpingo kumaonetsera kusowa kwa chidwi.
- Sipamakhala chidwi chokapanga ulaliki kunja.
- Amene amapanga ziganizo ndi ena olusa ambiri amakhala amene ali ma membala pamene mpingo umayamba ndi zinthu zabwino zakale.
- Mtumiki amauona utumiki wake ngati wakale osati wakutsogolo.
- Mpingo umakhutira kuti ngati ungapeze mbusa wamphamvu ndi kuchotsa mtumiki, mavuto awo angathe.
- Utsogoleri wa mpingowo umaona kuti ntchito yawo yoyamba ngati chilolezo polesa kuti sangalese mamebala chimene sichiyenera. Mumpingo wochitachita, utsogoleri umalimbikitsa luso, machitachita achikhulupiriro ndi zina zimene zingachitike kusiyana ndi kungokhala ndi chilolezo.
- Ndondomeko zatsopano zimakwaniritsidwa ndi mtsutso wakuti, “chifukwa chiyani izo sizitheka pano.”
- Chidwi chimakhala pa kuphunzira osati kuchita.
- Membala weniweni sangatchule anthu okwana asanu dzina lawo.
- Anthu amakhala otsutsa pa zimene zikuchitika ndi zimene sizikuchitika.
- Mamembala atsopano amaona zovuta kukhala gawo limodzi la mpingowo kapena ofunika.

Zinthu zonsezi zimaonetsera kusakhala ndi chidwi, kusiyana ndi kukhala osachita kanthu.

#### **MUNTHU WOKONZEKERETSEDWA:**

Munthu amene watakasika kapena kumemezeka amakhala wokonzeka kulolera ndi kutenga udindo mwa chitsogozo cha Mzimu Woyera. Samayendera zinthu za iye mwini ayi. Amakonzekeretsa chotengera chake cha uzimu kulandira zinthu zatsopano kwa Mulungu. Munthu amene wamemezeka amadalira kwa Mulungu osati iwo okha. Amakhala wa uzimu osati wakuthupi ayi. Amakondwera ndi ntchito ya Mulungu ndipo amachita nawo za mu ufumu wa Mulungu.

Munthu amene walimbikitsidwa amakhala wokonzeka kutenga ukaziotche wa chikhulupiriro ndi kutenga udindo pa zimene angachite. Munthu amene wamemezedwa amakhala okhazikika, omvera, ndipo mmalo mobwenzera mu nyengo yoipa, amafunafuna mayankho. Amakhazikika pa lamulo osati pa zosowa. Samanyengerera kapena kugwiritsa ntchito anthu ena molakwikwa. Amakhala womva chifundo, okondwa ndi ntchito yonse ya ufumu.

#### **ANTHU AMENE AKONZEKERETSEDWA:**

Onaninso zizindikiro za mpingo umene umangokhala wosachita kanthu mu phunziro limene langothali. Ganizirani za kusiyana kwa zizindikirozi. Kusiyana kwa khalidwe lililonse kumalongosola za mpingo wolimbikitsidwa kapena womemezedwa.

Mpingo umene wamemezedwa ku uzimu umakonzedwanso. Mpingo womwe ndi wolimbikitsidwa, woyaka ndi chikondi ndi chisoni pa iwo osochera. Umakhala ndi anthu amene ndi ochitachita pofula kukwaniritsa kutuma kwakukulu. Umakhala ndi malingaliro a ufumu osati a chimpingopingo. Umakhala wolambira, mpingo wotsitsimuka odzadzidwa ndi mphamvu ndi ulemerero wa Mulungu.

#### **ZOMUYENEREZA MUNTHU KUKHALA WOKONZEKERETSA WABWINO**

Mbuyomu panali katswiri wa za sayansi wotchedwa Sala Isaki Nyutoni. Anaphunzira ndi kulemba za mmene zinthu zimayendera. Lamulo loyamba lokhudza kayendedwe ka zinthu limati... “Thupi limakhalabe likuyenda pamene liyenda ndipo limapuma pamene lipoma.”

Izi ndi zoonanso ngakhale ku uzimu. Anthu azakhalabe osasintha, osakhudzika, ongokhala pokhapokha alimbikitsa kapene amemezedwa kuchita ntchito ya ufumu.

Apa ndi pamene utumiki wa munthu womemezedwa umabwera. Munthu wolimbikitsa ndiye amene amalimbikitsa ena. Koma pofuna kuchita izi koyamba ayenera kuzilimbikitsa yekha. Munthu amene walimbikitsidwa amathanso kulimbikitsa ena pokhala chitsanzo ndi kulimbikitsa osati kukakamiza kapena kuchititsa mantha.

Wolimbikitsa amadzipereka ku ntchito yapadera ya kutumidwa. Chidwi chake chimakhala pa anthu akunja osati zofuna zake ndi zokonda zake. Samangokhala munthu wadongosolo.

Samakhala munthu wachimpingopingo. Amakhala munthu wa ufumu. Zolinga, masomphenya ake zimakhala pa ufumu wa Mulungu.

Munthuyu amakonzekeretsa anthu ku ntchito ya Mulungu powatsimikizira ndi masomphenya a uzimu, kuti akhazikike pa maziko a chikhulupiriro ndi kukhala woberekana mu uzimu. Amathandiza anthu kudziwa ndi kuonetsera maluso awo popanda ganizo la kuopsezewa ndi kukula kwawo kwa ku uzimu ndi kupita chitsogolo kwa ufumu wa Mulungu.

Mu zoonza zake, utsogoleri wa uzimu umene Mulungu amaukhazikitsa mu mpingo ngati atumwi, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi amakhala omemeza anthu. Cholinga ndicho kukonzekeretsa ena ku ntchito ya utumiki (Aefeso 4:11).

Wolimbikitsa samaona anthu ngati zifanizo zoimira zinthu zina. Amadziwa kuti kumemeza kumakhudza “kuchita ichi” ndi kuti munthuyo achita. Amazindikira kuti anthu ena analengedwa mu chifanizo cha Mulungu osati ngati zinthu zina mu ntchito ya ufumu.

Wolimbikitsa amakhala wolimba mtima mkatikati mwa chitsutso ndipo amakhala ndi luso lakuya la uzimu. Moyo wake umakhala kuti wakhudzidwa ndi mphamvu komanso ulemerero wa Mulungu. Amayenda mu ungwiro ndi kusunga ubale wake ndi Mulungu.

Yoswa, amene anasankhidwa ndi Mulungu kuti atsogoleri Israyeli kupita kudziko lamalonjezano, ndi chitsanzo chabwino cha anthu olimbikitsa. Muphunzira zambiri za iye ndi zomuyenera munthu kukhala wolimbikitsa mu chaputala cha 14 cha phunziroli.

Okhulupirira ambiri ndi okufa ku uzimu chifukwa amene amawalalikira ndi okufanso. Ambiri amakhala osachita kanthu, opanda chifundo, osasinthika komanso opanda chidwi. Ngati mulibe chidwi ndi kuchokera mumtima, ndiye kuti amene mukuwatsogolera azasowanso chidwi. Tikuyenera kukhudzidwa ndi moto wa Mulungu!

Numeri 16:46-48 amakamba za mmene Mulungu amamugwiritsira ntchito Aroni pokhala pati pa amoyo ndi akufa, popereka kwerero la moyo. Izi ndi zimene munthu womemeza ayenera kuchita. Amaima pakati pa akufa (ongokhala) ndi amoyo (ochitachita). Amagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu polimbikitsa okhulupirira kuchita ntchito. Amanyamula chotengera chokhala ndi moto wa Mulungu, mkuika pa moyo wa aliyense lawi la moto. Anthu ambiri akuyesera kutsogolera anthu a Mulungu ndi kugwira ntchito ya Mulungu ndi mtima wonse koma osayatsidwa moto mumtima kapena ndi mitima imene inathimitsa moto wa Mulungu. Kodi moto umene uyatsa tchire la chipululu uyake munthawi ya Mose ungayatse mitima yathu kufikira titayaka ndi Mulungu? Kodi mzotheke kuti moto umene Ezekieli anauona ukuchoka apo ndi apo kwa Israyeli ubwererenso?

## **KUKONZEKERETSA NDI KULALIKIRA**

Kodi ndi cholinga chanji chimene tikulimbikitsa anthu? Ndi chifukwa chiyani tikulimbikitsa anthu ofooka. Ngati anthu akukhala bwino mu mpingo ndipo zosowa zawo zikukwaniritsidwa, nanga mchifukwa chiyani kumawalimbikitsanso?

Tikuyenera kukhala ndi chidwi polimbikitsa zipangizo za Mulungu za ku uzimu chifukwa ndi njira yokhayo imene tingapezere zokolola zambiri za uzimu. Tikulimbikitsa katundu wa ku uzimu ndi cholinga chofuna kuchita ulaliki.

Pali kusiyana pakati pa kulimbikitsa ndi njira zina zochitira ulaliki. Mu ndondomeko zambiri za maulaliki, chidwi chambiri chimakhala pa iwo amene ali ndi mphatso. Kapena nthawi zina mmipingo yatsopano chimakhala kwa amene waphunzira ntchito ya ulalikiyo. Mu mtundu wa ulaliki umenewu, chidwi chimakhala pa kuchuluka kwa chiwerengero cha omvetsera. Kuulutsa malonda, kutumiza mauthenga, mmawailesi ndi mmakanema ndi njira zina zimagwiritsidwa ntchito. Chilichonse chotheka chimachitika pokudza zotsatira za utumiki wa ulaliki.

Palibepo cholakwa ndi njirazi. Ndi zofunikira kupezapo mwayi kuchokera kwa amene ali ndi mphatso za ulaliki mu mpingo wa Mulungu. Koma pofuna kufikira kholola la dziko lonse lapansi la uzimu, tikuyenera kutenga njira yomemeza ngati ya ulaliki.

Njira yomemezera ya ulaliki imaika chidwi pa okhulupirira onse, osati iwo okhawa amene alia li mphatso yongochita ulaliki. Imafuna kuchulukitsa chiwerengero cha okhulupirira atsopano polimbikitsa aliyense kuti achite ntchito yabwino ya ulaliki (II Timoteo 4:5).

Mtundu wa kumemeza kotereku, umachitika mumpingo mkati mwa mfundo za Mbaibulo. Umatchedwa “thupi la utumiki,” pamene munthu aliyense amatenga malo ake molingana ndi mphatso yake ya uzimu. Kenako thupi lonse limagwira ntchito mu umodzi pokwaniritsa zolinga zazikulu mogwirizana ndi kutumwa kwakukulu. Polimbikitsa mwakuchita ulaliki, timagwiritsa ntchito chilichonse chothekera ndi cholinga chofuna kufikira dera, ndi uthenga wabwino kwa anthu onse.

## **NTHAWI YOKONZEKERETSA ANTHU**

Asilikali a kudziko, ankhondo amamemezedwa munthawi ya nkhondo kapena pamene pali chosowa. Ku uzimu, iyi imakhala nthawi ya nkhondo. Tili pa nkhondo yaikulu ya mitima, miyoyo ndi maganizo a anthu a mdziko lapansi. Iyi ndi nthawi ya chosowa chachikulu. Timachiona pamene tikuona kholola la uzimu la dziko lapansi, limene lakonzeka kukololedwa, koma ndi ogwira ntchito amene ndi ochepa pamene dzuwa likulowa. Tsopano yakwana nthawi yomemeza anthu a Mulungu. Molingana ndi zimene mneneri Mika ananena, “Dzukani! Adani amanga...” (Mika 5:1).

Ngati tikufuna kuti tilimbikitse anthu, tikuyenera tibwerere ku lamulo la Mulungu osati kukhazikika pa zosowa za mu utumiki. Tikuyenera kudalira Mulungu osati ife eni. Dongosolo, mgwirizano, kuchulukana, ziphunzitso zonsezi ndi zofunikira. Koma ndi Mulungu yekha amene

angatumize moto, ulemerero ndi chitsitsimutso chimene chimatakasa anthu ake. Monga thupi lopanda mpweya ndi moyo, momwemonso anthu a Mulungu amene ali a dongosolo, amodzi ndi okhazikika mchiphunzitso, koma akusowa mpweya wa Mzimu Woyera.

Ngati mudalira maphunziro anu, mumakwaniritsa zimene maphunzirowo amafuna. Ngati mudalira luso lanu ndi kulimbikira kwanu, mudzafikira zofuna za luso ndi kulimbikira. Pamene mudalira pa utsogoleri wokha, mudzachita zambiri...koma zokhazo zimene utsogoleri umafuna kuchita. Koma ngati mudalira pa Mulungu, mufikira zimene Mulungu akhoza kuchita!

Kuchita kwa munthu sikudzafikira ntchito. Kholora lalikulu lotsiriza silingatheke ndi njira za kuthupi.

**Kodi muli opusa otere? Popeza mudayamba ndi Mzimu, kodi tsopano mutsiriza ndi thupi? (Agalatita 3:3)**

Ntchitoyi singakwaniritsidwe ndi kunamiza kapena kunyengerera kapena ndi mphamvu za munthu.

**Pamenepo anayankha, nanena kwa ine, ndi kuti, Awa ndi mau a Yehova kwa Zerubabele, Ndi khamu la nkondo ai, ndi mphamvu ai, koma ndi Mzimu wanga, ati Yehova wa makamu (Zkariya 4:6)**

Zaka zambiri zapitazo, Mulungu anapatsa mneneri Zakariya masomphenya a choikapo nyali. Nyaliyo imabweretsa kuwala ku chomwe imakhala chimene chinali ndi mafuta omwe amachokera ku mtengo wa Azitona. Nyali imayaka pamene mafuta amayenda.

Simungachite ntchito ya Mulungu popanda kudzodza kwa Mulungu kopitilira mmoyo wanu. Mukuyenera kulumikizidwa ku mtengo wa Azitona. Ngati chipatso chokhala ndi nthambi, chiyenera kukhala ku mpesa (Yohane 15). Ichi ndi chilimbikitso cha umulungu. Uku ndi kumemeza kwa ulamuliro.

Yesu anakhudzidwa ndi kukhudza kwa moto wa Mzimu Woyera (Luka 4:18). Mpingo woyamba unayaka moto ndi mphamvu ya Pentekosite ku Machitidwe 2. Davide anadziwa mphamvu ya Mzimu (II Samueli 23:2). Ezekieli anachitira umboni mobwereza. Ezara 7:6, Nehemiya 2:18 nawonso anakhudzidwa ndi mphamvu ya Mulungu pamene dzanja la Ambuye linalin pa iwo. Mtumwi Paulo anachidziwanso ichi pa II Akorinto 1:21-22, ndipo inu mukhoza kuchitanso!



## MAFUNSO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Perekani tanthauzo la mawu oti “Kunyengereredwa/kunamizidwa

---

---

3. Perekani tanthauzo la mawu oti “kumemezedwa/kulimbikidwa.

---

---

4. Longosolani kusiyana pakati pa kulimbikitsidwa ndi kunamizidwa ku uzimu.

---

---

5. Longosolani kusiyana pakati pa munthu wongokhala ndi amene walimbikitsidwa.

---

---

6. Ombani mkota pa za ubale wa pakati pa kumemeza ndi kuchita ulaliki.

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukulu)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani nkhani ya asilikali a Davide mu I Samueli 30. Onani za mmene anthuwa anakumana ndi mmene munthu wokhumudwa amakhaira:

“Munthu wokhumudwa ndiye amene samaona patali, alibe mphamvu, ulamuliro kuti achoke pamene ali. Amakanaka udindo wake, amada anthu ena pa zovuta, ndipo amafunitsitsa kubwenzera. Amakhala wosakhazikika ndi wosamvera.

Kodi Davide anatani kuti absinthe nyengoyo? Kodi mukuwadziwa anthu wokhumudwa? Nanga mungawalimbikitse bwanji?

2. Chikhalidwe cha kulimbikitsika kwa munthu molingana ndi Abraham Maslow. Ananena kuti pofuna kulimbikitsa anthu kuti achite chinthu, tikuyenera kufikira zosowa za moyo wawo monga:

-Kukwaniritsa luso lake.

-Kukula ndi kutukuka.

-Kulenga zinthu.

-Kulimbikitsa ena.

-Kudzilimbikitsa ena.

-Kukhala kwa wina.

-Kukonda.

-Kukondedwa.

-Malo okhala.

-Chitetezo.

-Kugonana.

-Luzu.

-Njala.

Pamene izi ndi zofunikira pamoyo wa kudziko, koma ndi zokhumba za kuthupi. Anthu amene amemezedwa pa zosowazi sazasowanso kulimbikitsidwa. Pamene zofuna zawo sizikukwaniritsidwa, azabwenzera posachita kanthu.

Simungalimbikitse anthu pa za uzimu ndi zosowa za kuthupi. Mukuyenera kuwalimbikitsa pa zauzimu ndi mfundo za za uzimu.

## CHAPUTALA CHA 2

### KUKONZEKERETSA KWA MBAIBULO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kulongosola za mmene kukonzekeeretsa kunasankhidwira.
- Kudziwa zimene Baibulo limakamba zokhudza kumeneza.
- Kudziwa lamulo la Mbaibulo lomemeza okhulupirira.
- Kudziwa za mmene kukonzekeeretsa kunakhalira mu Chipangano Chatsopano.
- Kulemba zitsanzo za Chipangano Chakale zokhudza kukonzekeeretsa pa moyo wa Gidioni.
- Kuomba mkota pa zimene mwaphunzira zokhudza kukonzekeeretsa pa moyo wa Gidioni.

#### VESI LOTSOGOLERA:

#### MAWU OYAMBA

Mu mbiri ya Mbaibulo, Mulungu amachita zinthu molingana ndi zolinga zake kudzera mwa anthu amene amalimbikitsidwa kugwira ntchito. Malemba amaulula kuti kumemeza ndi kosanthidwa ndi Mulungu ndipo kumagwira ntchito Mbaibulo. Kumaonetsedwa mu Chipangano Chakale ndi ku Mpingo wa Chipangano Chatsopano, ndipo ndi kofunika pa lamulo lopatsidwa kwa okhulupirira amene akwaniritsa kutuma kwakuluku.

Mu phunziro ili, muphunzira mfundo za kumemeza. Muphunziranso choonadi chofunika cha Mbaibulo pa nkhani ya kumemeza. Ndi zoonza kuti kumemezaku sikuli pa kufunafuna zinthu kapena chuma. Mulungu amachita zinthu zamphamvu kudzera mwa anthu ochepa amene alimbikitsidwa kugwira ntchito ndi kuvomera kuitana kwake.

#### KULIMBIKITSA NDI KOSANKHIDWA NDI MULUNGU

Werengani Aefeso 4:11-16. Ndimeyi imaululu chifukwa chimene Ambuye amapereka mphatso za utsogolero ku mpingo ndi cholinga chofuna kukonzekeeretsa anthu kutchito ya utumiki. Atumwi, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi ayenera kukhala okonzeka. Iwowa ali ndi mphatso za za utumiki zochokera kwa Mulungu ndi cholinga chofuna kukonzekeeretsa okhulupirira ku ntchito ya utumiki.

Chifukwa chakuti Mzimu Woyera amakhala ndi kupereka mphatso kwa okhulupirira ndi kuwatsimikizira kuti kukonzekeeretsedwa kwa thupi lonse la khristu ndi kosankhidwa ndi Mulungu. Aroma 12:3-8 ndi I Akorinto 12:1-31.

## **KUKONZEKERETSA KUMAONEKA NDI MACHITIDWE AKE**

Mawu ake amene amagwiritsidwa ntchito mu mpingo amakambanso za kukonzekeretsa. Aroma 12:3-8 ndi I Akorinto 12:1-31 amakamba za mpingo ngati thupi limene wokhulupirira aliyense amayenera kukwaniritsa cholinga chake. Unsembe wa okhulupirira ukupezeka pa Ahebri 10:19-22, komanso I Petro 2:9 ndi Chibvumbulutso amakamba za kukonzekeretsa mpingo wonse ku ntchito ya ufumu wa Mulungu.

## **KUKONZEKERETSA MKOFUNIKA PA LAMULO LA MBAIBULO**

Kukonzekeretsa mkofunika pa lamulo la Mbaibulo loperekedwa kwa okhulupirira onse. Mwachitsanzo, malemba malemba amafotokoza kuti okhulupirira analengedwa ku ntchito zabwino. Onani Aefeso 2:10, Tito 2:14; 3:8, Yakobo 2:17, ndi I Petro 2:12). Ngati tikufuna kukwaniritsa zimenezi, tikuyenera kulimbikitsidwa kugwira ntchito.

Kukonzekeretsedwa ndi kofunikanso pokwaniritsa kutuma kwakukulu kofalisa uthenga ku dziko lonse lapansi:

Vesiii

Mukani, lalikiranini, batizani...awa ndi mawu oti tigwire ntchito. Mphamvu ya kukonzekeretsa okhulupirira ndi yofunika kukwaniritsa zimenezi.

## **KUKONZEKERETSEDWA KUMACHITIKA MU CHIPANGANO CHATSOPANO**

Chipangano Chatsopano chinali gulu la anthu okonzekeretsedwa. Amatumikira tsiku ndi tsiku mkachisi ndi ku nyumba iliyonse (Machitidwe 5:42). Amatamanda ndi kulambira Mulungu, ndipo Ambuye amawachulukitsa tsiku ndi tsiku (Machitidwe 2:47).

Ngakhale chizunzo sichimachotsa chidwi chawo. Chizunzo chimatsatira kubalalika kwa anthu ena koma...

Vesii....

Mpingo woyamba unapanga magulu a umishoni ndi kutumizidwa ku madera ena (Machitidwe 13:1-3). Amatumikira kuchokera ku Yerusalemu, Yudeya, Samariya ndi malekedzero onse a dziko lapansi. Mu zoonza zake anatembenuza dziko lapansi (Machitidwe 17:10).

## **KUKONZEKERETSA KUMAPEZEKANSO MU CHIPANGANO CHAKALE**

Kukonzekeretsa kumapezekanso mu Chipangano Chakale. Werengani ndi kuona mmene Mulungu anakonzekeretsa anthu ake:

- Kumangidwa kwa guwa: Eksodo 35:4-29
- Kufunafuna dziko lamalonjezano: Yoswa 1:10-15
- Kumangidwakwa kachisi woyamba: I Mafumu 5:13-18; I Mbiri 29:1-9
- Kumangidwa kwa kachisi wachiwiri: Ezara 1:5-6; 3:8-13; Hagai 1:2-15
- Kumangidwanso kwa linga la Yerusalemu: Nehemiya 2:17-6:15

Mukhonza kuwerenganso mfundo zina mu nkondo ya Chipangano Chakale imene Mulungu anakonzekeretsa anthu ake pofuna kugonjetsa mphamvu ya mdani. Chitsanzo chimodzi chosangalasa ndi cha Gideoni.

### **ZIMENE GIDEONI ANACHITA**

Mfundo imodzi ya kukonzekeretsa ya Mbaibulo ndi imene Mulungu anakwaniritsa zinthu zazikulu kudzera mwa anthu ochepa amene anakonzekeretsedwa pa cholinga chake. Ichi chimadziwiki ndi kuti “zimene Gideoni anachita” pa kukonzekeretsa chifukwa zikuoneka ndi nkhani ya munthu ameneyi.

Werengano Oweruza 6:11-24. Pamene mngelo anaonekera kwa Gideoni, munthuyo samakamba za nkondo kapena kulowa mu mzinda. Amachita zinthu zosiyana. Amabisala kwa adani amene anabwera mdziko lawo Israyeli atadzala mbewu zawo. Adani amaba zokolola ndipo Gideoni amayesera kukolola zochepa mwachinsinsi ndi mantha.

Ichi ndi chinthuzi cha zambiri za ntchito yokolola imene imachitika mdziko lero. Anthu amayesera kukolola ku uzimu kwa Mulungu koma mwa mantha, ngakhale mobisala poopa mdani. Pochitabe mobisalira chonchi, chotengera chathu chidzakhala chosakwanira. Monga Israyeli, tidakhala ndithu osauka.

Pamene mngelo amalankhula kwa Gideoni pomutcha ngwazi tikhoza kuyerekeza kuti Gideoni amaziona yekha kuti panalibe wamphamvu. Samazindikira kuti Ambuye anali naye.

Chimene Gideoni amaona ndi nyengo yokhayo yowopsa imene inamuzungulira. Anafunsa kuti ngati Ambuye ali naye, nanga bwanji zowawa zinawagwera. Kodi zozizwa zimene anachita ndi makolo awo zinali kuti?

Mukayang’ana nyengo ya dziko lanu limene mukhala, mumayamba kufunsa ngati Mulungu ali nanu, nanga zachitika bwanji? Ndi zokhumudwitsa, komanso zoopsa. Kodi zozizwa za Mulungu zili kuti?

Ndi mu nyengo imeneyi ya mantha ndi kukaikira imene Mulungu amaitchula kuti a “Gideoni” al lero. Zoona zake za zimene Gideoni anachita ndi zoti Mulungu amaitanira anthu ofooka ku zinthu zazikulu. Mngelo anamuuzza Gideoni kuti amuke mu mphamvu yake, chifukwa choti ndi

iye amene anamutuma iye. Chokhacho chimene chimatilimbikitsa kutipatsa mphamvu yoti tikumane ndi zovuta mu mbadwo wanthu ndi lonjezo loti Ambuye ali nafe. Lonjezo la kupezeka kwake laperekedwa kwa iwo amene akonzekeredwa kugwira ntchito ndi kuvomera ku maitanidwe ake.

**Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: 20ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansu pano (Mateyu 28:19-20)**

Gideoni anamfunsa mngelo za mmene angachitire. Popeza anali wamng'ono mbanja lakwawo. Mose anakumana ndi zomwezo. Yeremiya komanso Paulo anakumana ndi zomwezo. Inunso mukhoza kukumana ndi zomwezo. Mukhozanso kumabwerera mbuyo ndi abale mmene mulili kwanu, zachuma, maphunziro anu ndi kuthekera kwanu.

Koma Mulungu amagwira ntchito kudzera mwa anthu ofooka amene akonzekeredwa kuvomera maitanidwe ake:

**Pakuti penyani maitanidwe anu, abale, kuti saitaniidwa ambiri anzeru, monga mwa thupi; ambiri amphamvu, mfulu zambiri, iai; koma Mulungu anasankhula zopusa za dziko lapansi, kuti akacititse manyazi anzeru; ndipo zofoka za dziko lapansi Mulungu anazisankhula, kuti akacititse manyazi zamphamvu; ndipo zopanda pace za dziko lapansi, ndi zonyozeka, anazisankhula Mulungu, ndi zinthu zoti kulibe; kuti akathere zinthu zoti ziriko; kuti thupi liri lonse lisadzitamande pamaso pa Mulungu (I Akorinto 1:26-29)**

Kuthekera kumene Mulungu anampasa Gideoni sikunali luso lake lokha lolamula asilikali. Kunalinso kuthekera kulimbikitsa anthu ena kukhala nawo mu ntchito imene amagwira. Tikudziwa kuti anachita bwino chifukwa anthu okwana 32,000 anamvera maitanidwe ake.

Koma Mulungu atatha kumulimbikitsa Gideoni polemba ogwira naye ntchito, anaomuonetsera kuti amatha kugwiritsa ntchito ambiri komanso ochepa. Mulungu nachotsa anthu okwana 22,000 amene anali ankhondo. Aliyense amene anali wochita mantha anabwerera kunyumba.

Mulungu anapitilira kuchotsa ena okwana 9,700. Awa ndiwo amene amaoneka kuti sanakonzekere ndipo anali osakhala tcheru anabwereranso kunyumba. Kenako anatsala ndi anthu okwana 300, amene ena mwa iwo anali ongozipereka. Tangonganizani mmene Gideoni akanamvera pothirana nkhondo ndi anthu okwana 135,000! Amene amaimira anthu okwana 450 a Midiyani. Koma Mulungu anakwaniritsa zinthu zazikulu kudzera mwa anthu ochepa. Anapambana nkhondoyo pa adani awo. Anatenganso malo awo amene anali awo ndipo anayamba kukoloranso.

Pamene amphamvu a Midiyani, Amaleki ndi ena anakumana pamodzi kufuna kuthirana nkondo ndi anthu a Mulungu, Mzimu wa Mulungu unabwera pa Gideoni. Mawu a Chiheberi oti “unadza pa Iye amatanthauza “kuvekedwa”. Mphamvu ya Mulungu inapatsidwa pa Gideoni munthawi ya chosowa osati nthawiyo isanafike kapena kutsogolo. Muzapezanso zimenezi mmoyo wanu. Mphamvu yokonzekeretsa ya Mulungu simabwera pa inu pokhapokha mumvera kuitana kwake.

Malo amene adani amakhala anali a chigwa cha dzombe. Nganira zawo zinali ngati mchenga wa panyanja. Anali anthu ambiri. Gideoni anadabwitsa adani ndi lipenga ndi kuwala kwa kwa zounikira. Chinali chpwirikiti mu mbiri. Chigonjetso cha Gideoni chinali cha ndondomeko yabwino imene analumikizana bwinonso pa ntchito yawo, koma zinapitilira aponso. Inali ntchito yopatulidwa ndi yokonzekeredwa ndi mphamvu ya Mulungu.

Mukhonza kukhala munthu wofooka ndi wamantha amene mumakhalanso ndi anthu amantha amene chiwerengero chawo chinali chochepa. Komatu Mulungu akhoza kukupatsani mphamvu monganso anampasa Gideoni. Kapena ndinu wamng’ono mwa anthu amene muli nawo, mu chuma, kapena katundu? Kondwerani, Mulungu amakondwera ndi kuchita zinthu zazikulu kudzera mu zinthu zochepa, ndipo akatero amalandira ulemmero.

Nkhani ya Gedioni imaonetsera za ankhondo owerengeka, amene anakonzekeredwa ndi mphamvu ya Mulungu, amene anali ndi ndondomeko ya masomphenya amodzi ndi cholinga chofuna kugonjetsa adani awo.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Kodi kukonzekeredwa kunapatulidwa motani?

---

3. Kodi ndi mawu ati amene amalongosola za kukonzekeretsedwa molingana ndi Baibulo?

---

4. Lembani lamulo limodzi la Mbaibulo la kukonzekeretsa ena.

---

5. Longosolani za mmene kukonzekeretsedwa kunanenedwa mu mpingo wa Chipangano Chatsopano.

---

---

6. Lembani zitsanzo za kukonzekere za mu Chipangano Chakale.

---

---

7. Ombani mkota pa zimene mwaphunzira zokhudzana ndi moyo wa Gideoni.

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)



## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

Mafanizo ambiri a mu Chipangano Chatsopano amene Yesu anawagwiritsa ntchito amaulula za kufunika kwa kukonzekeretsedwa. Werengani za mafanizowa:

1. Okhulupirira ayenera kukonzekeretsedwa kuti afunefune otayika ku uchimo:
  - Fanizo la nkhusa yosochera: Mateyu 18:12-14; Luka 15:4-7
  - Fanizo la ndalama yotaika: Luka 15:8-10
  - Fanizo la mwana wolowerera: Luka 15:11-32
  
2. Okhulupirira akuyenera kukonzekeretsedwa pa kubwera kwa Yesu:
  - Fanizo la matelente: Mateyu 25:14-30; Luka 19:11-27
  - Fanizo la munthu wa paulendo wautali: Marko 13:34-37
  - Fanizo la akapolo: Mateyu 24:43-51; Luka 12:39-46
  - Fanizo la akapolo woyang'anira: Luka 12:36-38
  - Fanizo la anamwali khumi: Mateyu 25:1-12
  
3. Okhulupirira ayenera kukonzekeretsedwa kuti agwire ntchito ya Mulungu yofalisa uthenga wabwino:
  - Fanizo la wofesa: Mateyu 13:3-8; Marko 4:3-8
  - Fanizo la nansongole ndi tirigu: Mateyu 13:24-30
  - Fanizo la nkhusa: Mateyu 13:47-50
  - Fanizo la mbeu ya mpiru: Mateyu 13:31-32; Marko 4:31-32; Luka 13:19
  - Fanizo la matalente: Mateyu 25:14-30; Luka 19:11-27
  - Fanizo la zokolola: Mateyu 9:37-38; Luka 10:2

## CHAPUTALA CHA 3

### MOTO WA MULUNGU

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.
- Kukambirana ubale wa pakati za uzimu ndi moto wa kudziko.
- Kutchula “moto wa Mulungu.”
- Kulemba chidule cha chimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza moto wa pa pentekosite.
- Kudziwa cholinga cha moto wa Mulungu.
- Kulongosola za mmene tingakhalire ndi moto wa Mulungu.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Atatha tsono Solomo kupemphera, moto unatsika kumwamba, nunyeketsa nsembe yopsereza, ndi nsembe zophera; ndipo ulemerero wa Yehova unadzaza nyumbayi.**

**Ndipo ansembe sanakhoza kulowa m'nyumba ya Yehova, popeza ulemerero wa Yehova unadzaza nyumba ya Yehova.**

**Ndi ana onse a Israyeli anapenyererera potsika motowo, ndi pokhala ulemerero wa Yehova panyumbayi; nawerama nkhope zao panso poyalidwa miyala, nalambira, nayamika Yehova, nati, Pakuti Iye ndiye wabwino, pakuti cifundo cace cikhala cikhali (II Mbiri 7:1-3).**

#### MAWU OYAMBA

Mu Chaputala cha 2 chimene mwachisanthula zokhuza kukonzekeretsedwa, mwaphunzira kuti Mulungu amayenda kudzera mwa anthu amene amemezadwa kaya ndi ambiri kapena ochepa. Chaputala ichi ndi choyamba cha machaputala chimene chikuika chidwi pa zinthu za uzimu zimene zimakonzeretsa anthu a Mulungu. Mu izi kapena phunziro likubwerali, muphunzira moto wa Mulungu, ulemerero wa Mulungu ndi malambiro a Mulungu.

Pumani kaya ndipo werenganinso Vesi Lotsogolera la I Mbiri 7:1-3. Mupeza kuti moto wa Mulungu unagwa koyamba, keneko ulemerero wa Mulungu unavumbuluka, ndipo komaliza anthu a Mulungu analowa mu kulambira. Moto wa Mulungu, ulemerero wa Mulungu ndi malambiro a Mulungu ndi mphamvu za uzimu zimene zimakonzeretsa ndi kumemeza anthu a Mulungu kuti agwire ntchito.

## MOTO WA KUDZIKO

Pali ubwino wambiri wa moto wa kudziko lapansi. Moto umapereka mphamvu ndi kufunda. Umakonzekeretsa chakudya. Moto umaperekanso phulusa limene lipatipasa manyowa a mmunda wa mbewu zathu.

Moto umanyeketsa zinthu zoipa. Umaotchaso zonyasa za golide ndi siliva. Moto umakopa anthu, zimene zimaonekera kwa anthu amene amazungulira chinthu chimene chikuyaka moto. Moto umayasa moto unzake, koma umathima ngati suyasadwanso. Lawo la moto limene likuthima, lingyakenso kukhala moto woyaka kwambiri.

## MOTO WA KU UZIMU

Moto wa kudziko umafana ndi wa ku uzimu. Moto wa Mulungu umabweretsa mphamvu pa ntchito ya Mulungu. Umatenthesa zozizira, komanso mzimu wosasintha. Umabweretsa chakudya cha uzimu ndi zokolola za ku uzimu. Moto wa Mulungu umanyeketsa zoipa za mmoyo wathu, umagwira ntchito monganso mmene umachitira ndi golide ndi siliva mu dziko la kuthupi ndi kuotcha zonse zimene ndi zoipa.

Munthu amene wayakitsidwa ndi moto wa Mulungu amakopa anthu ku uthenga wa mmawu. Monganso moto wa kudziko, moto wa uzimunsu umayasa moto umzake. Wokhulupirira amene wayaka ndi chifundo pa iwo amene ndi otayika ndi kuonetsa mphamvu ya Mulungu, amayasa miyoyo ya iwo amene ali nawo chifupi.

Koma monga moto wa kudziko, moto wa uzimu umayeneranso uziyakabe. Kodi inalipo nthawi pamene munali wauzimu kwambiri ndi moto wa Mulungu koposa mmene mulili apapa lero? Lawi la moto limene likuthima, likhoza kuyakanso ngati lakolezedwa.

Monga ngati mmene Mulungu amaperekera moto pa gula la nsembe, amaperekanso moto kuchokera kumwamba kuti ukhudze moyo wanu. Koma muli ndi udindo wosunga motowo kuti uziyakabe (Levitiko 9:24, II Mbiri 7:11). Inuyo mumayakatu ku uzimu. Chikhalidwe chanu cha uzimu chimalengedwa kuti chizikhala choyaka ndi moto wa Mulungu. Ili ndilo pemphero lathu la kwa inu mu phunziroli “Yakirani Mulungu.”

## MULUNGU NDI MOTO

Baibulo limayankhula kwambiri za moto wa Mulungu:

**Pakuti Yehova Mulungu wanu ndiye moto wonyeketsa, ndi Mulungu wansanje (Deuteronomo 4:24)**

**Pakuti Mulungu wathu ndiye mota wonyeketsa (Ahebri 12:29)**

Atumiki a Mbaibulo amene anali ndi masomphenya a Mulungu analemba kuti kupezeka kwake kunali ngati moto:

**Ndipo ndinapenya, ndipo taonani, cifaniziro ca maonekedwe a moto; kuyambira maonekedwe a m'cuuno mwace ndi kungsi kwace, moto; ndi kuyambira m'cuuno mwace ndi kumwamba kwace, monga maonekedwe a ceza, ngan citsulo cakupsa (Ezekieli 8:2)**

**Ndinapenyenera mpaka anaikapo mipando yacifumu, nikhalapo Nkhalamba ya kale lomwe, zobvala zace zinali za mbu ngati cipale cofewa, ndi tsitsi la pa mutu pace ngati ubweya woyera, mpando wacifumu unali malawi amoto, ndi njinga zace moto woyaka. Mtsinje wamoto unayenda woturuka pamaso pace, zikwi zikwi anamtumikira, ndi unyinjji wosawerengeka unaima pamaso pace, woweruza mlandu anakhalapo, ndi mabuku anatssegulidwa (Danieli 7:9; 10:6).**

**Ndipo tsitsi la pamutu pace linali loyera ngati ubweya woyera, ngati cipale cofewa; ndi maso ace ngati lawi la moto (Chibvumbulutso 1:14, 3:18 onaninso Masalmo 18:8,12)**

### **KODI MOTO WA MULUNGU NDI CHIYANI**

Pamene tikukamba za moto wa Mulungu, sitikukamba za moto wa ku dziko lapansi. Yesu anati:

**Ine ndinadzera kuponya mota pa dziko lapansi; ndipo ndifunanji, ngati unatha kuyatsidwa? (Luka 12:49)**

Kodi moto wa Mulungu ndi chiyani? Tikamakamba za moto wa Mulungu timakamba za moto wa pa tsiku la pentekosite umene kunali kutsanulidwa koyamba kwa Mzimu Woyera kumene kunaonekera:

**Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana, onga amoto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekha wayekha. Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa (Machitidwe 2:3-4)**

Moto wa Mulungu ndi moto wa pa pentekosite. Ndi moto umene umamasula lilime lanu kuti lilankhule. Ndi moto umene umapereka mphamvu kuti muthe kukwaniritsa utumiki wotumudwa.

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko (Machitidwe 1:8)**

Yesu anati:

**Inetu ndikubatzani inu ndi madzi kuloza ku kutembenuka mtima; koma Iye wakudza pambuyo panga, ali wakundiposa mphamvu, amene sindiyenera kunyamula nsapato zace: Iyeyu adzakubatzani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto (Mateyu 3:11)**

## **MOTO WA PA TSIKU LA PENTEKOSITE**

Izi ndi zina mwa zoonazake za moto wa pentekosite:

### **UMAYATSIDWA NDI MULUNGU:**

Mobwereza mmawu, Mulungu amanena kuti “adzayatsa moto” (onani Yereimiya 21:14; 22:7; 49:27; 50:32; Amosi 1:14; 2:2, 5). Moto wa Mulungu si za mmalingaliro kapena zokumvaimva. Sumayatsidwa ndi kuimba nyimbo zofulumira kapena kulalikira mokweza. Umayatsidwa ndi kukolezedwa ndi Mulungu. Moto wa pentekosite umayatsidwa ndi Mulungu mwini.

**komatu ici ndi cimene cinanenedwa ndi mneneri Yoeli,**

**Ndipo kudzali m' masiku otsiriza, anena Mulungu,  
Ndidzathira ca Mzimu wansa pa thupi liri lonse,  
Ndipo ana anu amuna, ndi akazi adzanenera,  
Ndipo anyamata anu adzaona masomphenya,  
Ndi akulu anu adzalota maloto;  
Ndiponso pa akapolo anga ndi pa adzakazi anga m' masiku awa  
Ndidzathira ca Mzimu wanga; ndipo adzanenera (Machitidwe 2:16-18).**

### **NDI MOTO UMENE UMATYAKA OPANDA MAFUTA:**

Werengani nkhani ya Mose ndi chitsamba choyaka moto mu Eksodo 3. Ichi ndi chitsanzo cha chilengedwe cha choonadi chachikulu. Moto wa Mulungu umakana kuthekera kwa mafuta kuyasa tchire ndi kupitiliza kuyasa. Chodzizwa sichili mu samba loyaka moto monga zimakhallira moto opanda mafuta.

Mose anadziwa kuyambira kumene amachokera pokupha mu Igupto poona kuti sangadalirensa maganizo ake kapena mphamvu ya ntchito ya uzimu imene Mulungu anamuitanira. Mu tsamba loyaka Mulungu anaonetsera kuti moto wake umayaka popanda mafuta. Mukhoza kuyesera ndi kulephera mu ntchito ya Mulungu. Koma moto wa Mulungu imakana mafuta a luso lanu lachibadwidwe.

### **NDI OPITILIRA:**

Mulungu amapereka moto, koma muli ndi udindo osunga motowo kuti uziyakabe:

### **Moto uziyakabe pa guwa la nsembe, wosazima (Levitiko 6:13)**

Mulungu amafuna kuti mukupize Makala a moyo wanu. Amafuna kuti muyasire ku ufumu wa Mulungu.

## **UMAGWIRIZANA NDI CHIKHALIDWE CHAKE:**

Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu imagwirizana ndi moto:

**Ndipo mu mpando wacifumu mudaturuka mphezi ndi mau ndi mabingu. Ndipo panali nyali zisanu ndi ziwiri za mota zoyaka ku mpando wacifumu, ndiyo Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu (Chibvumbulutso 4:5)**

Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu ndi:

- |                           |              |
|---------------------------|--------------|
| 1. Choonadi:              | Yohane 16:13 |
| 2. Chisomo:               | Ahebri 10:29 |
| 3. Moyo:                  | Aroma 8:2    |
| 4. Umwana:                | Aroma 8:15   |
| 5. Chiyero:               | Aroma 1:4    |
| 6. Luntha ndi vumbulutso: | Aefeso 1:17  |
| 7. Ulemerero:             | I Petro 4:14 |

Pamene moyo wanu wakhudzidwa ndi moto wa Mulungu, mzimu wake wa umwana umagwira ntchito mwa inu. Choonadi chake, moyo, chiyero, ndi ulemerero zimayaka mmoyo wanu.

## **UMAGWIRIZANA NDI PEMPHERO:**

Werengani nkhani ya Eliya pa phiri la Karimeri mu I Mafumu 18. Pamene Eliya anapemphera, moto wa Mulungu unatsika. Ngati tikufuna kukhala ndi moto wa pentekosite, tiyenera kuphunzira kupemphera. Mu chipinda cha pamwamba, okhulupirira anapemphera kwa masiku ochuluka ndipo analalikira uthenga kwa mphindi khumi. Timapemphera kwa mphindi khumi ndi kulalikira kwa maola ambiri osadwa chifukwa chake moto sutifikira.

## **UMAGWIRIZANA NDI MAWU AKE:**

Mawu a Mulungu amagwirizana ndi moto:

**Kodi mau anga safanafana ndi moto? ati Yehova... (Yeremiya 23:29)**

**Ndipo ngati nditi, Sindidzamchula Iye, sindidzanenanso m'dzina lace, pamenepo m'mtima mwanga muli ngati moto wotentha wotsekedwa m'mafupa anga, ndipo ndalema ndi kupirira, sindingathe kupiriranso (Yeremiya 20:9)**

**Cifukwa cace Yehova Mulungu wa makamu atero, Cifukwa munena mau awa, taona, ndidzayesa mau anga akhale m'kamwa mwako ngati moto, anthu awa ndidzayesa nkhu, ndipo udzawatha iwo (Yeremiya 5:14)**

**ndikulangiza ugule kwa Ine golidi woyengeka m'moto, kuti ukakhale wacuma, ndi zobvala zoyera, kuti ukadzibveke, ndi kuti manyazi a usiwa wako asaoneke; ndi mankhwala opaka m'maso mwako, kuti ukaone (Chivumbulutso 3:18)**

**6Mau a Yehova ndi mau oona; Ngati siliva woyenga m'ng'anjo yadothi, Yoieretsa kasanu ndi kawiri (Masalmo 12:6).**

Pamene moto wa Mulungu wakhudza moyo wanu, mawu ake adzakhala ngati moto wotseka mmafupa anu. Ndipo udzayaka mkati mwanu usiku ndi usana. Werengani Yeremiya 36, pamene mfumu anayesera kuononga mawu a Mulungu, koma anapezeka kuti sanakwanitse kuletsa mawu a moto.

#### **UMAGWIRIZANA NDI CHOTENGERA:**

Moto wa Mulungu umafuna chotengera choyakiramo. Choterengera chilichonse cha moto mu chigono kapena mu kachisi chimakhala choyera. Mukhoza kukhala woyera pamene moto wosambitsa wa chotengera cha Yesu wayaka mu moyo wanu. Ubale wa moto ndi chotengera cha Yesu chinaonekera pamene Aroni anaima pakati pa amoyo ndi akufa.

**Ndipo Mose anati kwa Aroni, Tenga mbale yako yofukiza, nuikemo mota wa ku guwa la nsembe, nuikepo cofukiza, nufulumire kumuka ku khamulo, nuwacitire cowatetezera; pakuti waturuka mkwiyo pamaso pa Yehova; wayamba mliri (Numeri 16:46)**

#### **CHOLINGA CHA MOTO WA MULUNGU**

Pamene mukuwerenga zolinga za moto wa Mulungu, mudzamvetsa chifukwa chimene moto wa ku uzimu ndi ofunika polimbikitsa ndi kukonzekera utumiki.

#### **UMAPATSA MPHAMVU UTUMIKI WANU:**

Munasankhidwa ndi Mulungu pakati pa zowawa za moto. Mumapatsidwa mphamvu ndi Mulungu pofuna kukwaniritsa utumiki wanu kudzera mu moto wake onyeketsa:

**monga pamene moto uyatsa zitsamba, ndi moto uwiritsa madzi; kudziwitsa kwa amaliwongo anu dzina lanu, kuti amitundu anthunthumire pamaso panu (Yesaya 64:2)**

**Taona ndakuyenga, koma si monga siliva, ndakuyesa iwe m'ng'anjo ya masautso (Yesaya 48:10)**

**Amene ayesa mphepo amithenga ace; Lawi la moto atumiki ace (Masalmo 104:4)**

#### **UMAONETSERA KUPEZEKA KWA MULUNGU:**

Chizindikiro cha moto wa kudziko chimagwiritsidwa ntchito kuonetsera kupezeka kwa Mulungu mu Chipangano Chatsopano:

**Pamenepo Yehova ananena ndi inu ali pakati pa moto; munamva kunena kwa mau, osaona maonekedwe, koma kunenako (Deuteronomo 4:12)**

**Ndipo tsiku loutsa kacisi mtambo unaphimba kacisi, ndiwo cihema cokomanako; ndipo madzulo padaoneka pakacisi ngati moto, kufikira m'mawa (Numeri 9:15)**

Moto wa ku uzimu wa Mulungu woyaka mmoyo wanu umaonetsera kupezeka kwa Mulungu. Utumiki wanu umayenerezedwa ndi kupezeka kwa Mulungu.

#### **UMAPEREKA CHITSOGOZO:**

Pamene anthu amemezgedwa ndi ntchito ya Mulungu, akuyenera kukhala ndi kolowera. Moto wa Mulungu ndi chizindikiro cha chitsogozo kwa anthu ake:

**Ndipo Yehova anawatsogolera usana ndi mtambo njo kuwatsogolera m'njira; ndi usiku ndi moto njo, wakuwawalitsira; kuti ayende usana ndi usiku; sanacotsa mtambo usana, kapena mtambo wamoto usiku, pamaso pa anthu (Eksodo 13:21-22)**

**ndipo adzawauza okhala m'dziko muno; adamva kuti inu Yehova muli pakati pa anthu awa; pakuti muoneka mopenyana, Yehova, ndi mtambo wanu umaima pamwamba pao, ndipo muwatsogolera, ndi mtambo njo msana, ndi moto njo usiku (Numeri 14:14) onaninso Nehemiya 9:12,19; Masalmo 78:14; 105:39)**

**amene anakutsogolerani m'njira, kukufunirani malo akumanga mahema anu ndi mota usiku, kukuonetserani njira yoyendamo inu, ndi mumtambo usana (Deuteronomo 1:33)**

#### **KUMATSUKA NDI KUYERETSA:**

Munthawi ya Chipangano Chakale, moto umagwiritsidwa ntchito poononga zinthu zomwe sizinali za umulungu.

Chilichonse chimene chinali chimakhudzidwa ndi khate chimatenthedwa ndi moto: Levitiko 13:52



Mafano amayenera kuthemthedwa ndi moto: Deuteronomo 7:5;25; 9:21; 12:3; I Mbiri 14:12; Yesaya 37:19; Yereimiya 43:13; Mika 1:7

Zotsala za kwa adani zimatenthedwanso: Deuteronomo 13:16

Moto wa Mulungu mmoyo wa okhulupirira umayeresanso, kutentha zodetsa:

**Taona, ndalenga wacipala amene abvukuta moto wamakala, ndi kuturutsamo cida ca nchito yace; ndipo ndalenga woononga kuti apasule (Deuteronomo 54:16)**

**Ndi gawo lacityatulo ndidzalitengera kumoto, ndi kuwayenga ngati ayenga siliva, ndi kuwayesa monga ayesa golidi; adzaitana dzina langa, ndipo ndidzawamvera; ndidzati, Awa ndi anthu anga; ndi iwo adzati, Yehova ndi Mulungu wanga (Zakariya 13:9)**

**Koma ndani adzampirira tsiku la kudza kwace? ndipo adzaima ndani pooneka Iye? pakuti adzanga moto wa woyenga, ndi sopo wa otsuka (Malaki 3:2)**

Ngati mumagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu, zoipa zanu zonse ndiye kuti ziyenera kutenthedwa mmoyo wanu. Ngati mukana kueyeretsedwaku, mukhala ngati wokana siliva zimene sizabwino:

**Onse ali opikisana ndithu, ayendayenda ndi maugogodi; ndiwo mkuwa ndi citsulo; onsewa acita mobvunda; 29mbvukuto yatenthedwa ndi moto; mthobvu watha ndi moto wa ng'anjo; ayenga cabe; pakuti oipa sacotsedwa. Anthu adzawacha nthale ya siliva, pakuti Yehova wakana iwo (Yereimiya 6:28-30)**

## **UMAKUSIYANITSA:**

Moto umagwiritsidwa ntchito posiyanyitsa, za kudziko la kuthupi ndi la ku uzimu:

**zonse zakulola moto, mupititse m'moto, ndipo zidzakhala zoyera; koma muziyeretsenso ndi madzi akusiyanyitsa. Koma zonse zosalola moto, muzipititse m'madzi (Numeri 31:23)**

**Cifukwa cace monga ngati lilime la moto likutha ciputu, ndi monga udzu wouma ugwa pansu m'malawi, momwemo muzu wao udzakhala monga wobvunda, maluwa ao adzauluka m'mwamba ngati pfumbi; cifukwa kuti iwo akana cilamulo ca Yehova wa makamau, nanyoza mau a Woyera wa Israyeli (Yesaya 5:24)**

**Ndiponso tsopano lino nkhwangwa yaikidwa pa mizu ya mitengo; cifukwa cace mtengo uli wonse wosabala zipatso zabwino udulidwa nuponyedwa pamoto (Mateyu 3:10) onaniso Mateyu 7:19 ndi 13:40-42**

**Ngati wina sakhala mwa Ine, watayika kunjira monga nthambi, nafota; ndipo azisonkhanitsa nazitaya kumoto, nazitentha (Yohane 15:6)**

Pamene mwakonzeretsedwa ndi Mulungu moona mtima, ndiye kuti mumasiyanitsidwa ku uchimo ndi zinthu za dziko lapansi. Mumapatulidwira ku cholinga cha ntchito yake ya ufumu.

### **UMAYESA:**

Moto wa Mulungu ndi “moto woyesa.” Moto umayesa chikhulupiriro chanu mwa Mulungu:

**kuti mayesedwe a cikhulupiriro canu, ndiwo a mtengo wace woposa wa golidi amene angotayika, ngakhale ayasedwa ndi moto, akapezedwe ocitira ciyamiko ndi ulemerero ndi ulemu pa bvumbulutso la Yesu, Kristu (1 Petro 1:7)**

Motowo umayesanso ntchito zanu za Mulungu:

**nchito ya yense idzaonetsedwa; pakuti tsikulo lidzaisonyeza, cifukwa kuti yabvumbuluka m'moto; ndipo mota wokha udzayesera nchito ya yense ikhala yotani. Ngati nchito ya munthu ali yense khala imene anaimangako, adzaandira mphotho. Ngati nchito ya wina itenthedwa, zidzaonongeka zace; koma iye yekha adzapulumutsilwa; koma monga momwe mwa moto (I Akorinto 3:13-15)**

Ziputu, maudzu ndi zonse za pa mtunda, zizaotchedwa mu moto. Golide ndi siliva za pansa pa nthaka sizizapsa ndi moto. Chilichonse chimene chooneka chimene muchita koma mwamasewera chidzaonongedwa ndi moto wa Mulungu. Ntchito yabwino ya muyaya yamtengo wapatali imene sioneka ndipo imachitdwa ulemu ndi anthu.

### **UMAONETSA CHITSIMIKIZO:**

Werengani nkhana ya kugalukira kwa Kora mu Numeri 16. Pamene moto unatsika, unanyeketsa anthu ogalukira ndi kuonetsa chitsimikizo cha Mulungu pa atsogoleri ake. Mu II Mafumu 1:10-14 Eliya anatsimikizidwa ngati munthu wa Mulungu pamene moto wa Mulungu unatsika ndi kunyeketsa akalonga ndi anthu awo. Ngakhale Mulungu sangatumize moto weniweni pofuna kuonetsera chitsimikizo, moto wa uzimu wa Mulungu umene umakhala pa moyo wanu ndi utumiki wanu, umaonetsera chitsimikizo chake.

### **UMAONETSERA MPHAMVU YAKE:**

Onaniso kawiri nkhani ya Eliya pa phiri la Kalimeri mu I Mafumu 18. Mphamvu ya Mulungu inaoneka mu moyo wake mu moto. Mulungu akhoza osaonetsa mphamvu yake mmoyo wanu ngati mtumiki, koma adzaonetsa moto wa ku uzimu. Pamene anthu akuchitira umboni mawu a mphamvu ndi zozizwa, azazindikira Mulungu mmodzi woona wamoyo.

### **NDI CHIDA CHA UZIMU:**

Moto wa Mulungu ndi chida cha uzimu:

**Ndipo kunali, ulonda wa mamawa, Yehova ali m'moto ndi m'mtambo njo anapenyera pa ulendo wa Aaigupto, Baubvuta ulendo wa Aaigupto. Ndipo anagurula njinga za magareta ao, nawayendetsa molemetsa; pamenepo Aaigupto anati, Tithawe pamaso pa Israyeli; pakuti Yehova alikuwagwirira nkondo pa Aaigupto (Eksodo 14:24).**

**Potero mudziwe lero lino, kuti Yehova Mulungu wanu ndiye amene aoloka pamaso panu ngati moto wonyeketsa; iye adzawaononga, iye adzawagwetsa pamaso panu; potero mudzawapitikitsa, ndi kuwaononga msanga, monga Yehova analankhula ndi inu (Deuteronomo 9:3)**

**Aletsa nkondo ku malekezere adziko lapansi; Athyola uta, nadula nthungo; (Maslmo 46:9)**

**Adzafika Mulungu wathu, ndipo sadzakhala cete: Moto udzanyeka pankhope pace (Masalmo 50:3).**

Mdani alin ndi moto wonyeketsa wokozedwa ndi cholinga choononga chilichonse chimene ndi chabwino ndi choyera mu moyo wanu. Wonani gawo la kuptitiliza kuphunzira la phunziroli. Monga mmene mukulimbana ndi moto mu dziko lapansi pokhala ndi zothimisa moto, mumalimbananso ndi moto wa mdani ndi moto wa uzimu wa Mulungu:

**Ndipo iwo okhala m'midzi ya Israyeli adzaturuka, nadzasonkha moto, nadzatentha zida za nkondo, ndi zikopa zocinjiriza, mauta, ndi mibvi, ndi ndodo, ndi mikondo; ndipo adzasonkha moto nazo zaka zisanu ndi ziwiri; osatenga nkuni kuthengo, kapena kuzitema kunkhalango; popeza adzasonkha moto ndi zidazo; nadzafunkha iwo amene anawafunkha, ndi kulanda zao za iwo adalanda zaozo, ati Ambuye Yehova (Ezekieli 39:9-10)**

Moto wa Mulungu umanyeketsa moto wa mdani:

**Adandizinga ngati njuci; Anazima ngati moto waminga; Indedi, m'dzina la Yehova ndidzawaduladula (Masalmo 118:12)**

**Makala amoto awagwere; Aponyedwe kumoto; M'maenje ozama, kuti asaukenso (Masalmo 140:10)**

**Pakuti udzaunjika makala amoto pamtu pace; Ndipo Yehova adzakupatsa mphotho (Miyambo 25:22)**

**Moto umtsogolera, Nupsereza otsutsana naye pozungulirapo (Masalmo 97:3).**

**Ndipo m'gulu mwao mudayaka moto; Lawi lace lidapsereza oipawo (Masalmo 106:18)**

Ngakhale Paulo mtumwi anachita mu dziko la thupi, kuti tiyenera kugwedeza machenjerero a satana ndi moto wa Mulungu:

**Koma pamene Paulo adaola cisakata ca nkhuni, naciika pamoto, inaturukamo njoka, cifukwa ca kutenthaku, nilumadzanja lace (Machitidwe 28:3)**

Zinanenedwa kwa munthu wa chikhulupiriro mu buku la Ahebri 11, za iwo amene anathimisa ukali wa moto (Ahebri 11:34).

### **MMENE TINGAPEZERE MOTO WA MULUNGU**

Umu ndi mmene mungapezere ndi kukhala wopitilira ndi kusunga moto wa Mulungu mmoyo wanu:

#### **KUBADWA MWATSOPANO:**

Chifukwa cha moto wa Mulungu ndi moto wa uzimu, mukuyenera kukhala nawo mu uzimu mwanu. Izi zikutanthauza kuti mukuyenera kubadwa mwatsopano polapa machimo anu ndi kulandira Yesu kukhala mbuye ndi mpulumutsi wa moyo wanu.

#### **LANDIRANI UBATIZO WA MZIMU WOYERA:**

Mwaphunzira kuti moto wa Mulungu umafana ndi wa pa pentekosite wa ubatizo wa mzimu woyera. Choncho pali buku lotchedwa “Utumiki wa Mzimu Woyera limene lidzakutsogolerani kuti mukumane ndi ubatizo wa Mzimu Woyera.

#### **LORANI MOTO UYERETSE MOYO WANU:**

Monga mmene moto wa kudziko umayatsa zoipa za golide ndi siliva, moto wa Mulungu umanyeketsa zoipa mmoyo wanu wa uzimu. Kutu mupitilire kukhala ndi mphamvu ya Mulungu, mukuyenera kulora moto wa Mulungu kuti uyeretse. Pamene mukukana moto umene umanyeketsa zoipazi zili ngati kuthira madzi pa moto wa kudziko. Malawi amathimitsidwa.

#### **YASANI MOTO WINA:**

Mu dziko la kuthupi, moto umakula kwambiri malingana ndi mmene wapezerana ndi moto wina chifupi. Izi zili chomwechonso ku dziko. Ngati mukufuna kupitilira kukhala ndi moto wa Mulungu, mukuyenera kukhala wochitachita poyatsa moto wina wa anthu amene muli nawo chifupi. Mumachita izi pokwaniritsa lamulo la kutuma kwakukulu pofalisa uthenga wabwino kwa anthu ena. Moto umakopa anthu, zimene zimaonekera kuchokera ku khamu la anthu limene limasonkhana pamene chinachake chikuyaka. Lolani mot wa Mulungu umene uli mkati mwanu uyake ndi kukopa ndi kuyasa ku uzimu anthu ena.

#### **PITILIZANI KUTHIRA MOTO MAFUTA:**

Mu dziko lapansi pali chizolowezi choti moto umazima ngati supitilira kuthiridwa mafuta. Chomwechonse moto wa ku dziko la uzimu. Mukuyenera kuthira mafuta a uzimu ndi moto ndi kuwerenga mawu a Mulungu. Lawi loyaka limene lasala pang'ono kuthima likhoza kuyakanso kukhala moto wambiri.

### **MOTO, ULEMERERO NDI MALAMBIRO**

Moto wa Mulungu umafana ndi ulemerero wa Mulungu:

**Tsoka, okhala m'dziko la kunyanja, mtundu wa Akereti! Mau a Yehova atsutsana nawe, Kanani, dziko la Afilisti; ndidzakuononga, kuti pasakhale wokhala m'dziko (Zakariya 2:5)**

**ndipo munati, Taonani, Yehova Mulungu wathu anationetsa ulemerero wace, ndi ukuru wace, ndipo tidamva liu lace ali pakati pa mote; tapenya lero lino kuti Mulungu anena ndi munthu, ndipo akhala ndi moyo (Deuteronomo 5:24). Onaninso Eksodo 24:17.**

**Cifukwa cace lemekezani inu Yehova kum'mawa, ngakhale dzina la Yehova, Mulungu wa Israyeli, m'zisumbu za m'nyanja (Yesaya 24:15)**

Moto ndi ulemerero wa Mulungu zimagwirizana ndi kulambira. Dziwani kuti moto, ulemerero ndi kulambira zimachitika mu ndondomeko:

**Atatha tsono Solomo kupemphera, moto unatsika kumwamba, nunyeketsa nsembe yopsereza, ndi nsembe zophera; ndipo ulemerero wa Yehova unadzaza nyumbayi. Ndipo ansembe sanakhoza kulowa m'nyumba ya Yehova, popeza ulemerero wa Yehova unadzaza nyumba ya Yehova. Ndi ana onse a Israyeli anapenyenera potsika motowo, ndi pokhala ulemerero wa Yehova panyumbayi; nawerama nkhope zao panso poyalidwa miyala, nalambira, nayamika Yehova, nati, Pakuti Iye ndiye wabwino, pakuti cifundo cace cikhala cikhali (II Mbiri 7:1-3)**

Sitingakonzekeretsedwe ku ntchito ya utumiki ndi maganizo athu. Ukuyenera kukhaladi moto weniweni wa Mulungu wamoyo. Sitingakonzekeretsedwe ndi ulemerero wa munthu, munthu kapena dziko lapansi. Tikuyenera kukonzekeretsedwa ndi ulemerero wa Mulungu. Sitingalambire mongokwaniritsa. Kulambira kwathu kukuyenera kukhala kwa moto ndi ulemerero wa Mulungu.

Moto, ulemerero ndi kulambira, mu ndondomeko yotero.

Muphunziro likudzali, muyamba kuphunzira za “ulemerero.”

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Longosolani ubale ndi phindu la moto wa kudziko lapansi.

---

---

3. Perekani tanthauzo la moto wa Mulungu.

---

---

4. Lembani chidule cha zimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza moto wa pa pentekosite.

---

---

5. Tchulani zolinga za moto wa Mulungu.

---

---

6. Fotokozani za mmene mungakumanire ndi kusunga moto wa Mulungu mmoyo wanu.

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## CHAPUTALA CHA 4

### ULEMERERO WA MULUNGU

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pantima.
- Perekani tanthauzo la mawu oti “ulemerero.”
- Tchulani maziko a ulemerero.
- Lembani chidule cha chikhalidwe cha ulemerero wa Mulungu.
- Fotokozani kumene Mulungu amaulula ulemerero wake.
- Landirani “ulemerero” ngati mphatso yochokera kwa Mulungu.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Nyamuka, wala, pakuti kuunika kwake kwafika, ndi ulemerero wa Yehova wakuturukira. Pakuti taona, mdima udzaphimba dziko lapansi, ndi mdima wa bii mitundu ya anthu; koma Yehova adzakuturukira, ndi ulemerero wace udzaoneka pa iwe (Yesaya 60:1-2)**

#### MAWU OYAMBA

Kumayambiriro kwa phunziroli, talongosola za moto wa Mulungu, ulemerero ndi kulambira koono ngati mphamvu za uzimu zimene zimakonzekeretsa anthu a Mulungu ku utumiki (II Mbiri 7:1-3). Mu chaputala chomaliza mwaphunzira za moto wa Mulungu ndi kufunika kwake pokonzekeretsa inu ku ntchito ya utumiki poonetsera kupezeka kwake, mphamvu, chitsimikizo, kuyenereza utumiki wanu, kutsuka, kuyeretisa, kusiyanita ndi kupereka chitsogozo. Mwaphunziranso kufunika kwake ngati chida cha uzimu cholimbana ndi Satana mdani.

Chaputalachi ndi choyamba cha maphunziro a ulemerero wa Mulungu. Phunziroli likukamba zoono zokhudza ulemerero wa Mulungu. Mu chaputala cha 5, muphunzira “cholinga cha ulemerero wa Mulungu” ndipo mu chaputala cha 6 muphunzira za “mmene mungampatsire Mulungu ulemerero.” Mu chaputala cha 7 ndi 8 muphunzira za mmene mungabwenzere ulemerero wotayika.

Mukhoza kukhala wokhumudwa, wozizira kapena wopanda moyo wa uzimu. Koma mawu a Mulungu ali kwa inu...

**Nyamuka, wala, pakuti kuunika kwake kwafika, ndi ulemerero wa Yehova wakuturukira. Pakuti taona, mdima udzaphimba dziko lapansi, ndi mdima wa bii**

**mitundu ya anthu; koma Yehova adzakuturukira, ndi ulemerero wace udzaoneka pa iwe (Yesaya 60:1-2)**

Mavesiwa ali gawo limodzi la uneneri okudza Israyeli, mtundu umene ndi wa mpingo. Inu ndi gawo limodzi la mpingo, choncho vesiyi ikuonetsa kuti ulemerero wa Mulungu uli pa inu ngati munthu komanso ngati mpingo wonse. Ambuye analonjense:

**ndipo ulemerero wa Yehova udzabvumbulutsidwa, ndipo anthu onse adzauona pamodzi, pakuti pakamwa pa Yehova panena comweco (Yesaya 40:5)**

Vesili likuonetsa kuti thupi lonse lidzaona ulemerero wa Mulungu. Thupi likuonetsa ngati kusayenerezedwa kukhala ndi ulemerero wa Mulungu, koma ili ndi lonjezo la Mulungu! Mukuyenera kuona ulemerero wa Mulungu ukuvumbulutsidwa kwa inu, keneko mukuyenera kumvetsa kuti ndi chiyani, cholinga chake ndi mmene mungamulemekezere Mulungu.

### **TANTHAUZO LA ULEMERERO**

Ulemerero, ndi mawu amodzi aakulu mu chiyankhulo cha chingerezi. Palibe mawu amodzi abwino ofanana, koma pali mawu ena amene amalongosola za ulemerero.

Kupatsa ulemu, kukweza, kuwala, mphamvu, kuyamika, kufanana, kukongola ndi ena.

Pamene mawu a “ulemerero” akugwiritsidwa ntchito kwa Mulungu, amaonetsera umulungu wake. Ulemerero wa Mulungu umaonekera ku ubwino wake, kukongola, mphamvu, ungwiro wake. Ndipo kumbukirani kuti ulemerero wodabwisawu uli pa INU!

### **GWERO LA ULEMERERO**

Mulungu ndiye gwero la ulemerero umene tikuyankhula. Amatchedwa “Mulungu wa ulemerero” (Machitidwe 7:2). Mulungu ndiye amene amapereka ulemerero kwa anthu. Mneneri Danieli analankhula kwa mfumu...

**Inu mfumu ndinu mfumu ya mafumu, pakuti Mulungu wa Kumwamba anakupatsani ufumu, ndi mphamvu yaikuru, ndi ulemu (Danieli 2:37)**

### **CHIKHALIDWE CHA ULEMERERO**

Izi ndi zoonza zofunika zokhudza ulemerero wa Mulungu:

#### **NDI WAMUYAYA:**

**Ulemerero wa Yehova ukhale kosatha; Yehova akondwere mu nchito zace (Masalmo 104:31)**

**Ndipo kwa Mfumu yosatha, yosabvunda, yosaoneka, Mulungu wa yekha, ukhale ulemu ndi ulemerero, kufikira nthawi za nthawi. Amen (I Timoteo 1:17)**



**Kwa iye kukhale mphamvu ku nthawi za nthawi. Amen (I Petro 5:11)**

**UMAGWIRIZANA NDI UKULU WAKE:**

Ndizalankhula za ulemerero ndi ukulu wake, ntchito zanu zodwabwitsa. Masalmo 145:5

Ulemerero wa ukulu wake ukunenedwa mu Yesaya 2:10, 19, ndi 21.

**UMAGWIRIZANA NDI KUFULA KWA MAWU AKE:**

**Ndipo Mulungu azapangitsa mau ake a ulemerero kumedwa (Isamueli 30:30)**

**UMAGWIRIZANA NDI MASO AKE:**

Yesaya amalankhula za maso a ulemerero wake (Yesaya 3:8).

**NDI WAPADERADERA:**

Ulemerero wa Mulungu superekedwa kwa wina:

**Ine ndine Yehova; dzina langa ndi lomweli; ndipo ulemerero wanga Ine sindidzapereka kwa wina, ngakhale kunditamanda kwa mafano osemmedwa (Yesaya 42:8)**

**Cifukwa ca Ine ndekha, cifukwa ca Ine ndekha ndidzacita ici, pakuti dzina langa lidetsedwerenji? ndi ulemerero wanga sindidzakupereka kwa wina (Yesaya 48:11)**

**UMAGWIRIZANA NDI CHIYERO CHAKE:**

**Manana ndi Inu ndani mwa milungu, Yehova? Manana ndi Inu ndani, wolemekezedwa, woyera, Woopsa pomyamika, wakucita zozizwa? (Eksodo 15:11)**

**Kumwamba kulalikira cilungamo cace. Ndipo mitundu yonse ya anthu ipenya ulemerero wace (Masalmo 97:6)**

**UMAGWIRIZANA NDI DZINA LAKE:**

**Atate, lemekezani dzina lanu. Pomwepo adadza mau ocokera Kumwamba, ndalilemekeza, ndipo ndidzalilemekezanso (Yohane 12:28)**

**Mukapanda kusamalira kucita mau onse a cilamulo ici olembedwa m'buku ili, kuopa dzina ili la ulemerero ndi loopsa, ndilo YEHOVA MULUNGU ANU (Deuteronomo 28:58)**

**ULI PAMWAMBA PA MIYAMBA:**

**Dzina lanu liposadi nanga pa dziko lonse lapansi! Inu amene munaika ulemerero wanu pa thambo la kumwamba (Masalmo 8:1)**

**yehova akwezeka pamwamba pa amitundu onse, Ulemerero wace pamwambamwamba (Masalmo 113:4)**

#### **ULI PAMWAMBA PA DZIKO LAPANSI:**

**Kwezekani pamwamba pa thambo, Mulungu; Ndi ulemerero wanu pamwamba pa dziko lonse lapansi (Masalmo 108:5, 57:5)**

#### **UMAGWIRIZANA NDI UFUMU WAKE:**

Ufumu wa Mulungu ndi wa ulemerero:

**Adzanenera ulemerero wa ufumu wanu, Adzalankhulira mphamvu yanu (Masalmo 145:11)**

Vesi ya 12 imakambanso za ukulu wa ulemerero wa ufumu wake (onani Danieli 7:14)

#### **UMAGWIRIZANA NDI MPANDO WAKE:**

Mpando wa Mulungu umatchedwa “mpando wa ulemerero” (I Samueli 2:8, Yereimiya 14:21; 17:12).

#### **UMAGWIRIZANA NDI NTCHITO YAKE:**

Baibulo limalengedza kuti ntchito ya Mulungu ndi ya ulemu ndi ya umelerero (Masalmo 11:3)

#### **UMAGWIRIZANA NDI MPHAMVU YAKE:**

Mau amakamba za ulemerero wa mphamvu yake (II Atesalonika 1:9).

#### **NDI WAUKULU:**

**Ndipo adzayimbira njira za Yehova; Pakuti ulemerero wa Yehova ndi waukuru (Masalmo 138:5)**

Ndimezi zikuonetsera kuti Mulungu amadziwika ndi ulemerero, kuimira ulemerero, ndi kuzungulilidwa ndi ulemerero. Ulemerero ndi chizindikiro cha chikhalidwe chake. Kumudziwa Mulungu bwinobwino ndi kudziwa ulemerero wake.

#### **KUMENE MULUNGU AMAULULA ULEMERERO WAKE**

Kuonjedzera pa zoonza zake za ulemerero wa Mulungu, Baibulo limakambanso za zimene Mulungu amaonetserako ulemerero wake:

## **CHILENGEDWE:**

Njira yoyamba imene Mulungu amaonetsera ulemerero kwa munthu ndi chilengedwe cha miyamba ndi pansi:

**Zakumwamba zimalalikira ulemerero wa Mulungu; Ndipo thambo lionetsa nchito ya manja ace (Masalmo 19:1)**

Yobu amakamba za machaputala ambiri olongosola za mmene Mulungu amaziululira yekha mu chilengedwe. Onani Yobu 38-41. Ngakhale mu zinthu zozowika monga mphenzi ndi madzi, ulemerero wa Mulungu umaululika (Masalmo 29:3)

Satana amalimbana ndi choonadi cha umulungu wa chilengedwe kwambiri pochita maboza ngati nkhani ya kusintha kwa zinthu (Evolution) chifukwa amdziwa kuti Mulungu amaonekera mu chilengedwe chake:

**Pakuti cilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yace yosatha ndi umulungu wace; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwiringula (Aroma 1:20)**

## **KUMWAMBA NDI DZIKO LAPANSI:**

Ulemerero wa Mulungu umaonekera kumwamba ndi dziko lapansi, monganso okhulupirira amamuonetsera mu matamando, malambiro, ndi kugawana uthenga wabwino ndi anthu ena:

**Kwezekani m'mwambamwamba, Mulungu; Ulemerero wanu ukhale pamwamba m'dziko lonse lapansi (Masalmo 57:11)**

**Ndipo dzina lace la ulemerero lidalitsike kosatha; Ndipo dziko lonse lapansi lidzale nao ulemerero wace. Amen, ndi Amen (Masalmo 72:19)**

## **MU NTCHITO ZAKE:**

**Nchito zanu zonse zidzakuyamikani, Yehova; Ndi okonedwa anu adzakulemekezani. Adzanenera ulemerero wa ufumu wanu, Adzalankhulira mphamvu yanu; Kudziwitsa ana a anthu zamphamvu zace, Ndi ulemerero waukuru wa ufumu wace. Ufumu wanu ndiwo ufumu womka muyaya, Ndi kuweruza kwanu kufikira mibadwo yonse yonse (Masalmo 145:10-13)**

## **MWA YESU:**

Ulemerero wa Mulungu umaonekera mwa Yesu, amene anali nawo ulemerero wa mulungu kuyambira ya chiyambi:

**Ndipo tsopano, Atate Inu, lemekezani Ine ndi Inu nokha ndi ulemerero umene ndinali nao ndi Inu lisanakhale dziko lapansi (Yohane 17:5)**

Mulungu anali chiyambi cha ulemerero. Yesu samalankhula za ulemerero wake, amalemekeza Mulungu (Yohane 8:50). Yesu sanadzilemekeze yekha. Mulungu anamulemekeza (Ahebri 5:5).

**Tsono m'mene adaturuka, Yesu ananena, Tsopano walemekezeka Mwana wa munthu, ndipo Mulungu walemekezedwa mwa iye; ndipo Mulungu adzamlemekeza iye mwa iye yekha, adzamlemekeza iye tsopano apa (Yohane 13:31; 17:1)**

**Pakuti analandira kwa Mulungu Atate ulemu ndi ulemerero, pakumdzera iye mao otere ocokera ku ulemerero waukuru, Uyu ndi Mwana wanga wokondedwa, amene Ine ndikondwera naye (II Petro 1:17)**

## **MU CHIPULUMUTSO:**

Ulemerero wa Mulungu umaonekera mu dongosolo lake la chipulumutsi:

**Ulemerero wace ngwaukuru mwa cipulumutso canu: Mumcitira iye ulemu ndi ukulu (Masalmo 21:5)**

## **MALO APADERA:**

Mulungu waonetsera ulemerero wake ku malo apaderadera. Mu nthawi yakale, amaonetsera ku madera ena. Anaonetsera ulemerero wake mu Chipangano Chatsopano mu chigono ndi mu kachisi. Mulungu anaonetsera ulemerero wake kwa Israyeli, ndipo tsopano akuonetsera ulemerero wake kumpingo kwa okhulupirira payekhapyekha.

### **1. Malo apadera:**

Mulungu anamuza Ezekieli kupita ku malo amene Mulungu azaonetsera ulemerero, monganso mmene anaonetsera ku mtsinje wa Keba:

**Ndipo ndinauka ndi kuturuka kumka kucidikha, ndipo taonani, ulemerero wa Yehova unaimako monga ulemerero uja ndinauona ku mtsinje Kebara, ndipo ndinagwa nkhope pansu (Ezekieli 3:23)**

**Ndipo taonani, pomwepo panali ulemerero wa Mulungu wa Israyeli, monga mwa maonekedwe ndinawaona ku cidikha cija (Ezekieli 8:4)**

Mose anaudzidwa kuima pa thanthwe pamene Mulungu anamululira ulemerero wake (Eksodo 33:22)

### **2. Mu chihema**

Ulemerero wa Mulungu umaonekera mu Chipangano Chakale mu chihema:

**Ndipo pamenepo ndidzakomana ndi ana a Israyeli; ndipo chihema cidzapatulidwa ndi ulemerero wanga (Eksodo 29:49)**

**Pamenepo mtambo unaphimba cihema cokomanako, ndi ulemerero wa Yehova unadzaza kacisiyo.**

**Ndipo Mose sanathe kulowa m'cihema cokomanako, popeza mtambo unakhalabe pamenepo; ndi ulemerero wa Yehova unadzaza kacisi. (Eksodo 40:34-35)**

**Koma khamu lonse lidati liwaponye miyala, Ndipo ulemerero wa Yehova unaoneka m'cihema cokomanako kwa ana onse a Israyeli (Numeri 14:10)**

### **3. Mu Kachisi:**

Mulungu amaululanso ulemerero wake mu kachisi mu Chipangano Chatsopano:

**Ndipo mzimu unandinyamula numuka nane ku bwalo la m'kati; ndipo taonani, ulemerero wa Mulungu unadzaza kacisi (Ezekieli 43:5)**

**Atatero anamuka nane njira ya cipata ca kumpoto kukhomo kwa kacisi, ndipo ndinapenya, taonani, ulemerero wa Yehova unadzaza nyumba ya Yehova; pamenepo ndinagwa nkhope pansi (Ezekieli 44:4)**

**Kwerani ku dziko la mapiri, ndi kukwera nayo mitengo, nimumange nyumbayi; ndipo kudzandikomera, ndipo ndidzalemekezedwa, ati Yehova (Hagai 1:8)**

**... ndipo ndidzadzaza nyumba iyi ndi ulemerero... (Hagai 2:7)**

### **4. Mu Israyeli**

Israyeli anasankhidwa kuti...

**...Pakuti monga mpango uthina m'cuuno ca munthu, comweco ndinathinita kwa Ine nyumba yonse ya Israyeli ndi nyumba yonse ya Yuda, ati Yehova, kuti akhale kwa Ine anthu, ndi dzina, ndi cilemekezo, ndi ulemerero; koma anakana kumva (Yeremiya 13:11)**

Zinanendwa kuti Mulungu anali “ulemerero wa anthu ake a Israyeli” Luka 2:32. Mulungu anati kwa Israyeli...

**...Iwe ndiwe mtumiki wanga, Israyeli, amene ndidzalemekezedwa nawe (Yesaya 49:3)**

**Yimbani m'mwamba inu, pakuti Yehova wacicita ico; kuwani inu, mbali za pansi pa dziko; yimbani mapiri inu; nkhalango iwe, ndi mitengo yonse m'menemo; cifukwa kuti Yehova wapulumutsa Yakobo, ndipo adzadzilemekezetsa yekha mwa Israyeli (Yesaya 44:23)**

### **5. Mumpingo:**

Mu Chipangano Chatsopano, Mulungu anayamba kuulula ulemerero wake kudzera mwa gulu latsopano lotchedwa mpingo:

**...ndiwo Aisrayeli; ali nao umwana, ndi ulemerero, ndi mapangano, ndi kupatsa kwa malamulo, ndi kutumikira m'kacisi wa Mulungu, ndi malonjezo (Aroma 9:4)**

**Pamenepo ndipo simulinso alendo ndi ogonera, komatu muli a mudzi womwewo wa oyera mtima ndi a banja la Mulungu; omangika pa maziko a atumwi ndi aneneri, pali Kristu Yesu mwini, mwala wa pangondya; mwa iye cimango conse, columikizika pamodzi bwino, cikula, cikhale kacisi wopatulika mwa Ambuye; cimene inunso mumangidwamo pamodzi, mukhale cokhalamo Mulungu mwa Mzimu (Aefeso 2:19-22)**

Mulungu amakhumba mpingo wa ulemerero, umene ndi odzadzidwa ndi ulemerero wake:

**Kuti iye akadziikire yekha Eklesia wa ulemerero, wopanda banga, kapena khwinya, kapena kanthu kotere; komatu kuti akhale woyera, ndi wopanda cirema (Aefeso 5:27)**

## **6. Mwa okhulupirira:**

Mpingo umapangidwa ndi okhulupirira. Kuti ulemerero wa Mulungu uonekere mu mpingo, ukuyenera kuonekera kwa okhulupirira aliyense payekha:

**Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu? (I Akorinto 3:16)**

**Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kacisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha. Pakuti munagulidwa ndi mtengo wace wapatali; cifukwa cace lemekezani Mulungu m'thupi lanu (I Akorinto 6:19-20)**

Khalani kaye chete pang'ono pa phunziro lanu ndi kuwerenga Hagai 2:3-9. Pakuti ndi nyumba yotsiliza (matupi athu ngati kachisi) umene ulemerero wa Mulungu udzaonekera:

**Koma tiri naco cuma ici m'zotengera zadothi, kuti ukulu woposa wamphamvu ukhale wa Mulungu, wosacokera kwa ife (II Akorinto 4:7)**

Ulemerero kapena chuma mu zotengera za dziko, ngati zinali mu zotengera za golidi, anthu adzakopeka ku chotengeracho mmalo mwa zamkatimo:

**Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyerera monga mwa kalirole ulemerero wa Ambuye, tisandulika m'cithunzihunzi comweci kucokera kuulenerero kumka kuulemerero, monga ngati kucokera kwa Ambuye Mzimu (II Akorinto 3:18)**

**Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwacitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wace.**

**Cifukwa kuti iwo amene iye anawadziwiratu, iwowa anawalamuliratu afanizidwe ndi cifaniziro ca Mwana wace, kuti iye akakhale mwana woyamba wa abale ambiri; ndipo amene iye anawalamuliratu, iwo anawaitananso; ndimo iwo amene iye anawaitana, iwowa anawayesanso olungama; ndi iwo amene iye anawayesa olungama, iwowa anawapatsanso olemerero (Aroma 8:28-30)**

### **ULEMERERO EA KHRISTU**

Mwaphunzira kale za mmene ulemerero wa Mulungu unaonekera mwa Yesu, koma kodi mmadziwa kuti mukuyenera kukhala ulemerero wa Khristu? Werengani mavesi awa:

**Taona, iwe udzaitana mtundu umene sunaudziwa, ndi mtundu umene sunakudziwa udzakuthamangira, cifukwa ca Yehova Mulungu wako, ndi cifukwa ca Woyera wa Israyeli; pakuti Iye wakukometsa (Yesaya 55:5)**

**yense wochedwa dzina langa, amene ndinamlenga cifukwa ca ulemerero wanga; ndinamuumba iye; inde, ndinampanga iye (Yesaya 43:7)**

tikuyenera kuyenda mayendedwe oyenera a Mulungu amene anakuitanani ku Ufumu wake ndi ulemerero (I Atesalonika 2:12).

Ife ndi aminthenga a mpingo ndi ulemerero wa Khristu (II Akorinto 8:23). Mulungu anasankhiratu kuti tikhale matamando a ulemerero wake (Aefeso 1:12).

**Iwe udzakhalanso korona wokongola m'dzanja la Yehova, korona wacifumu m'dzanja la Mulungu wako (Yesaya 62:3)**

**ndi kuti iye akadziwitse ulemerero wace waukuru pa zotengera zacifundo, zimene iye anazikonzeratu kuulemerero (Aroma 9:23)**

**Cifukwa cace mulandirane wina ndi mnzace, monganso Kristu anakulandirani inu, kukacitira Mulungu ulemerero (Aroma 15:7)**

Ife taitanidwa ndi Yesu ku ulemerero wake wamuyaya (I Petro 5:10)

**Popeza mphamvu ya umulungu wace idatipatsa ife zonse za pamoyo ndi cipembedzo, mwa cidziwitso ca iye amene adatiitana ife ndi ulemerero ndi ukoma wace wa iye yekha (II Petro 1:3)**

**kumene aoaitanako inu mwa Uthenga Wabwino wathu, kuti mulandire ulemerero wa Ambuye wathu Yesu Kristu (II Atesalonika 2:14)**

tikuyenera kukhala matamando a ulemerero wake (Aefeso 1:12)

Mulungu amafuna ife tidziwe chuma cha ulemerero wake (Akolose 1:27)

### **MPHATSO YA ULEMERERO**

Uwu ndi ulemerero wodabwitsa wa Mulungu umene watisungira ngati mphatso yathu. Yesu anati:

**Ndipo ulemerero umene mwandipatsa Ine ndapatsa Iwo; kuti akhale amodzi, monga Ife tiri mmodzi (Yohane 17:22)**

Pakuti ndi chokhumba cha Mulungu kuti tilandire ulemerero umwewo umene analemekezedwa ndi atate. Pakuti ndi mphatso. Chimene mungachite ndi kungoitantsa basi:

**Pakuti Yehova Mulungu ndiye dzuwa ndi cikopa; Yehova adzapatsa cifundo ndi ulemerero; Sadzakaniza cokoma iwo akuyenda angwiro (Masalmo 84:11)**

Monga mmene musinthikira ndi mau a Mulungu, pemphero ndi zimene mumadutsamo, ndiye kuti muli pa ulendo wolandira ulemerero:

**Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyenera monga mwa kalirole ulemerero wa Ambuye, tisandulika m'cithunzihunzi comweci kucokera kuulenerero kumka kuulemerero, monga ngati kucokera kwa Ambuye Mzimu (II Akorinto 3:18)**

Ulemerero umaonekera kuchokera pa kalilore wa mau a Mulungu wosati wogonjetsedwa. Ulemerero wa Mulungu ukuyenera kukhala mphamvu yokonzekeretsa kwa inu. Amuna akunena lero ngati sananenepo, “Tikanamuona Yesu, amene Mulungu anapereka...

**Dzuwa silidzakhanso kuunika kwako usana, ngakhale mwezi sudzakuunikiranso kuti kuyere; koma Yehova adzakhala kwa iwe kuunika kosatha, ndi Mulungu wako adzakhala ulemerero wako (Yesaya 60:19)**



**Pakuti Mulungu amene anati, Kuunika kudzawala kuturuka mumdima, ndiye amene anawala m'mitima yathu kutipatsa ciwalitsiro ca cidziwitso ca ulemerero wa Mulungu pankhope pa Yesu Kristu (II Akorinto 4:6)**

Kulira kwanu kukhale ngati kwa Mose:

**Ndipo anati, Ndionetsenitu ulemerero wanu (Eksodo 33:18)**

Ndipo kukhale kumene Davide anakufunafuna:

**Kuti ndione mphamvu yanu ndi ulemerero wanu, Monga ndinakuonani m'malo oyera (Masalmo 63:2)**

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

---

2. Perekani tanthauzo la mawu oti “ulemerero.”

---

---

3. Kodi ndi ndani amene ali gwero la ulemerero?

---

4. Lembani chidule cha chikhalidwe cha ulemerero wa Mulungu.

---

---

---

5. Kodi ndi kuti kumene Mulungu amaulula ulemerero wake?

---

---

6. Kodi chiganizochi ndi choona kapena chonama: Mukuyenera kuchita ntchito zabwino kuti mulandire ulemerero kwa Mulungu. Pakuti si mphatso. Chiganizochi ndi \_\_\_\_\_

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Mu phunziroli mwaphunzira za ulemerero wa Mulungu. Baibulo limakamba za ulemerero wina umene “ndi ulemerero wopanda pake.” Ulemerero umenewu ndi...

### **ULEMERERO WA MUNTHU:**

Anthu onse amafuna ulemerero wina wake. Ngati sukhalala ulemerero nwa Mulungu, ndiye kuti ndi ulemerero wopanda pake. Ena amakonda ulemerero wa anthu kwambiri kuposa ulemerero wa Mulungu.

Mateyu 6:2

Chilichonse chimene mulandira kuchokera kwa anthu, matamando awo ndi mphoto yanu. Paulo anakambapo za maonekedwe a ulemererowo koma osati mu mtima mwawo (II Akorinto 5:12). Ulemerero wa munthu sukhalitsa.

I Petro 1:24-25

Musakhumbe ulemerero wa munthu:

### **ULEMERERO WA IWE MWINI:**

Mutha kulakwanso pokhala ndi ulemerero wopanda pake pozilemekeza nokha:

Ulemerero wambiri umakhala wa kuthupi (II Akorinto 12:6). Alipono ena amene azilemekeza mmanyazi awo (Afilipi 3:19). Ndipo chimaliziro chawo ndi chionongeko! Yakobo 3:14 akuti ngati tili ndi ziwawa mu mtima, nkhwizi sitili mu ulemerero komanso sitikhala mu choonadi.

## CHAPUTALA CHA 5

### ZOLINGA ZA ULEMERERO WA MULUNGU

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchoketa pantima.
- Kulemba chidule cha zolinga za ulemerero wa Mulungu.

#### VESI LOTSOGOLERA

**ndipo ulemerero wa Yehova udzabvumbulutsidwa, ndipo anthu onse adzauona pamodzi, pakuti pakamwa pa Yehova panena comweco (Yesaya 40:5)**

#### MAWU OYAMBA

Mu phunziro lathali, mwaphnzira mfundo za ulemerero wa Mulungu, mmene ulili, kumene amaululirako ulemerero ndi kuti munapatsidwa ngati mphatso. Mphatso yodabwitsa ya ulemerero ili ndi cholinga mmoyo wanu chokukonzekeretsani kuti mukwaniritse gawo lanu dongosolo la Mulungu.

#### CHOLINGA CHA ULEMERERO WA MULUNGU

Mobwereza mu malemba Mulungu ananena amavumbulutsa ulemerero ku dziko ndi cholinga kuti amudziwe Iye:

**Anthu ako adzakhalanso onse olungama; dzikolo lidzakhala colowa cao ku nthawi zonse, nthambi yooka Ine, nchito ya manja anga, kuti Ine ndikuzidwe (Yesaya 60:21)**

Koma pali zolinga zina za ulemerero wa Mulungu, zimene zambiri mwa izo zimagwirizana ndi munthu. Ulemerero waperekedwa chifukwa:

#### THANDIZO:

Pamene mwakonzekeretsedwa kuchita ntchito ya Mulungu, mukhala ndi zosowa za kuthupi ndi za ku uzimu, ulemerero wa Mulungu umakupatsani zosowazi.

**Koma Mulungu wanga adzakwaniritse cosowa canu ciri conse monga mwa cuma cace m'ulemerero mwa Kristu Yesu (Afilipi 4:19)**

Mulungu amakwaniritsanso zosowa zanu za ku uzimu:

**kuti monga mwa cuma ca ulemerero wace akulimbikitseni inu ndi mphamvu mwa Mzimu wace, m'kati mwanu (Aefeso 3:16)**

**MPHAMVU:**

Ulemerero wa Mulungu umakupatsani mphamvu yotumikira:

**olimbikitsidwa m'cilimbiko conse, monga mwa mphamvu ya ulemerero wace, kucitira cipiriro conse ndi kuleza mtima conse pamodzi ndi cimwemwe (Akolose 1:11)**

**CHIMWEMWE:**

Ulemerero wa Mulungu umakupatsani chimwemwe pamene mukutumikira:

**Okonedwa ace atumphe mokondwera m'ulemu: Apfuule mokondwera pamakama pao (Masalmo 149:5)**

**UFULU:**

Ulemerero wa Mulungu umakhala ndi udindo okumasulani ku ukapolo mkukhala mfulu. Ndi ulemerero wake umene udzachita chimodzimidzi kwa iwo amene mukuwatumikira.

**ndi ciyembekezo kuti colengedwa comwe cidzamasulidwa ku ukapolo wa cibvundi, ndi kolowa ufulu wa ulemerero wa ana a Mulungu (Aroma 8:21)**

**MPUMULO:**

Pamene mukugwira ntchito mumatopa, mulungu amakupatsani mpumulo wa ulemerero.

**Ndipo padzakhala tsiku lomwelo, kuti muzu wa Jese umene uima ngati mbendera ya mitundu ya anthu, amitundu adzafunafuna uwu; ndipo popuma pace padzakhala ulemerero (Yesaya 11:10)**

**CHIYERETSO:**

Ulemerero wa Mulungu umakuyeretsani kuti muthe kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu.

Ndipo pamenepo ndidzacomana ndi ana a Israyeli; ndipo cihema cidzapatulidwa ndi ulemerero wanga (Eksodo 29:43)

**UMODZI:**

Ulemerero wa Mulungu umabweretsa umodzi, umene ndi wofunika ku mpingo pamene ukukonzekeretsedwa ku ntchito yotumidwa:

**Ndipo ulemerero umene mwandipatsa Ine ndapatsa Iwo; kuti akhale amodzi, monga Ife tiri mmodzi (Yohane 17:22)**

### **CHITSOGOZO:**

Mulungu amakutsogolerani ndi ulemerero wake:

**amene anayendetsa mkono wace waulemerero pa dzanja lamanja la Mose? amene anagawanitsa madzi pamaso pao, kuti adzitengere mbiri yosatha (Yesaya 63:12)**

### **NZERU:**

Mumafunikira nzeru kuti muchite bwino pa utumiki. Nzeruzi zimachokera ku ulemerero wa Mulungu.

**kuti Mulungu wa Ambuye wathu Yesu Kristu, Atate wa ulemerero, akupatseni inu mzimu wa nzeru, ndi wa bvumbulutso kuti mukamzindikire iye; ndiko kunena kuti maso amitima yanu awalitsike, ktiti mukadziwe inu ciyembekezo ca kuitana kwace nciani; cianinso cuma ca ulemerero wacolowa cace mwa oyera mtima (Aefeso 1:17-18)**

### **CHIBVUMBULUTSO:**

Mzimu Woyera umalemekeza Mulungu pamene akuvumbulutsa zinthu za Mulungu kwa inu:

**Iyeyo adzalemekeza Ine; cifukwa adzatenga za mwa Ine, nadzalalikira kwa inu. 15Zinthu ziri zonse Atate ali nazo ndi zanga; cifukwa cace ndinati, kuti atenga za mwa Ine, nadzalalikira kwa inu (Yohane 16:14)**

### **KULEMEKEZA MAU AKE:**

Chibvumbulutso nthawi zonse chimalemekeza mau a Mulungu. Pamene chinavumbuluka chipulumutso chinapita kwa a mitundu...

**Ndipo pomwepo mngelo wa Ambuye anamkantha, cifukwa sanampatsa Mulungu ulemerero; ndipo anadyedwa ndi mphutsi, natsirizika (Machitidwe 12:23).**

### **CHIUKITSO:**

Mudzaukitsidwa kwa akufa ndi ulemerero wa Ambuye. Mulungu ali pa ntchito yosintha matupi anu kukhala a ulemerero (Afilipi 3:21). Pamene Yesu adzaonekera, mudzafanana naye mu ulemerero.

### **NKHONDO:**

Mdani amafuna kuba ulemerero wanu. Chifukwa chimene amafunira kuba ulemerero ndi chakuti popeza ndiwo ofunika pa ntchito ya Mulungu. Amadziwanso kuti ulemerero wa Mulungu ndi chida champhamvu pa nkondo ya uzimu.

**Pakuti atero Yehova wa makamu: Utatha ulemererowo ananditumiza kwa amitundu amene anakufunkhani; pakuti iye wokhudza inu, akhudza mwana wa m'diso lace (Zakariya 2:8)**

Ulemerero wa Mulungu ndi gawo limodzi la chida chanu cha nkondo, ndipo pamakhala kulumikizana kwa ulemerero pa nkondo ya uzimu. Ulemerero ndi chozitetzerapo chanu, pamene mwamasulidwa mumapereka ulemerero.

**ndipo ulemerero wa Yehova udzabvumbulutsidwa, ndipo anthu onse adzauona pamodzi, pakuti pakamwa pa Yehova panena comweco (Yesaya 40:5)**

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Lembani mwachidule zimene mwaphunzira zokhudza cholinga cha ulemerero wa Mulungu.

---

---

---

---

---

---

(Mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)



## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Chibvumbulutso cha ulemerero wa Mulungu sichimadalira pa kuyenera kwa munthu. Werengani za anthu awa amene Mulungu anawaululira ulemerero wake:

### **Abrahamu: Munthu amene ananena bodza.**

Chibvumbulutso cha ulemerero chinamupangitsa kusiya zonse za lamulo la Mulungu. Genesis 12:1-4. Baibulo limanena kuti “anali wamphamvu mu chikhulupiriro” (Roma 4:20)

### **Mose.Mbusa wosatha kulankhula**

Anatsogolera mtundu kuchoka mu ukapolo chifukwa cha bvumbulutso la ulemerero. (Eksodo 34:29)

### **Yakobo: Wonamiza**

...Komabe Mulungu anabvumbulutsa ulemerero wake mu masomphanya ndi kumpanga yakobo kukhala wamkulu (Genesis 28:10-15)

### **Yesaya: Wachichepere wa milomo yodetsedwa.**

Masomphenya a Yesaya a ulemerero wa Mulungu anabweretsa utumiki wa ulemerero. Yesaya 6.

### **Paulo (Sauli). Yemwe anazunza ndi kupha a khristu.**

Chibvumbulutso cha ulemerero wa Mulungu chinasintha moyo wake. Machitidwe 9.

Mulungu alibe sankhu. Ngati anaulula ulemerero kwa anthu owoneka osayenera, akhoza kuonetsera ulemerero kwa INU.

**Kwa iwo amene afunafuna ulemerero ndi ulemu ndi cisaonongeko, mwa kupirira pa nchito zabwino, adzabwezera moyo wosatha; koma ulemerero ndi ulemu ndi mtendere kwa munthu ali yense wakucita zabwino, kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene; 11pakuti Mulungu alibe tsankhu (Roma 2:7,10-11)**

## CHAPUTALA CHA 6

### MMENE MUNGAMPATSIRE MULUNGU ULEMERERO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pantima.
- Kulongosola mmene mungampatsire Mulungu ulemu.
- Kukambirana pa kupitilira kwa kupereka ndi kulandira ulemerero.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Yesu ananena naye, Kodi sindinati kwa iwe, kuti, ngati ukhulupira, udzaona ulemerero wa Mulungu? (Yohane 11:40)**

#### MAWU OYAMBA

Mu machaputala awiri mwaphunzira za ulemerero wa Mulungu ndi cholinga chake. Mwaphunziranso kuti munalengedwa ndi cholinga choti mumulemekeze Iye ndi kuti ulemerero wake uwonekere mwa inu ndi utumiki wanu.

Ngati mukufuna kukumana ndi ulemerero wa mulungu ndi kutsogolera ena kukumana nawo, ndiye kuti mukuyenera kudziwa kumulemekeza Iye. Pamene mukumulemekeza Iye amavumbulutsa zambiri kwa inu. Mose anakumana ndi ulemerero wa Mulungu ndipo anatsogolera ena kuonanso ulemererowo.

**Ndipo Mose anati, Ici ndi cimene Yehova anakuuzani kuti mucicite; ndipo ulemerero wa Yehova udzaonekera kwa inu...**

**Ndipo Mose ndi Aroni analowa ku cihema cokomanako, naturuka, nadalitsa anthu; ndipo ulemero wa Yehova unaonekera kwa anthu onse. (Levitiko 9:6,23)**

Mose anatsogolera ena kuti awone ulemerero wa Mulungu monga mmenenso mukuchitira. Phunziroli likuonetsera mfundo za Mbaibulo zimene zimalongosola za mmene tingamulemekezere Mulungu.

#### MMENE TINGAMULEMEKEZERE MULUNGU

Molingana ndi Mau a Mulungu, mungamulemekeze Mulungu munjira izi:

#### MWACHIKHULUPIRIRO:

Ulemerero wa Mulungu umaonekera pamene mwakonzekeretsedwa kukhulupirira ndi kuchita mwachikhulupiriro:

**Yesu ananena naye, Kodi sindinati kwa iwe, kuti, ngati ukhulupira, udzaona ulemerero wa Mulungu? (Yohane 11:40)**

Malemba amafotokoza za Abrahamu:

**ndipo poyang'anira lonjezo la Mulungu sanagwedezeka cifukwa ca kusakhulupirira, koma analimbika m'cikhulupiriro, napatsa Mulungu ulemu (Aroma 4:20)**

### **MWACHIOMBOLO**

Mulungu amalemekezedwa pa chiombolo chanu cha machimo. Kulemekeza kokha kumatchedwa chipulumutso ndi kulungamitsa:

**ndipo amene iye anawalamuliratu, iwo anawaitananso; ndimo iwo amene iye anawaitana, iwowa anawayesanso olungama; ndi iwo amene iye anawayesa olungama, iwowa anawapatsanso olemerero. (Aroma 8:30)**

### **POLAPA MACHIMO:**

Mulungu amalemekezedwa pamene mukulapa machimo anu pakutembenuka mtima kuchoka ku machimo ndi kulapa kwanu kopitilira pamene mupezeka kuti mwachimwa:

**Ndipo Yoswa anati kwa Akani, Mwana wanga, ucitiretu ulemu Yehova Mulungu wa Israyeli, numlemekeze iye; nundiuze tsopano, wacitanji? Usandibisire (Yoswa 7:19)**

Kulapa kumakhudza kudziyeretsa nokha ku maganizo ndi ntchito zoipa. Zimenezi zimapereka ulemerero kwa Mulungu.

**Kuti lye akadziikire yekha Eklesia wa ulemerero, wopanda banga, kapena khwinya, kapena kanthu kotere; komatu kuti akhale woyera, ndi wopanda cirema (Aefeso 5:27)**

### **POVOMEREZA:**

Mulungu amalemekezedwa pamene mukuvomereza kuti Yesu ndi Ambuye:

**ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali Ambuye, kucitira ulemu Mulungu Atate (Afilipi 2:11)**

### **PODZICHEPETA NOKHA:**

Mulungu amalemekezedwa pamene mukudzichepetsa nokha:

**Ndipo Mose ndi Aroni anacoka pamaso pa msonkhano kumka ku khomo la cihema cokomanako, nagwa nkhope zao pansu; ndipo ulemerero wa Yehova unaonekera iwo (Numeri 20:6)**

Kudzichepetsa nokha ndi kusala kudya ndi kupemphera. Yesaya 58:8. Pamene mukudzichepetsa ndi kupemphera, Mulungu amayankha, mapemphero anu ndipo izi zimalemekedza Mulungu.

#### **POKHALA MKUPEZEKA KWAKE:**

Mumapereka ulemu kwa Mulungu pamene mukhala mkupezeka kwake. Mumakhala mkupezeka kwake kwa Mulungu polora Yesu kukhala mwa inu.

**cifukwa ali anu: ndipo zanga zonse ziri zanu, ndi zanu ziri zanga; ndipo ndilemekezedwa mwa iwo (Yohane 17:10)**

Mumakhala mkupezeka kwake polora Mulungu kugwora ntchito mwa inu.

#### **MUMSAUTSO:**

Pamene mukumana ndi mavuto, mayesero, ndi zowawa mmoyo, Mulungu amalemekezedwa pamene muchita moyenera ku zowawazi:

**ndipo ngati ana, pomweponso olova nyumba; inde olova nyumba ace a Mulungu, ndi olova anzace a Kristu; ngatitu ife timva zowawa pamodzi naye, kuti tikalaodirensa ulemerero pamodzi ndi iye. Pakuti ndiyesa kuti masauko a nyengo yatsopano sayenera kulinganizidwa ndi ulemerero umene udzaonetsedwa kwa ife (Aroma 8:17-18)**

Paulo ananena kuti:

**Ndipo si coteri cokha, komanso tikondwera m'zisautso; podziwa ife kuti cisautso cicita cipiriro; ndi cipiriro cicita cizolowezi; ndi cizolowezi cicita ciyembekezo: 5ndipo ciyembekezo sicicititsa manyazi; cifukwa cikondi ca Mulungu cinatsanulidwa m'mitima mwathu mwa Mzimu Woyera, amene wapatsidwa kwa ife. Pakuti pamene tinali cikhalire ofok a, pa nyengo yace Kristu anawafera osapembedza (Aroma 5:3-6)**

I Petro 5:1 ndi 4 amakamba za kulawa nawo zowawa zake, pamene mukhala ndi ulemerero wake. Ngakhale matenda angathe kuonetsera ulemerero wa Mulungu pamene machiritso abwera:

**Koma Yesu pamene anamva, anati, Kudwala kumene sikuli kwa imfa, koma cifukwa ca ulemerero wa Mulungu, kuti Mwana wa Mulungu alemekezedwe nako (Yohane 11:4)**

Mawalitsidwe a Yesu anachitika chifukwa cha zowawa zimene anakumana nawo. Kuona ulemerero wake kumawalitsa mayesero!

### **POKWANIRITSA UTUMIKI WANU:**

Mulungu amalemekezedwa pamene mukukwaniritsa utumiki umene munaitanidwako:

**akalankhula wina, alankhule ngati manenedwe a Mulungu; wina akatumikira, acite ngati mu mphamvu imene Mulungu ampatsa, kuti m'zonse Mulungu alemekezedwe mwa Yesu Kristu, amene ali nao ulemerero ndi mphamvu ku nthawi za nthawi. Amen (I Petro 4:11)**

Utumiki wanu umakhudzanso ntchito zabwino ndipo Mulungu amalemekezedwa pamene muchita ntchito zabwinozi:

**Comweco muwalitse inu kuunika kwanu pamaso pa anthu, kuti pakuona nchito zanu zabwino, alemekeze Atate wanu wa Kumwamba (Mateyu 5:16)**

Ntchito zabwino zimakhudzanso makhalidwe ndi zolankhula zanu. II Petro 2:12, amanena kuti Mulungu adzalemekezedwa ngati makhalidwe komanso zokamba zanu ndi zoyera. Ntchito za Mulungu ndi kubala chipatso cha uzimu. Izinso zimabweretsa ulemerero kwa Mulungu.

**Mwa ici alemekezedwa Atate wanga, kuti mubale cipatso cambiri; ndipo mudzakhala akuphunzira anga (Yohane 15:8)**

Ntchito zabwino za Mulungu ndiko kufalitsa uthenga wabwino umene umaulula ulemerero ku dziko lapansi:

**Nyamuka, wala, pakuti kuunika kwake kwafika, ndi ulemerero wa Yehova wakuturukira. Pakuti taona, mdima udzaphimba dziko lapansi, ndi mdima wa bii mitundu ya anthu; koma Yehova adzakuturukira, ndi ulemerero wace udzaoneka pa iwe (Yesaya 60:1-2)**

Pamene mukutumikira Mulungu amaonetsa ntchito zake ndipo anthu amamulemekeza Iye: Machitidwe 4:21.

Lemekezani Mulungu pomalizitsa ntchito imene munaitanidwirako:

**Ine ndalemekeza Inu pa dziko lapansi, m'mene ndinatsiriza nchito imene munandipatsa ndicite (Yohane 17:4)**

Mukhodza kumulemekeza Mulungu pa zonse zimene mumachita:

**akalankhula wina, alankhule ngati manenedwe a Mulungu; wina akatumikira, acite ngati mu mphamvu imene Mulungu ampatsa, kuti m'zonse Mulungu alemekezedwe**

**mwa Yesu Kristu, amene ali nao ulemerero ndi mphamvu ku nthawi za nthawi.  
Amen (I Petro 4:11)**

Kuchuluka ndi mtundu wa ntchito umene mumachita kaya ndi zonyezeka koma zimakhala zamphamvu pamene zachitika popeleka ulemerero kwa Mulungu.

### **POKHALA MMAU AKE:**

Ulemerero wa Mulungu umaonekera Mmau ake:

**Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyera monga mwa kalirole ulemerero wa Ambuye, tisandulika m'cithunzihunzi comweci kucokera kuulenero kumka kuulemerero, monga ngati kucokera kwa Ambuye Mzimu (II Akorinto 3:18)**

Pamene Mose anaswa malamulo a Mulungu amene analembedwa pa miyala, ulemerero unachoka pa nkhope yake. Mulungu amapereka ulemerero kwa anthu amene amalandira ndi kusunga Mau ake. Sitingakambe za ulemerero wa Mulungu popandapo Mau Ake, chifukwa Yesu ndiye Mau.

### **KUDZERA MMATAMANDO NDI MALAMBIRO:**

Munthu, amene ndi wokhudzidwa ndi ulemerero wa Mulungu, amabwenzanso ulemerero ndi matamando kwa Iye:

**Wopereka nsembe yacyyamiko andilemekeza Ine (Masalmo 50:23)**

Zoona zake zenizeni za kulambira mu Chipangano Chatsopano zimachika pamene zolengedwa zikumulemekedza Mulungu. Ulemerero ukuyenera

1. **Kupita kwa Mulungu:** I Samueli 6:5, I Mbiri 16:29
2. **Kuperekedwa kwa Mulungu:** Masalmo 29:1, Mateyu 16:13
3. **Kupatsidwa kwa Mulungu:** Malaki 2:2
4. **Kutheketsa ndi ulemerero wake mwa ife:** Masalmo 57:8, 108:1, 30:12
5. **Kuchitika mu umodzi:** Aroma 15:6

Kulemekeza Mulungu sikumachitika popandapo kanthu. Mukuyenera kupereka ulemerero kwa Mulungu chifukwa...

1. Ndi lamulo:

**Mcitireni Yehova ulemerero wa dzina lace; Bwerani naco copereka, ndipo fikani pamaso pace; Lambirani Yehova m'ciyero cokometsetsa (I Mbiri 16:29)**

**2. Ndi woyenera kwa Iye:**

**Perekani kwa Yehova ulemerero wa dzina lace: Gwadirani Yehova moyera ndi mokometsetsa (Masalmo 29:2)**

**3. Chifukwa cha chikhalidwe chake:**

**Ndani adzakhala wosaopa ndi wosalemekeza dzina lanu Ambuye? Cifukwa Inu nokha muli woyera; cifukwa mitundu yonse idzadza nidzalambira pamaso panu, popeza zolungama zanu zidaonetsedwa (Chibvumbulutso 15:4)**

**4. Chifukwa cha dzina lake:**

**Ndidzakuyamikani, Ambuye, Mulungu wanga, ndi mtima wanga wonse; Ndipo ndidzalemekeza dzina lanu nthawi zonse (Masalmo 86:12)**

**5. Analenga zinthu zonse:**

**Muyenera inu, Ambuye wathu, ndi Mulungu wathu, kulandira ulemerero ndi ulemu ndi mphamvu; cifukwa mudalenga zonse, ndipo mwa cifuniro canu zinakhala, nizinalengedwa (Chibvumbulutso 4:11)**

**6. Amateteza zinthu zonse:**

**Cifukwa zinthu zonse zicokera kwa iye, zicitika mwa iye, ndi kufikira kwa iye. 8 K wa Iyeyo ukhale ulemerero ku nthawi zonse. Amen (Aroma 11:36)**

**7. Chifukwa cha chiombolo:**

**ndipo amene iye anawalamuliratu, iwo anawaitananso; ndimo iwo amene iye anawaitana, iwowa anawayesanso olungama; ndi iwo amene iye anawayesa olungama, iwowa anawapatsanso olemerero (Aroma 8:30)**

**8. Chifukwa cha chiweruzo:**

**ndi kunena ndi mau akuru, Opani Mulungu, mpatseni ulemerero; pakuti yafika nthawi ya ciweruziro cace; ndipo mlambireni iye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi nyanja ndi akasupe amadzi (Chibvumbulutso 14:7)**

**9. Chifukwa cha cholowa chathu mwa Iye:**

**Kuti ndione cokomaco ca osankhika anu, Kuti ndikondwere naco cikondwerero ca anthu anu, Kuti ndidzitamandire pamodzi ndi colowa canu (Masalmo 106:5)**

Muphunzira zambiri za mmene mungamupatsire Mulungu ulemerero mu chaputala cha 8 ndi 9 zimene zimakamba za mutu wokhudza kulambira.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Longosolani za mmene mungampatsire Mulungu ulemerero.

---

---

---

---

---

3. Fotokozani kupitilira kopereka ndi kulandira ulemerero.

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)



## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani Yesaya chaputala cha 60. Mavesi asanu oyamba amatitsimikizira:

**Nyamuka, wala, pakuti kuunika kwake kwafika, ndi ulemerero wa Yehova wakuturukira (Yesaya 60:1)**

2. Werengani Yesaya 43. Onetsetsani Vesi ya 7.
3. Werengani Masalmo 24. Chaputalachi chimakamba za mmene mfumu ya ulemerero ikubwera. Ikubwera kwa iwo amene ndi: ojera mmanja, ojera mitima ndi opanda chinyengo.
4. Onani zimene zimachitika pamene simumupatsa Mulungu ulemu:

**Mukapanda kumvera, mukapanda kuliika mumtima mwanu, kupatsa dzina langa ulemerero, ati Yehova wa makamu, ndidzakutumizirani temberero, ndi kutemberera madalitso anu; inde, ndawatemberera kale cifukwa simuliika mumtima (Malaki 2:2)**

## CHAPUTALA CHA 7

### LIKASA LIKUBWERA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.
- Kulongosola chifukwa chiyanin ulemerero umawachokera anthu.
- Lembani chidule cha zocchitika ndi kufunika kwa ku uzimu pamene likasa linapita ku: -Ebeneza, Afeki, Ashidoki, Gati, Ekroni, Betisemesi, Kiriya-Yerimu ndi ku Yerusalemu.
- Kudziwa zinthu zinayi zofunika pobweretsa likasa la Mulungu.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Momwemo Aisrayeli onse anakwera nalo likasa la cipangano la Yehova ndi kupfuula, ndi kumveka kwa lipenga, ndi mphalasa, ndi nsanje zomveketsa, ndi zisakasa, ndi azeze (I Mbiri 15:28)**

### MAWU OYAMBA

Mulungu anamuza Mose, kuti ngati upanga chihema molingana ndi mndandanda, ulemerero wanga udzakhalamo (Eksodo 25:9). Munthu analengedwa mwa ulemerero wa Mulungu. Tinalengedwa mu chifanizo chake ndi kuikidwa mu ntchito ya manja ake kuti tipereke ulemerero kwa Iye (Ahebri 2:7). Pamene munthu anachimwa, dongosolo lina sintha ndipo ulemerero unachoka:

**pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu (Aroma 3:23)**

Monga chihema cha mose, inunso ndinu chihema cha mulungu. Ngati mumanga moyo wanu wa uzimu molingana ndi dongosolo la ulemerero umene udakhala pamenepo. Koma mukasintha dongosolo ulemerero udzachoka.

**cifukwa kuti, ngakhale anadziwa Mulungu, sanamcitira ulemu wakuyenera Mulungu, ndipo sanamyamika; koma anakhala opanda pace m'maganizo ao, ndipo unada mtima wao wopulukira, Pakunena kuti ali anzeru, anapusa; nasandutsa ulemerero wa Mulungu wosaonongeka, naufanizitsa ndi cifaniziro ca munthu woonongeka ndi ca mbalame, ndi ca nyama zoyendayenda, ndi ca zokwawa (Aroma 1:21-23)**

Kudzera mu chiweruzo cha Mulungu, ena adzalapa ndipo ulemerero udzabwenzeretsedwa:

**Ndipo panthawipo panali cibvomezi cacikuru, ndipo limodzi la magawo khumi a mudzi lidagwa; ndipo anaphedwa m'cibvomezico anthu zikwi zisanu ndi ziwiri; ndipo otsalawo anakhala amantha, napatsa ulemerero kwa Mulungu wa m'Mwamba (Chibvumbulutso 11:13)**

Ena sadzalapa ndi kutenganso ulemerero:

**Ndipo anatenthedwa anthu ndi kutentha kwakukuru; ndipo anacitira mwano dzina la Mulungu wokhala nao ulamuliro pa miliri iyi; ndipo sanalapa kuti amcitire ulemu (Chibvumbulutso 16:9)**

Wochimwa alibe ulemerero, umabwenzeretsedwa kudzera mu njira ya chiombolo:

**Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwacitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wace. Cifukwa kuti iwo amene iye anawadziwiratu, iwowa anawalamuliratu afanizidwe ndi cifaniziro ca Mwana wace, kuti 4 iye akakhale mwana woyamba wa abale ambiri; ndipo amene iye anawalamuliratu, iwo anawaitananso; ndimo iwo amene iye anawaitana, iwowa anawayesanso olungama; ndi iwo amene iye anawayesa olungama, iwowa anawapatsanso olemerero (Aroma 8:28-30)**

Ulemerero umachokanso kwa anthu a Mulungu pamene tchimo lawalekanitsa pamaso pa Mulungu. Kodi chingachitike ndi chiyani pamene ulemerero wa Mulungu wachoka chifukwa cha tchimo limene limasinthu zinthu? Chipangano Chakale cha kutengedwa ndi kubwerera kwa likasa la Mulungu kwa Israyeli zimaonetsa kugwirizana kwa choonadi cha uzimu chimene chimayankha mafunso.

### **KUTENGEDWA NDI KUBWERERA KWA LIKASA**

Likasa la Mulungu linali chizindikiro cha ulemerero wa Mulungu pakati pa anthu ake. Likasa linatsogolera Israyeli mu ulendo wa mchipululu. Linatsogolera njira imene anaoloka Mtsinje wa Yorodani kupita ku Kanani. Linawatsogolera ku nkondo ngati chizindikiro cha kupezeka kwa Mulungu.

Mu I Samueli chaputala cha 4 mpaka 7, pali nkhani yomvetsa chisoni ya mmene likasa ngati chizindikiro cha Mulungu pa anthu mmene linasowera. Werengani machaputalawa mu Baibulo lanu musanayambe kupitiliza ndi phunziroli.

**KUCHOKA KU SHILO KUPITA KU EBENEZA:**

I Samueli 4 amayamba ndi mtundu wa Israyeli ukulimbana ndi Afilisiti. Israyeli yemwe anali pa malo otchedwa Ebeneza ndipo asirikali a Afilisiti pa Afeki. Israyeli anakanthidwa ku nkondo chifukwa cha tchimo limene linali pakati pawo, makamaka utsogoleri wawo (Onani I Samueli 3). Pamene anaphetsa asirikali 4,000, anayamba kufunsa “Chifukwa chiyani Ambuye watikantha?”

Mmalo mufunafuna nkhope ya Ambuye mmitima mwawo kuti awauze za vuto lenileni, asirikali a Israyeli anaganiza zokatenga Likasa, chizindikiro cha kupezeka kwa Mulungu, ndikukhala nalo pa nkondo. Mu nkondo yomwe inangotha, pa chilamulo cha Mulungu, Likasa linasogolera Israyeli ku nkondo, koma chinali ngati chizindikiro cha kupezeka kwa Mulungu. Chifukwa cha tchimo, kupezeka kwa Mulungu sikunali kwa iwo pa nkondo, choncho chizindikiro cha kupezeka kwake kunali kopanda tanthauzo.

Atatha kuchita nkondo koyamba ku Kanani, chihema chinaikidwa pa malo otchedwa Shilo. A Israyeli anapita ku Shilo kukatenga Likasa mkupitisa ku Ebeneza. Pamene likasa linapita kumaloko, Israyeli anachita mfuu chifukwa anatsimikizika kuti nkondo apambana ndi Afilisiti.

Komatu chizindikiro popanda kuozeke kwenikweni kwa Mulungu kunali kopanda tanthauzo. Pamene nkondo inayambanso, asilikali a Israyeli okwana 30,000 anaphedwa ndi Afilisiti ndipo analanda Likasa la Mulungu. Ndipo ana a Eli wa nsemba anaphedwa.

Pamene nthumwi ianafika Eli wansembe ndi uthenga, ananjenjemera ndikugwa pamene anakhala nathyoka khosi mkufa. Mpongozi wake anabereka mwamsanga mwana, amene anamutcha “Ikabodi” kutanthauza kuti “ulemerero wa Mulungu unachotsedwa.”

**Ndipo iye anati, Ulemerero wacoka kwa Israyeli; cifukwa likasa la Mulungu lalandidwa (I Sameuli 4:22).**

Chizindikiro cha kupezeka kwa Mulungu, kunali mmanja mwa adani ndipo Israyeli anagonjetsedwa ku nkondo. Pamene tilibe kupezeka kwa Mulungu, timagonjetsedwa ku nkondo.

Mmalo ambiri lero, mpingo wathutira ndi zizindikiro za kupezeka kwa Mulungu. Tili ndi zizindikiro za mitanda, nkunda, mgonero, makandulo ndi mamangidwe a mipingo. Tikhoza kumakondwera ndi kutamanda Mulungu, monganso mmene Israyeli anachitira pamene Likasa linafika pamalo awo.

Koma kupezeka kwake kwa Mulungu kulidi ndi ife, kapena takhutira ndi zizindikiro ndi miyambo? Pamene takhutira ndi zizindikiro, miyambo ndi zina, kupezeka kwa Mulungu kumachoka. Ulemerero wa Mulungu umapita kwa adani. Kodi mwakhazikika pa zizindikiro osati pa kupezeka kwa Mulungu kwenikweni?

Werengani I Samueli chaputala cha 4, 5 ndi kuona mmene Likasa linayendera.

### **KUBWERERA KWA LIKASA**

Werengani za chipambano cha Davide pobwerera ndi Likasa mu I Mbiri 13:17. Zinthu zinayi zinali zofunika pobwerera kwa Likasa la ulemerero wa Mulungu kwa anthu ake. Zinthu zimenezi ndi zofunikianso ngati tikufuna ulemerero wa Mulungu ubwerere kwa ife lero:

#### **1. CHOKHUMBA:**

Kwa zaka zokwana 20, mtundu wa Israyeli unakhumbitsa ubale wabwino ndi Mulungu. Anali ndi khumbo la mbiriyi. Chinthu choyamba chimene anachita ndiko kukhumba ulemerero wa Mulungu. Komatu khumbo lokha silokwanira. Mukhoza kufuna chinthu kwambiri, koma kuti mukhale nacho, mumuyenera kukhala nachonso...

#### **2. KUTSIMIKIZIKA:**

Davide anatsimikizika kukatenganso Likasa. Ananena kuti, “Tiyeni tikazitengere likasa la Mulungu” (I Mbiri 13:3). Simukuyenera kukhumba kokha ulemerero wa Mulungu, koma mukuyenera kutsimikizika mu mtima mwanu kuti simusiya koma mulandira. Ngakhale kulephera sikunamulepheretse Davide. Pamene samachita bwino koyamba, anayeseranso kachiwiri!

#### **3. CHITSOGOZO:**

Davide ndi anthu ake anayamba ulendo wopita kumene kunali Likasa kuti akalitenge. Khumbo silokwanira. Ngakhale kutsimikizika sikukwanira. Mukuyenera kuyamba kuyenda mu njira ya kupezeka kwa Mulungu ngati mukufuna kuti ulemerero ubwerere. Simungakhale ndi ulemerero ngati mwatenga njira ina ya kudziko lapansi. Simungakhale ndi ulemerero ngati muthawa Mulungu pa kusamvera maitanidwe ake moyo wanu. Mukuyenera kupita njira ya Mulungu ngati mukufuna ulemerero.

#### **4. DONGOSOLO LOYENERA:**

Pofuna kubweretsa Likasa, ng’ombe zinapunthwa ndipo ngolo inali pafupi kugwa. Ulemerero sukanabwerera pa ngolo yopangidwa ndi munthu. Limayenera kubwerera molingana ndi dongosolo loyenera. Tayesetsa kubweretsa ulemerero wa Mulungu pakati pathu kudzera mu zinthu zopanga tokha. Tili ndi madongosolo athu ndi miyambo ndipo timalimbikitsa umodzi wa abale.

Kupitilira apo, mayina a anthu awiri amphamvu amene ananyamula Likasa (Uza) ndi (Ahiyo). Ngolo zathu zimatha kuoneka bwino komatu ndi mphamvu za anthu. Zotsatira zake za zinthu zopangidwa ndi anthu ndi kukhumudwa, kulephera ngakhale imfa imene. Sitingakwanitse ndi malinganliro athu, njira zathu kapena mphamvu zathu kubweretsa

mphamvu ku Zione... Zikuyenera kuchokera kwa Mulungu kudzera mu Mau ake. Davide kumapeto kwake anavomereza:

**Pakuti, cifukwa ca kusalinyamula inu poyamba paja, Yehova Mulungu wathu anacita cotipasula, popeza sitinamfunafuma Iye monga mwa ciweruzo (I Mbiru 15:13)**

Pamene dongosolo loyenera la Mulungu latsatidwa, ulemerero umabwerera.

### **MOTO, ULEMERERO NDI KULAMBIRA**

Moto ndi ulemerero ndi zofunika pokonzekeretsa mphamvu za ku uzimu. Popanda moto, ulemerero umatha. Popanda moto ndi ulemerero, timakhala opanda mphamvu mmaso mwa adani.

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

---

2. Longosolani chifukwa chiyani ulemerero umachoka pakati pa anthu a Mulungu.

---

---

---

3. Lembani chidule cha zochitika ndi kufunika kwa ku uzimu pamene Likasa linali ku madera awa:

Ebeneza

---

---

Afeki

---

---

Ashidodi

---

---

Gati

---

---

Ekironi

---

---

Betisemeti

---

---

Kiriya-Yerimu

---

---

Yerusalemu

---

---

4. Kodi ndi zinthu ziti zinayi zofunikira pobweretsa Likasa la ulemerero wa Mulungu?

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)



## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Gwiritsani ntchito mapu a Palesitina mu nthawi ya Chipangano Chatsopano kupeza mmene Likasa linayendera:

Ebeneza: Miyambo  
Afeki: Kugwirira  
Asidoki: Kupereka maganizo  
Gati: Kuyankhapo  
Ekironi: Kuyankhapo  
Betisemeti: Kukana  
Kiriya-yerimu: Kukana  
Yerusalemu (Zione): Kubwenzeretsa

2. Kodi malowa angapereke tanthauzo kwa munthu? Kapene athanso kugwiritsidwa ntchito ku gulu monga mpingo?

## CHAPUTALA CHA 8

### KUBWENZERETSA CHIHEMA CHA DAVIDE

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kulongosola tanthauzo la “kubwenzeretsa chihema cha Davide.”
- Kulemba mavesi amene amakamba za uneneri wobwenzeretsa.
- Longosolani za nthawi imene chidzabwenzeretsedwe.
- Longosolani za mmene ungapzabwenzeretsedwe.
- Lembani chidule cha mmene chihema cha Davide chimafananira kwa inu.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Zikatha izo ndidzabwera, Ndidzamanganso chihema ca Davide, cimene cinagwa; Ndidzamanganso zopasuka zace, Ndipo ndidzaciimikanso (Machitidwe 15:16)**

#### MAWU OYAMBA

Nkhani yobwenzeretsa Likasa ndi yofunika kwambiri, chifukwa ikugwirizana ndi mpingo watsopano ndi malonjezo a Mulungu amene amati...

**Zikatha izo ndidzabwera, Ndidzamanganso chihema ca Davide, cimene cinagwa; Ndidzamanganso zopasuka zace, Ndipo ndidzaciimikanso (Machitidwe 15:16)**

Tisapitilize ndi phunziroli, werengani I Mbiri chaputala 13-17.

#### LONJEZO LA KUBWENZERETSA

Werengani mavesiwa. Mulungu anati...

**Tsiku lomwelo ndidzautsa msasa wa Davide udagwawo, ndi kukonzanso zopasuka zace; ndipo ndidzautsa zogumuka zace, ndi kumanga monga masiku a kalelo; kuti alandire otsala a Edomu akhale colowa cao, ndi amitundu onse akuchedwa dzina langa, ati Yehova wakucita izi. Taonani akudza masiku, ati Yehova, akud wolima adzapezana ndi wodula, ndi woconda mphesa adzapezana ndi wofesa, ndi mapiri adzakhetsa vinyo watsopano, ndi zitunda zonse zidzasungunuka (Amosi 9:11-13)**

Ichi ndi chidule cha uneneri mmavesiwa:

Ambuye adzabbwerera

Adzamanganso chihema cha Davide chimene chinagwa. Adzadzutsa zokugwa ndikumanganso Zolinga zochitira izi ndi zoti otsalawo a Edomu amfune Ambuye ndipo amitundu akhale ndi dzina la Ambuye pa iwo.

Pakuti ndi Ambuye amene achita izi zonse.

Linali dongosolo nla Mulungu lochokera pachiyambi cha dziko.

Kodi malembawa akutanthauza chiyani? Kodi kubwenzeretsa ndi chiyani? Kodi ndiliti kubwenzeretsaku kudzachitike nanga kudzachitika motani? Kodi zikutanthauzaji ku mpingo walero? Kodi zikugwirizana bwanji ndi kukonzekeretsedwa?

### **KODI KUBWENZERETSA NDI CHIYANI?**

“Kubwenzeretsa” kumatanthauza “kupanga chinthu chamtunthu, kuchipatsa moyo.” Ndi kubwereranso ku chiyambi kapena ku chimene chinalili.

### **KODI NDI CHIYANI CHIMENE CHIMABWENZERETSEDWA?**

Chihema cha Davide ndi chimene chikubwenzeretsedwa. Kufuna kumvetsa tanthauzo, tikuyenera kuonanso mbiri ya Likasa la Mulungu.

### **KUMANGIDWE KWA LIKASA:**

Mose anapatsidwa malangizo ochokera kwa Mulungu a mmene angamangire Likasa pamene anali pa phiri la Sinayi (Eksodo 26:10-22). Werengani kutalika kwake ndi zimene anapangira likasalo. Mulungu amalankhula za umulungu wake (I Petro 2:24). Magawo atatu a Golide, mtengo ndi golide amatikumbutsa kuti pa mulungu mmodzi wa anthu atatu.

### **ZOMWE ZINALI MU LIKASA:**

Mu likasa munali zinthu zitatu, zomwe zimaimira ku uzimu. Miyala imaimira chiyero, kuti Yesu ndi njira ya kwa Mulungu. Mpoto wa mana umaimira Mau a Mulungu. Yesu amene ndi Mau kapena choonadi. Ndodo ya Aroni kuimira kud zodza ngati Yesu amene ali moyo (Yohane 14:6).

### **KUFUNIKA KWA LIKASA:**

Likasa linali malo a pansu, a uzimu, achiyanjano ndi ubale ndi Mulungu. Ndi malo amene Mulungu amaonetserapo mphamvu, kupezeka ndi ulemerero.

### **MALO AKE A LIKASA:**

Pamene Likasa linatengedwa ku chihema cha Mose ku Shilo, silinabwererenso. Pamene linabwenzeretsedwa, linabwenzeretsedwa ku chihema cha Davide. Panali wansembe amene amapereka nsembe ya mwazi ku Shilo. Kupezeka kwa Mulungu kunali mu chihema cha Davide.

Pamene sembe za matamando, malambiro ndi nyimbo zimaperekedwa. Panalibe malo a kunja, ojera. Aliyense anali ndi mwayi wopita pamene Mulungu amapezekapo.

### **KODI KU UZIMU ZIKUTANTHAUZA CHIYANI?**

Kubwenzeretsa kwa chihema cha Davide ndi kubwenzeretsa kwa chihema cha ku uzimu, chimene ndi nyumba ya Mulungu, njira, choonadi ndi moyo amene ndi Yesu. Chihema cha uzimu chili ndi mautumiki atatu a Yesu monga mneneri, wansembe ndi mfumu. Ndi malo okhalamo mphamvu ya Mulungu, kupezeka kwake ndi ulemerero.

### **KODI CHIDZABWENZERETSEDWA LITI?**

Baibulo limatiuza kuti chihema cha Davide chidzabwenzersedwa “mmasiku akale.” Chihema cha Davide chidzamangidwanso mu nthawi zinthu zidzakhala zofana ndi nthawi imene idzabwenzersedwa, “mmasiku akale.”

Kodi masikuwo adzakhala otani? Davide anamanga chihema chake mu nthawi imene ulemerero ndi mphamvu ya kupezeka kwa Mulungu zidachoka. Kulambira kunasanduka mwambo. Mulungu anaiwala malo a kulambira chifukwa cha nyengo zoipa za uzimu za anthu ake:

**Koma anamuyesa napikisana ndi Mulungu Wam'mwambamwamba,  
Osasunga mboni zace; Koma anabwerera m'mbuyo, nacita zosakhulupirika monga  
makolo ao: Anapatuka ngati uta wolenda,  
Ndipo anautsa mtima wace ndi malo amsanje ao,  
Namcititsa nsanje ndi mafano osema.  
Pakumva ici Mulungu, anakwiya, Nanyozatu Israyeli. Ndipo anacokera cokhalamo  
ca ku Silo, Cihemaco adacimanga mwa anthu; Napereka mphamvu yace m'ukapolo,  
Ndi ulemerero wace m'dzanja la msautsi (Masalmo 78:56-61)**

Kodi mwaona nyengo za mu mpingo zofanana ndi zimene zikutchulidwa mmalemba? Ndiye kuti ndi nthawi ya kubwenzeretsa chihema cha Davide!

### **KODI CHIDZABWENZERETSEDWA BWANJI?**

Likasa lathu la kupezeka kwa Mulungu lidzabwenzersedwa mofanana ndi nthawi ya Davide:

#### **DONGOSOLO LOYENERA:**

Kumayambiriro Davide poyesera kubweretsa Likasa, analephera chifukwa sanatsate dongosolo. Mulungu analamula kuti likasa linyamulidwe pa mapewa a levi (atsogoleri a uzimu). Davide anayesera kuyendetsa likasa pa ngolo monga Afilisiti anachitira amene chiweruza cha Mulungu chinawapeza. Pamene Davide ananyamulanso likasa moyenera, iye anachita bwino.

Zina ndi monga malo okonzedwa (I Mbiri 15:1,3,12. Komanso chihema chatsopano (II Samueli 7:6). Osaiwalanso kusunghanitsa anthu a Mulungu pamodzi. Pamodzi ndi chiyeretso. Kubwerera ku kulambira kwenikweni.

### **KODI IZI ZIKUGWIRIZANA BWANJI NDI INU?**

Dongosolo lonse la mamangidwe ndi ulendo wa Likasa ndi chitsanzo chathu cha ife lero.

**Koma izi zinacitika kwa iwowa monga zoticenjeza, ndipo zinalembedwa kuticenjeza ife, amene matsirizidwe a nthawi ya pansi pano adafika pa ife (I Akorinto 10:11).**

Chihema chathu cha uzimu ndi kupezeka kwa Mulungu pa anthu ake. Ngati mukufuna kukumana ndi mphamvu ndi ulemmero wa Mulungu, tikuyenera kukonzekera ku uzimu pochita izi:

Kusatira dongosolo, kukhala ndi malo okonzedwa ndiwo moyo wathu komanso mpingo wathu. Komanso tikuyenera chihema chatsopano molingana ndi II Petro 1:13-14. Mpingo ndi gulu la anthu okhulupirira ndipo ndi chihema cha kupezeka kwa Mulungu. Werengani Mateyu 16:18.

**Koma mutu wafzi tanenazi ndi uwu: Tiri naye Mkuruwansembe wotere, amene anakhala pa dzanja lamanja la mpando wacifumu wa Ukulu m'Kumwamba, Mtumiki wa malo opatulika, ndi wa chihema coona, cimene Ambuye anacimanga, si munthu ai (Ahebri 8:1-2)**

Osaiwalanso kusunghanitsa anthu a Mulungu pamodzi. Izi ndi molingana ndi Machitidwe 14:27. Werenganiso Masalmo 133 ndi Machitidwe 2:1-4. Palinso chiyeretso zimene ndi ungwiro wa uzimu mu utumiki komanso kayendetsedwe ka chuma kabwino. Komaliza ndi kubwerera ku kulambira koono. Izi muziphunzira ku phunziro likubwerari.

### **KUBWENZERETSA NDI KUKONZEKERETSA.**

Ambuye analonjeza kubwenzeretsa chihema cha Davide, malo okhalamo Mzimu Wamulungu. Pakuti ndi kubwenzeretsaku, kumene kumabweretsa umodzi, chiyeretso, matamando ndi kulambira kwenikweni, kumene kumabweretsa nthawi yotsiriza ya kholora la miyoyo yobwera kwa Yesu khristu.

**Tsiku lomwelo ndidzautsa msasa wa Davide udagwawo, ndi kukonzanso zopasuka zace; ndipo ndidzautsa zogumuka zace, ndi kumanga monga masiku a kalelo; kuti alandire otsala a Edomu akhale colowa cao, ndi amitundu onse akuchedwa dzina langa, ati Yehova wakucita izi. Taonani akudza masiku, ati Yehova, akud wolima adzapezana ndi wodula, ndi woconda mphesa adzapezana ndi wofesa, ndi mapiri adzakhetsa vinyo watsopano, zitunda zonse zidasungunuka (Amosi 9:11-13)**

Pamene chihema cha Davide chabwzweretsedwa, pamakhala kholora lambiri, ndipo zokolala zambiri zimakhala chilowa kwa wina ndi wina. Mitundu komanso anthu amene sadziwa Mulungu amayamba kubwera kwa Ambuye.

Limalankhula za kumwamba kwatsopano ndi dziko latsopano limene Yohane anaona...

**Ndipo siridinaona Kacisi momwemo; pakuti Ambuye Mulungu Wamphamvuyonse, ndi Mwanawankhosa ndiwo Kacisi wace (Chibvumbulutso 21:22)**

**Ndipo ndinamva mau akuru ocokera ku mpando wacifumu, ndi kunena Taonani, cihema ca Mulungu ciri mwa anthu; ndipo adzakhalisa nao, ndi iwo adzakhala anthu ace, ndi Mulungu yekha adzakhala nao, Mulungu wao ((Chibvumbulutso 21:3)**

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

---

2. Perekani tanthauzo la “kubwengeretsa chihema cha Davide.”

---

---

3. Lembani mavesi amene akufotokoza za uneneri wa kubwengeretsa chihema cha Davide.

---

4. Kodi ndi liti limene chihema cha Davide chidzabwengeretsedwe?

---

5. Kodi chidzabwengeretsedwa bwanji?

---

---

6. Kodi kubwengeretsedwa kwa chihema cha Davide zikufanana bwanji ndi inu?

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## CHAPUTALA CHA 9

### OFUNIKA: WOLAMBIRA

#### ZOLINGA:

Pakutyha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kupereka tanthauzo la kulambira.
- Kufotokoza kulambira mu uzimu.
- Kufotokoza kulambira mu choonadi.
- Kulemba chidule chitatu cha zifukwa zimene timalambira.
- Kufotokoza ndondomeko ya kulambira.
- Kulemba zotsatira zisanu za kulambira.
- Kudziwa mitundu itatu ya kulambira.
- Kulemba mavesi amene amakamba za kukonzekera kulambira.
- Kulongosola chifukwa chimene timalambira.
- Kulongosola kumene timayenera kulambira.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Koma ikudza nthawi, ndipo tsopano iripo, imene olambira oona adzalambira Atate mumzimu ndi m'coonadi; pakuti Atate afuna otere akhale olambira ace. Mulungu ndiye mzimu; ndipo omlambira iye ayenera kumlambira mumzimu ndi m'coonadi (Yohane 4:23-24)**

### MAWU OYAMBA

Kubwenzeretsedwa kwa kukonzekeretsa pa kupezeka kwa Mulungu kudzabwera kudzera mu kulambira. Mulungu amafuna olambira! Mu chaputalachi, mupitiliza kuphunzira za kulambira, tanthauzo la kulambira ndi mawu ena. Mu phunziro lina muonanso za mmene mungalambirire Mulungu mu Mzimu ndi choonadi.

### MATANTHAUZO

Kulambira kumatanthauza kupereka ulemu, kopsyopsyona, kuyendera, kuchita mantha kapena kupereka ulemu. Kulambira ndi kuzindikira Mulungu, chikhalidwe chake, njira zake kapena ndi kutamanda, kuyamika chifukwa cha kuchita ntchito zabwino za chikhristu. Kutumikira kumatanthauzanso kulambira. Kulambira kumatanthauza kupereka kuyenera kwa munthu.



Kulambira si luso chidukwa Mulungu sagawana ulemerero wake ndi munthu wina. Sikuti ndi miyambo, mawu a chikhulupiriro, obwerezabwereza sabata ndi sabata.

Awa ndi mawu ena ogwirizana ndi kulambira mmalemba:

Kuthokoza: kumatanthauza kudzindikira, kuyamikira, kukondwera ndi kuvomereza.

Kutamanda: kukweza. Baibulo limakamba matamando mmadera ambiri. Imodzi yake ndi kuimba zoimbira.

Kupereka ulemu: kuyamikira, kukoma, kukhala pamwamba. Ndi mawu ena amene anagwiritsidwa ntchito pa ulemerero

### **UBALE WA PAKATI PA KUYAMIKA, KUTAMANDA NDI KULAMBIRA**

Pali kusiyana kwakukulu pakati mawuwa. Pamene mukulambira mukhoza kupezeka kuti mwayamba kuyamika kapena kutamanda molingana ndi buku la Masalmo. Komabe pali kusiyana kwa mawu atatuwa:

Kuyamika: kuyakhazika pa zimene Mulungu wachita. Baibulo limati osayiwala zabwino zimene wachita kwa inu.

Kutamanda: kumakhazika kwa Mulungu, amene ali ndi makhalidwe ake. Njira imodzi yotamanda Mulungu ndi kuyang'ana maina ake ndi makhalidwe ake.

Kulambira: uwu ndi utumiki wanu kwa Mulungu. Ambiri aife timatanganidwa ndi kutumikira Mulungu polalikira, kuphunzitsa ndi maphunziro ena. Koma utumiki wanu wofunika kwa Mulungu ndi matamando ndi kulambira.

### **MAGANIZO ENA**

Kulambira kumayerekeza kuti Mulungu alipo ndipo akhodza kudziwdwa ndi munthu. Baibulo limaphunzitsa kuti matamando ndi kulambira kukuyenera kuchitika poyera kapena mseli. Mfundo yaikulu mu kulambira ndi mtima wokhumba Mulungu. Chifukwa chimene kulambira kumalephera kuchitika mmipando ndi chifukwa choti kulambirako sikumachitia tsiku ndi tsiku kwa anthu. Iwo amene amalambira mmipingo ndi amene amalambira poyera komanso mseli. Kulambira ndi zotsatira za makhalidwe a kulambira, osati dongosolo longokonzedwa mu ola linalake. Matamando ndi malambiro si mwambo wag ulu la anthu ayi. Ndi machitidwe a munthu kwa Mulungu. Pamene timvana mmatamando ndi kukhala mmagulu, koma aliyense amalambira mwayekha.

**Potero mwa iye tipereke ciperekere nsembe yakuyamika Mulungu, ndiyo cipatso ca milomo yobvomereza dzina lace (Ahebri 13:15)**

## MZIMU NDI CHOONADI

Molingana ndi vesi lotsogolera mu phunziroli, kuti kulambira kukhale kovomerezeka kukuyenera kuchitika “mzimu ndi mu choonadi.” Yohane 4:23-24 amagwirizana ndi Mateyu. Yesu anawauza atsogoleri achipembedzo a nthawi yake:

Malemba amakamba za choonadi mu kulambira kwathu. Mphamvu ya Mulungu imaonekera mu mzimu wa kulambira kwathu. Monganso malemba ndi mphamvu ya Mulungu ndi zofunika pa kumvetsetsa kwa zinthu za uzimu, mzimu ndi choonadi ndi zofunikanso kuti kulambira kuvomerezeke.

### **Koma Yesu anayankha, nati kwa iwo, Mungolakwa a osadziwa malembo, kapena mphamvu za Mulungu (Mateyu 22:29)**

Kuti timvetse zimene Yesu amanena zokhudza kulambira, tiyeni tisanthule nyengo imene inamupangisa kunena zimenezi. Onaninso Yohane 4.

### **MZIMU:**

Munthu ali magawo atatu, thupi, moyo ndi mzimu. Thupi ndi looneka, moyo ndi maganizo ndi zofuna pomwe mzimu ndi wamkati. Mzimu wanu alinso ndi maganizo ngati moyo. Moyo ndi mzimu ndi zoyandikana koma ndi zosiyana. Baibulo limati mau a Mulungu ali akuthwa moti athu kuzisiyanitsa. Simungalambire ndi mzimu wanu pokhapokha utapatsidwa mphamvu ndi Mzimu wa Mulungu, choncho kulambira mu mzimu kumakhudzanso Mzimu Woyera. Pamene mukulambira, Mzimu wa Mulungu amachitira umboni mzimu wanu (Aroma 8:16).

Mzimu amatanthauza kuposa malambiro a mkati. Pokhala kuti munthu ali magawo atatu, pamene mulambira ndi mzimu, mukuyenera kulambiranso ndi moyo ndi thupi.

### **CHOONADI:**

Mawu oto choonadi amatanthauza kuulula, kutsekula osabisa. Kuti chinthu chinachake chikhale choona, chikuyenera kukumana ndi zinthu zitatu izi:

1. Chikuyenera kukhala cha wina aliyense: chikhudze aliyense
2. Chikuyenera kukhala chofanana: chifikire aliyense kaya osauka, olemera, wamkulu, mwana
3. Chikuyenera kukhala chosatha: chamuyaya

Kulambira kukuyenera kukhazikike pa choonadi chimene ndi chidziwitso chochokera mu kulingalira pa nthawi imene mumakhala ndi Mulungu. Mukuyenera kumvetsetsa chifukwa ndi chimene mukulambira. Ngati muchita bwino mu kalilikidwe kamene kamakhudza anthu ndi nkhani zanu mkufika poyamikilidwa mmalo molambira Mulungu. Ichi ndi chifukwa chake mukuyenera kudzipereka pa kuphunzitsa ndi kulalikira mawu mwaukadaulo.

Ngati mukufuna kulambira mukuyenera kudzipereka ku mau a Mulungu, osati maganizo anu. Chifukwa chimene Mulungu amafuna kulambira koono ndi...

**Inu muli ocokera mwa atate wanu mdierekezi, ndipo zolakalaka zace za atate wanu mufuna kucita. Iyeyu anali wambanda kuyambira paciyambi, ndipo sanaima m'coonadi, pakuti mwa iye mulibe coonadi. Pamene alankhula bodza, alankhula za mwini wace; pakuti ali wabodza, ndi atate wace wa bodza (Yohane 8:44)**

**ndipo mudzazindikira coonadi, ndipo coonadi cidzakumasulani (Yohane 8:32)**

## **NDI NTHAWI YANJI YOLAMBIRA**

Mukuyenera kulambira:

Tsiku ndi tsiku: werengani II Mbiri 30:21. Komanso machitidwe 2:46-47)

Mopitilira: werengani Masalmo 35:27 komanso Ahebri 13:15.

Mulungu atadzionetsera mwapaderadera: werengani kuonekera kwa Mulungu kwa Abrahamu mu Genesis 12. Komanso Eksodo 34. Pamene amadzionetsera mwapadera anthu analambira.

Mutalandira malonjezo a Mulungu: Genesis 13:14-18

Mutayankhidwa mapemphero: Genesis 24

Mutapatsidwa chisomo ndi anthu: Genesis 24:52

Mutachoka mu nyengo yovuta: werengani Masalmo 27:5, 116:17, 107:22.

Mumayesero ndi mu nkondo: onani Yobu

Mu zonse zimene muchita: mukuyenera kulambira Mulungu mu zonse zimene muchita popereka ulemerero kwa Mulungu.

Kwa muyaya: werengani Masalmo 52:9.

## **KODI MUNGALAMBIRE KUTI**

Mu mpingo: werengani Masalmo 22:22

Mnyumba mwanu: werengani Masalmo 149:5

Pamaso pa osakhulupirira: werengani Masalmo 40:3

Pamaso pa mitundu yonse ya anthu a mdziko: werengani Masalmo 108:3

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

---

2. Kodi kulambira ndi chiyani?

---

---

3. Fotokozani tanthauzo la kulambira mu mzimu.

---

---

4. Fotokozani tanthauzo la kulambira mu choonadi.

---

---

5. Perekani zifukwa zitatu zimene timalambira.

---

---

---

6. Longosolani dondomeko ya kulambira.

---

---

7. Lembani zotsatira zisanu za kulambira.

---

---

---

---

---

8. Dziwani mitundu isanu ya kulambira.

---

---

---

---

---

9. Perekani mavesi amene akukamba za kukpnzekera kulambira.

---

10. Longosolano nthawi imene tikuyenra kulambira.

---

11. Tchulani kumen tiyenera kulambira.

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## **CHAPUTALA CHA 10**

### **TINGALAMBIRE BWANJI**

#### **ZOLINGA:**

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kulemba chidule cha zimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza mmene tingalambire.
- Kulongosola ubale wa pakati pa moto, ulemerero ndi kulambira.

#### **VESI LOTSOGOLERA:**

**Mlemekezeni ndi lingaka ndi kuthira mang'ombe: Mlemekezeni ndi zoyimbira za zingwe ndi citoliro (Masalmo 150:4)**

### **MAWU OYAMBA**

Mu phunziroli muphunzira njira zolambira moopa Mulungu. Kulambira ndi imodzi mwa njira zazikulu Mbaibulo za kukonzekeretsa, pakuti kulambira koona kumalimbikitsa ndi kukonzekeretsa anthu a Mulungu.

### **TIMALAMBIRA BWANJI**

Izi ndi zina mwa njira za Mbaibulo za kulambira Ambuye:

#### **KUTUMIKIRA:**

Utumiki wanu waukulu wotumikira ndi matamando ndi malambiro. Komanso mumalambira pamene mukumutumikira iye pochita ntchito ya Mulungu mu choonadi. Mwachitsanzo njira imodzi yotumikira Mulungu ndi kuvomera maitanidwe ophunzitsa mitundu ya anthu.

#### **KUPEREKA:**

Mu chipangano chakale ndi chatsopano, amakamba za kupereka chuma ndi katundu wina ngati mbali imodzi yolambira.

**KUKHALA CHETE PAMASO PAKE:** Maganizo okhala chete amaonetsa mantha ndi kulingalira za mau a Mulungu. Zachariya 2:13.

#### **KULAMBIRA NDI MILOMO YANU:**

Sayance imanena kuti monga zala za munthu, munthu aliyenseso ali ndi mawu amene ndi osiyana ndi a wina. Mulungu amadziwa mawu anu ndipo amadikira mmamando anu a tsikundi tsiku. Izi ndi zina mwa njira zimene mungawiritse ntchito mawu anu kulambira Mulungu:

**MATAMANDO OLANKHULA:**

Werengani Ahebrei 13:15. Chinali chikhalidwe cha akhristu oyamba Luka 24:53.

**KULANKHULA MMALILIME:**

Werengani I Akorinto 14:14-18. Matamando anu amakhala angwiro pamene mukulambira mu chilankhulo chakumwamba. Ichi ndi chifukwa Paulo amakondwa chifukwa amachita kuposa aliyese.

**KUFUULA:** Werengani Yobu 38:7 ndi Masalmo 65:13

**KUSEKELERA:** Iyinso ndi njira yowonetsera matamando mmawu kwa Mulungu. Werengani Masalmo 126:1-3

**KUIMBA:** kuimba si mbali imodzi yokonzekera ulaliki ayi, koma ndi gawo limodzi lofunika pa kulambira. Werengani Akolose 3:16, Aefeso 5:19.

**KUTAMANDA NDI ZIDA ZOYIMBIRA:** Werengani Amosi 6:5. Ndipo pali mitundu itatu ya zida zoimbira. Werengani Eksodo 28:33-35, I Samueli 10:5 ndi Yesaya 5:12.

**KULAMBIRA NDI THUPI LANU:**

Pokhala magawo atatu a munthu, mukuyeneranso kumulambira Mulungu ndi thupi lanu. Nthawi zambiri timakana kuchita izi chifukwa sitimafuna kudzionetsera tokha. Timaopa ndipo sitifuna kuchotsa matama athu. Zina mwa zolepheretsa kulambira ndi matawa, kusamasuka, miyambo ndipo sitidziwa kuti ndi lamulo la Mulungu.

**KUIMA PAMASO PAKE:** Werengani II Mbiri 20:19, Masalmo 135:1-2

**KUKWEZA MANJA ANU:** Werengani Masalmo 63:3-4

**KUOMBA MMANJA:** Werengani Masalmo 47:1

**KUWERAMA KAPENA KUGWADA:** Werengani Genesis 24:48, Eksodo 4:31

**MOTO, ULEMERERO NDI MALAMBIRO**



Mu chaputala 3 cha phunziroli, munaphunzira za moto, ulemerero ndi kulambira Mulungu ngati zida zamphamvu yokonzekeretsa kutumikira Mulungu. Moto wa Mulungu uli ndi mphamvu yoyeretsa ndi cholinga chofuna kuvumbulutsa ulemerero wake. Chibvumbulutso cha ulemerero wake kumabweretsa kulambira koono pamene tikubwenzeretsa chihema cha Davide polambira mu mzimu ndi mu choonadi.

**Atatha tsono Solomo kupemphera, moto unatsika kumwamba, nunyeketsa nsembe yopsereza, ndi nsembe zophera; ndipo ulemerero wa Yehova unadzaza nyumbayi. Ndipo ansembe sanakhoza kulowa m'nyumba ya Yehova, popeza ulemerero wa Yehova unadzaza nyumba ya Yehova. Ndi ana onse a Israyeli anapenyera potsika motowo, ndi pokhala ulemerero wa Yehova panyumbayi; nawerama nkhope zao panso poyalidwa miyala, nalambira, nayamika Yehova, nati, Pakuti Iye ndiye wabwino, pakuti cifundo cace cikhala cikhali (II Mbiri 7:1-3)**

Pamene takhudzidwa ndi moto, mkulandira chibvumbulutso cha ulemerero wa Mulungu, ndi kuyamba kulambira mu uzimu ndi choonadi, pameneo mpamene mumalandira chitsitsimutso. Maphunziro atatu otsatirawa akukamba za chitsitsimutso chimene chimapereka mphamvu yokonzekeretsa anthu a Mulungu.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

---

2. Lembani chidule cha zimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza kulambira.

---

---

---

3. Longosolani ubale wa pakati pa moto, ulemerero ndi malambiro.

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa Bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

Masalmo ndi buku la malambiro a Baibulo ndipo limaphunzitsa zambiri zokhudza kulambira. Davide anati:

**Inu Mulungu, ndinu Mulungu wanga; ndidzakufunani m'matanda kuca:  
Moyo wanga ukumva ludzu la kwa Inu, thupi langa lilirira Inu,  
M'dziko louma ndi lotopetsa, lopanda madzi.  
Kuti ndione mphamvu yanu ndi ulemerero wanu, Monga ndinakuonani m'malo  
oyera (Masalmo 63:1-2).**

Davide sanazolowere zomapita ku kachisi wakale wafuka kumene samasangalalako ndipo kunalibe kupezeka kwa mphamvu ya Mulungu. Zitsanzo za Masalmo zimene zimaphunzitsa za matamando, werengani Masalmo chaputala cha 81, 149, 93, 100.

## CHAPUTALA CHA 11

### KODI CHITSITSIMUTSO NDI CHIYANI?

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kupereka tanthauzo la chitsitsimutso.
- Kufotokoza za mmene tingakonzekerere chitsitsimutso.
- Kuzindikira nthawi imene chitsitsimutso chimafunika.
- Kulongosola zizindikiro za nyengo yobwerera mmbuyo.
- Kupereka chitsanzo cha chipangano chatsopano cha munthu wa Mulungu amene anabweretsa chitsitsimutso.
- Kulemba chidule cha zotchinga za chitsitsimutso.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera (Machitidwe 2:38)**

#### MAWU OYAMBA

Palibe utumiki udzakhalabe okonzekeretsedwa popandapo kupezeka kwa Mulungu wa ulamuliro mu chitsitsimutso. Mu maphunziro awiriwa muona za chitsitsimutso, kusanthula mbiri ya Chipangano Chakale pa za chitsitsimutso cha Mbaibulo.

#### ZOMWE MUNTHU AMAKUMANA NAZO

Mpingo umene mumasonkhana ukhodza kukhala wakufa ku uzimu, komatu simungaone zinthu mwapagulu zimene mwanokha simunazione. Ngati chitsitsimutso chichitikira pagulu limene inuyo mumapezeka, mukuyenera kukumana nacho kaye nokha. Ngakhale chipentekosite chinayamba chafikira munthu kaye payekha.

Timapemphera, kusala ndi kupempha chitsitsimutso, koma ngati tichifuna pagulu, tikuyenera kukumana nacho patokha kaye.

#### TANTHAUZO LA CHITSITSIMUTSO

Chitsitsimutso si kuimba nyimbo mokweza kapena kulalikira uthenga wa gehena. Kapenanso si kuitanira anthu atsopano mumpingo. Kukula kwa mpingo ndi zotsatira za chitsitsimutso, koma osati chitsitsimutso. Chitsitsimutso si kufalitsa uthenga wabwino. Chitsitsimutso chimabwera pambuyo pa kulalikira uthenga wabwino, pamene wokhulupirira akufa atsitsimuka. Komaliza chitsitsimutso si mikumano yaikulu, pokhapokha ngati mikumanoyi yakhudzidwa ndi Mulungu.

Chitsitsimutso ndi ntchito yapadera ya Mulungu wa ulamuliro, amene kudzera mwa anthu amaphunzira ndi kugwiritsa ntchito mfundo za Mbaibulo mu Mau a Mulungu. Chitsitsimutso ndi kubwenzeretsa anthu a Mulungu, kuperekanso mphamvu kwa zinthu zimene zikhalitsa. Kubweranso kwa moyo.

### **KUKONZEKERA CHITSITSIMUTSO**

Monga mmene amachitira mlimi, amene amapempherera zokolora zambiri. Koma ngati sakonzekera munda wake, kuzala mbeu, kuthirira mbeuzo, ndiye kuti sakolora. Ndipo mulungu ndiye amene amabweretsa mvula, dzuwa ndi nyengo yabwino kwa mlimi.

Momwemonso chitsitsimutso, pakuti ndi kuyenda kwa Mulungu, koma kukolora chitsitsimutso tikuyenera kukonzekera potsatiramfundo za Mau a Mulungu. Chitsitsimutso ndi ntchito yothandizana ndi Mzimu Woyera ndi mmene anthu a Mulungu achitira kwa Mulungu.

### **KODI TIKUFUNA CHITSITSIMUTSO?**

Chitsitsimutso mu mpingo wa Chipangano Chatsopano chinayamba chifukwa cha kumwazikana kwa okhulupirira Kamba ka chizunzo, kuphedwa, mndende ndi zina. Ndi angati amene angagwe mkufa ngati Hananiya ndi Safira chifukwa cha chitsitsimutso choonadi? Kodi tikufuna chitsitsimutso?

### **NTHAWI YANJI TIKUFUNA CHITSITSIMUTSO?**

Chitsitsimutso ndi chinthu chofunika kwambiri, koma sichifunika ngati pali nyengo zabwerera mmbuyo. Werengani Yeremiya 1:3-4 ndi Miyambo 14:14. Werenganinso Yeremiya chaputala cha 2:5.

Kubwerera mmbuyo ndi tchimo lomuchotsa Mulungu mmoyo wako mkuyamba kukhala wekha. Zimakhala ngati nkhumba yobwerera ku masanzi ake (II Petro 2:21-22).

### **ZIZINDIKIRO ZA NYENGO YA KUBWERERA MMBUYO**

Izi ndi zina za zitsanzo za nyengo ya kubwerera mmbuyo. Santhulani mtima wanu pamene mukuwerenga izi:

1. Pamene pemphero lasiya kukhala lofunika mmoyo wanu.
2. Pamene chidwi chofuna choonadi cha Mbaibulo chatha ndipo mwayamba kudalira nzeru zanu.
3. Pamene maganizo ofuna zamuyaya atha
4. Pamene muzikhulukira nokha machimo anu ndi chilungamo mwa inu nokha.
5. Pamene zokambirana za uzimu zakhala zochititsa manyazi kwa inu.
6. Pamene mukonda zamasewero kwambiri mmoyo wanu
7. Pamene mulola tchimo opanda kutsutsika mchikumbumtima.
8. Pamene chiyero chatha mmoyo wanu.
9. Pamene musaka ndalama ndi zinthu zina kwambiri.
10. Malambiro amakhala ngati a chidzowezi.
11. Simusamala pamene dzina la Mulungu litchulidwa pachabe.
12. Maziko a umodzi sapereka chidwi kwa inu.
13. Madandaulo anu amakhala omveka kwa inu.
14. Pamene thupi lanu likulamulirani.
15. Pamene mukhala ndi makhalidwe a kudziko ngati moyo wanu.
16. Simukhumbira Mulungu mmoyo mwanu.
17. Mpingo wanu watsika ku uzimu.
18. Ngakhale za makhalidwe, chuma, za uzimu, ndale za dziko sizikukhuzani.
19. Pamene mtima wanu uli wouma.
20. Pamene mwataya mphamvu zanu za uzimu.

### **MUNTHU AMENE MULUNGU AMUGWIRITSA NTCHITO**

Yohane Mbatizi ndi chitsanzo cha munthu amene Mulungu anamugwiritsa ntchito kubweretsa chitsitsimutso. Mu nthawi ya Chipangano Chatsopano, Yohane Mbatizi anabweretsa uthenga wa kulapa koma makolo ake anauzidwa kuti “adzakhala wamkulu pamaso pa Mulungu.”

Timazitcha aneneri a Mulungu. Aneneri amakhala ndi zozizwa, koma chodziwika ndi chakuti amayenera kukhala ndi uthenga, monga mmene analili Yohane Mbatizi. Maulaliki a mantha ndiwo amene achulukira koposa odzudzula ndi olimbikitsa.

Maulaliki opanda mphamvu ndi osasunthika chifukwa anabadwa mmanda osati mimba. Ambiri achiritsa odwala, ndipo gome lasanduka malo onetsa mphatso ndi luso. Tikuyenera kulalikira ndi kuphunzitsa ngati munthu akufa kwa anthu amene akufa.

Mulungu akudzutsa anthu amene ali mseli mu nthawi ino, amene adzalankhula zinthu zamphamvu za choonadi cha mau a Mulungu chimene tiyenera kuchimva. Kodi mukufuna kukhala gawo limodzi la dongosolo la Mulunguli? Ngati ndi choncho koyamba muyenera kukumana ndi chitsitsimutso mwa inu nokha. Mwina simungasinthe zinthu mu mpingo wanu koma mutha kusintha moyo wanu.

## **ZOTCHINGA ZA CHITSITSIMUTSO**

Izi ndi zina mwa zimene zimalepheretsa Mulungu kupezeka mu mpingo wathu:

### **Utsogoleri:**

Atsogoleri amene salalikira mawu a Mulungu mwamphamvu. Amene sapemphera moyo wawo, kapena kuwerenga mawu a Mulungu ndi kuonetsera zamphamvu. Atsogoleri amene sasamala za nkhosa. Werengani Yoweli 2:15-18.

### **Mpingo:**

Makamaka ngati mpingo ukuyenedera pa miyambo ya anthu osati zimene Mulungu akufuna. Izi zimalepheretsa kuti choonadi cha Mulungu chisadziwike mu mpingowo.

### **Zotchinga zina:**

Pali zotchinga zina zimene zikhoza kupezeka mwa atsogoleri ndi mpingo. Machimo amatchinga chitsitsimutso, kaya zikupezeka mumpingo kapena mwa atsogoleri. Werengani Yesaya 59:1-2 ndi Miyambo 28:13.

Malingaliro ozisiya ponena kuti awa ndi masiku otsiriza choncho sitingayembekezere kuti zambwino zingakhaleko. Izinsu zimatchinga chitsitsimutso. Kusakhala ndi chidwi ndi Mau a Mulungu, kukana kudzichepetsa ndi kusafuna Ambuye kumatchinganso chitsitsimutso. Werengani Masalmo 78:42 ndi Mateyu 13:58.

Kusankhala ndi chidwi kumatchinganso chitsitsimutso. Anthu sakhala ndi chidwi ndi za Yesu ndi zosowa za anthu. Kusasamala za moyo wawo wa uzimu ndi kuyenda kwa Mzimu wa Mulungu kumatchinganso chitsitsimutso.

Komaliza, chisankho chatu chosafuna chimatchinganso chitsitsimutso: Kodi tikufunadi chitsitsimutso?

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Perekani tanthauzo la chitsitsimutso.

---

---

3. Kodi timakonzekera bwanji chitsitsimutso?

---

---

4. Nanga ndi nthawi yanji imene imafunika chitsitsimutso?

---

---

---

5. Lembani zizindikiro za nyengo yobwerera mbuyo mu phunziroli.

---

---

6. Perekani chitsanzo cha munthu amene Mulungu amugwiritsa ntchito mu Chipangano Chatsopano.

---

---

7. Lembani chidule cha zotchinga za chitsitsimutso.

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)



## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Mu phunziroli mwaphunzira za nyengo za kugwa za nthawi ya Israyeli mu Yeremiya 2. Ahebri 11 amakamba za okhulupirira amene anagonjetsa maufumu ndipo anasiya kamwa ya mikango. Tikuyenera kukumana ndi mphamvu ya Mulungu, osamangolankhula ayi.

## CHAPUTALA CHA 12

### ZITSITSIMUTSO MU CHIPANGANO CHAKALE

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kudziwa mfundo za chitsitsimutso mu Chipangano Chakale.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Koma izi zinacitika kwa iwowa monga zoticenjeza, ndipo zinalembedwa kuticenjeza ife, amene matsirizidwe a nthawi ya pansi pano adafika pa ife (I Akorinto 10:11)**

#### MAWU OYAMBA

Mulungu amapezeka mu dzikolo kudzera mwa anthu ake amene ndi omvera mfundo za Mmau ake. Phunziro la chitsitsimutso cha mu Chipangano Chakale limapereka mfundo zimene zitha kugwiritsidwa ntchito pokukonzekeretsani kutsitsimuka ndi mphamvu ya Mulungu mmoyo mwanu. Pali mau amene amatilimbikitsa...

**Koma izi zinacitika kwa iwowa monga zoticenjeza, ndipo zinalembedwa kuticenjeza ife, amene matsirizidwe a nthawi ya pansi pano adafika pa ife (I Akorinto 10:11)**

Muphunziroli muphunzira za chitsitsimutso cha mu Chipangano Chakale. Kenako muzaphunzira mfundo za chitsitsimutso kuchokera mu zimenezi zomwe mutha kuzigwiritsa ntchito mmoyo mwanu.

Umu ndi mmene phunziroli likhalire:

Malemba aperekedwa oti muth kuwerenga zokhuza chitsitsimutso.

Nyengo zimene zilipo zimene zimabwera pambuyo pa chitsitsimutso zafotokozedwa.

Zinthu zimene zinayambitsa chitsitsimutso zaperekedwanso.

Zotsatira za chitsitsimutso zasanthulidwanso.

Chifukwa cha ndondomeko ya phunziroyi, palibe mayeso odziyetsa nokha komanso kupitiliza kuphunzira.

### CHITSITSIMUTSO MU NTHAWI YA YAKOBO

Mavesi: Genesis 35:1-15

Nyengo zimene zinalipo:

1. Mutu wabanja unachoka pa ubale ndi Mulungu.
2. Dongosolo la banja silinali molingana ndi Baibulo
3. Panali nyengo yosauka ya uzimu.

Zimene zinabweretsa chitsitsimutso:

1. Zochitika zowawa zimene zinadabwitsa Yakobo: Genesis 35.
2. Chitsitsimutso chinayamba ndi Mau a Mulungu: Genesis 35:1

Zotsatira:

Chitsitsimutso chinachitika mnyumba. Ngati nyumba zathu zatsitsimuka, mipingo yathu idzatsitsimukanso!

1. Banja linachotsa milungu mkudziyeretsa wokha: Genesis 35:2.
2. Linadzindikira Mulungu woona: Genesis 35:3.
3. Anabwerera ku malo amene anakumana ndi za uzimu: Genesis 35:3.
4. Anamanga maguwa, nalapa, mkubwerera ku kulambira koona: Genesis 35:7.
5. Miyoyo yawo inasintha: Dzina la Yakobo linasintha mkuonetsa kusintha ku uzimu: Genesis 32:24-32
6. Yakobo analandira vumbulutso latsopano kwa Mulungu: Genesis 32:24-32

## **CHITSITSIMUTSO MU NTHAWI YA MOSE**

Malemba: Eksodo 32:1-35; 33:1-23; machaputala 34-35

Nyengo zimene zinalipo (zoyamba kunali atsogoleri a Mulungu, kudandaula, kukhumba za thupi)

1. Maso a anthu anali pa munthu. Eksodo 32:1
2. Kukana Mulungu woona: Eksodo 32:1
3. Kuchita zopanda pake
4. Chinyengo: Eksodo 32:7
5. Kukana Mau: Eksodo 32:8
6. Kuumitsa khosi: Eksodo 32:21-24
7. Kuda ena pa tchimo: Eksodo 32:21-24

Zinthu zimene zinabweretsa chitsitsimutso:

1. Zotsatira za machimo awo. Anapatsidwa mwayi wosankha moyo ndi imfa: Eksodo 32:25:28
2. Kupezeka kwa Mulungu kunachotsedwa: Eksodo 33:3-11
3. Pembedzero la Mose: Eksodo 32:11-14, 30-34; 33:12-16

Zotsatira:

1. Ulemerero wa Mulungu unadzala mu chihema: Eksodo 40:34-35
2. Amakonzekeretsedwa kupita ku Kanani: chaputala cha 40.
3. Anazipatula ku tchimo: Eksodo 33:7-11
4. Kupereka: Eksodo 33:6; 35:5,21-26,29
5. Anthu analapa: Eksodo 33:4-6
6. Pangano latsopano: Eksodo 34:11
7. Anapambana ku nkhondo: Eksodo 34:12-13
8. Anatsindika pa kulambira: Eksodo 34:14
9. Anasiya mafano: Eksodo 34:15-16
10. Chiyero cha munthu ndi gulu: Eksodo 34:12,15-17
11. Kusunga Sabata: Eksodo 34:21
12. Anakonzekera chihema cha Mulungu: kumapeto kwa buku la Eksodo.

### **CHITSITSIMUTSO MU NTHAWI YA SAMUELI**

Mabuku: I Samueli 7:1-17

Nyengo zimene zinalipo:

1. Panalibe mfumu ku Israyeli: Oweruza 17:6; 18:1; 19:1; 21:25
2. Panali chipembedzo chachinyengo: I Samueli 2:11-17 ndi 3:13
3. Khungu la ku uzimu: I Samueli 3:1 ndi 4:1-11
4. Kugonja ndi adani: I Samueli 4:3 ndi 7:3.

Dziwani: chitsitsimutsochi chinapitilira mpakana nyengo ya Eliya, Asa, Yehosafati, Hezekiya, Yosiya, Zerubabele, Yona ndi Nehemiya. Pitolizani kuona malemba, nyengo zimene zinalipo, zomwe zinabweretsa chitsitsimutso ndi zotsatira.

## CHAPUTALA CHA 13

### MFUNDO ZA MBAIBULO ZA CHITSITSOMUTSO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pantima.
- Kulemba mfundo 7 za chitsitsomutso zopezeka mu Chipangano Chatsopano.
- Kulemba mavesi amene amakamba za dongosolo la Mulungu la chitsitsimutso.
- Kulemba zinthu zinayi zimene okhulupirira ayenera kuchita ngati akufuna chitsitsimutso.
- Kulemba chidule cha zinthu zitatu zimene Mulungu adzachita.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Ndipo anthu anga ochedwa dzina langa akadzicepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zao zoipa; pamenepo ndidzamvera m'Mwamba, ndi kukhulukira coipa cao, ndi kuciritsa dziko lao (II Mbiri 7:14)**

#### MAWU OYAMBA

Mu chaputala ichi muphunzira mfundo za Mbaibulo za chitsitsimutso zochokera mu Chipangano Chakale.

### MFUNDO ZA MBAIBULO ZA CHITSITSIMUTSO

Palibe zitsitsimutso ziwiri zomwe ndi zofanana, koma mfundo izi ndi zopezeka mu Chipangano Chakale:

1. zitsitsimutso zambiri za muchipangano chakale zimabwera pamene moyo wa uzimu unalowa pansu.
2. chitsitsimutso chilichonse chimayamba mu mtima mwa munthu.
3. chitsitsimutso cha chipangano chakale chinakhazikika pa mphamvu ya kulalikira mau a Mulungu.

**Ndipo Eliya anayandikira kwa anthu onse, nati, Mukayika-kayika kufikira liti? ngati Yehova ndiye Mulungu, mtsateni iye; ngati Baala, mumtsate iyeyo. Ndipo anthu nnena kumyankha mau amodzi (I Mafumu 18:21)**

4. Kulapa ku machimo kumabwera pambuyo pa chitsitsimutso.
5. Panali kubwerera ku zinthu zenieni.
6. panali kubwerera ku kulambira Mulungu kwenikweni.

7. Chitsitsimutso chilichonse chimabwera ndi nthawi ya kupambana, chimwemwe ndi kuchita bwino.

## **DONGOSOLO LA MULUNGU LA CHITSITSIMUTSO**

Chipangano Chakale chimakamba za dongosolo la Mulungu la chitsitsimutso:

**Ndipo anthu anga ochedwa dzina langa akadzicepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zao zoipa; pamenepo ndidzamvera m'Mwamba, ndi kukhululukira coipa cao, ndi kuciritsa dziko lao (II Mbiri 7:14)**

Izi ndi zimene anthu ayenera kuchita ngati akufuna chitsitsimutso:

1. Adzichepetse okha:

Werengani Levitiko 26:40-41, II Mbiri 34:1-13

2. Apemphere:

Pemphero monga lachindunji, lofuna Mulungu, kuleka zoipa. Ndi kumufunsa Mulungu kuti atsitsimutse miyoyo.

3. Kufuna nkhope ya Mulungu:

Werengani Eksodo 33:7; Deuteronomo 4:29; Ezra 8:22; II Samueli 12:16; 21:1; I Mbiri 16:10-11; II Mbiri 7:14; 11:16; 15:4; 20:4; Masalmo 105:3-4; 24:6; 27:8; 40:17; 69:7; 70:5; Miyambo 28:5; Yesaya 51:1; Yeremiya 29:13; 50:4; Hoseya 3:5; 5:6-7,15; 7:10; Danieli 9:3; Zefaniya 1:6; Zakariya 8:21; Malaki 3:1.

4. Kusiya njira zawo zoipa:

Werengani Machitidwe 2, komanso Chibvumbulutso 22:16. Kulapa ndi mphatso ya Mulungu imene imakupangisani kusintha mayendedwe a moyo wanu. Onani Machitidwe 5:29-31. Kulapa kumakhudza kusiya ntchito zoipa (Ahebri 6:1-3). Ntchito zoipa ndi za chipembedzo zochitika pofuna kulandira kukondera kwa Mulungu chifukwa cha ntchito za munthu.

Ntchito zoipa ndi monga kulambira, kupereka chakhumi, ntchito zachifundo. Kulambira kuyenera kuchitika mu uzimu ndi choonadi apo bi zimakhala ntchito zokufa. Ntchito iliyonse imene sikhala ndi kuthekera kokhala ndi moyo mwa Mzimu wa Mulungu ndi yakufa imeneyo. Werengani Mateyu 7:6 ndi Miyambo 9:7-8.

Mukuyenera kusanthula moyo wanu wa uzimu, malingaliro anu, ndi njira zanu za utumiki ndi kulapa machimo omwe mumawachita ndi amene amabwera chifukwa simuchita zinthu zina zofunikira.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Lembani mfundo 7 za chitsitsimutso zimene zikupezeka mu Chipangano Chakale.

---

---

---

---

3. Lembani mavesi amene akufotokoza za dongosolo la Mulungu la chitsitsimutso.

---

---

4. Lembani zinthu zinayi zimene okhulupirira ayenera kuchita ngati akufuna chitsitsimutso.

---

---

5. Lembani zinthu zitatu zimene Mulungu amachita pamene anthu ake afuna chitsitsimutso.

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani zimene zikupezeka mu chipangano chatsopano zokhudza chitsitsimutso. Onani mawu a...

Yohane Mbatizi Mateyu 3:11

Yesu Marko 1:14-15; Luka 13:1-5

Petro Machitidwe 2:22-24

2. Onani mfundo za Mbaibulo za chitsitsimutso mu chipangano chakale, ngati mwapeza kodi mukuphunzira chiyani?

3. Pamene Mulungu Wayamba kugwira ntchito mu chitsitsimutso, Satana amakhazikitsa nkondo yoletsa kuyenda kwa Mulungu. Choncho tetezani chochitikacho.



## CHAPUTALA CHA 14

### WOKONZEKERETSA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotosgolera kuchokera pamtima.
- Kudziwa zitsanzo za munthu amene Mulungu anamugwiritsa ntchito kukonzekeeretsa mu chipangano chakale.
- Kulemba chidule cha zoyenera “wokonzekeeretsa.”

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Koma abale anga amene anakwera nane anasungunutsa mitima ya anthu; koma ine ndinamtsata Yehova Mulungu wanga ndi mtima wanga wonse (Yoswa 14:8)**

### MAWU OYAMBA

Phunziroli likuyamba ndi machaputala anayi ozondošana amene akuyang’ana za mmene Yoswa ndi mtundu wa Israyeli anakonzekeeredsa kulowa ndi kulandira dziko limene Mulungu anawalonjeza. Buku la Yoswa lili ndi mfundo zambiri zimene zitha kugwiritsidwa nchitho pamene mukonzekeeredsa kutengera mudzi, mzinda kapena mtundu wanu kwa Mulungu.

Phunziroli likyang’ana pa mtundu wa munthu umene Mulungu anamugwiritsa ntchito kukonzekeeretsa ena. Chaputala cha 15 chikuona za kukonzekeeretsa anthu asanayambe ulendo. Chaputala cha 16 chili ndi mfundo za kulowa mdziko. Chaputala cha 17 chikuona malangizo a mene angathanirane ndi kugonjetsedwa ndipo chaputala cha 18 ndi Nkhani za mizinda iwiri imene ikupereka mfundo zogonjetsa ziwanga za ku uzimu.

### DZIKO LA KANANI

Kanani linali dziko limene Mulungu analonjedza kwa Israyeli (Yoswa 1:2). Mulungu anawalonjeza kuti sadzawalephera pamene amakonzekeeredsa kukatenga dziko la kanani (Yoswa 1:5). Malonjezowa kuti akwaniritsidwe amayenera kukhala ndi chikhulupiro. Mulungu analonjedzanso iwo amene akulalikira uthenga ku dziko lapansi (Mateyu 28:19-20).

### WOKONZEKERETSA

Mulungu anamuza Yoswa kuti adzuke molingana ndi Yoswa 1:2. Ndi munthu wa mtundu wanjani amene amasankhidwa ndi Mulungu kuti akalankhule kwa anthu ake? Onani zimene zinali mwa Yoswa pamene Mulungu amamukonzekeretsa.

Yoswa koyamba anali wokhulupirira, dzina lake limatanthauza “Mulungu ndin Chipulumutso.” Analinso munthu amene...

Amamvetsera kulankhula kwa Mulungu: 1:1

Amalwaladi za kale, pamene Mulungu amamuza kuti Mose mtumiki wake wafa, amamuza Yoswa kuti aiwale zakale ndikupita kutsogolo. Kumbukirani mmene Paulo analankhula pa Afilipi 3:13.

Anadziwa gawo lake. Izi zikupezeka pa Yoswa 1:3-4. Yoswa anadziwa chimene chinali chake pamaso pa Mulungu. Baibulo limakamba za zimene okhulupirira alinazo monga chipulumutso, mphatso ndi chipatso cha Mzimu Woyera.

Anali wamphamvu ndi wolimba mtima: Molingana ndi Yoswa 1:5-6, Mulungu anapereka mphamvu, kupezeka kwake ndi chitetezo. Mukuyeneranso kukhala ndi makhalidwe abwino.

Anadziwa mafungulo a chipambano: Chinamupangitsa kupambana ndi Mau a Mulungu. Pakuti iye anali wochita mawu. Ndipo makhalidwe ake amagwirizana ndi Mau a Mulungu. Ifenso kuti tipambane tikuyenera kudalira Mau a Mulungu, ndipo makhalidwe azikhala ofanana ndi mawuwo.

Anali ndi Mzimu wa Mulungu pa iye: Yoswa anali munthu amene Mzimu wa Mulungu unali pa iye.

**Ndipo Yehova anati kwa Mose, Utenge Yoswa mwana wa Nuni, ndiye munthu mwa iye muli mzimu, nuike dzanja lako pa iye (Numeri 27:18)**

Anatsimikizika mwa Mulungu: Werengani Yoswa 1:11.

Anali munthu wachikhulupiriro: Werengani Numeri chaputala cah 13 mpaka 14.

Anali ndi mtima wa mtumiki: Izi zikupezeka pa Eksodo 33:11 ndi Yoswa 1:1.

Anali wodzadzidwa ndi nzeru: Werengani Deuteronomo 34:9

Anali munthu wophunzitsika:

**Ndipo Yoswa mwana wa Nuni, mtumiki wa Mose kuyambira ubwana wace, anayankha nati, Mose, mfumu yanga, aletseni (Numeri 11:28)**

Yoswa sanatenge chokhumudwitsa ngati langizo, koma anaphunzira kuchimenecho.

Anali wolimbikitsa anthu: Werengani Yoswa 1:1-9; 10-15; 16-18.

Anamtsata Ambuye ndi mtima wonse: werengani Yoswa 14:8

Amadziwa ngakhale kukhala yekha: amene amayenda mwachikhulupiriro amatsutsana ndi amene amayenda mwa zinthu zooneka. Werengani Numeri 13-14.

Amadziwa nkhondo: Werengani Eksodo 17:9-14. Kudziwa nkhondo kumeneku kunamuthandiza pamene amagonjetsa adani ku Kanani.

Anakumanapo ndi Mulungu: kumayambiriro kwa moyo wake. Werengani Deuteronomo 3:21-22.

Anadzodzedwa ndi Mulungu: Deuteronomo 34:9 amakamba za Mose amene Anaika manja pa Yoswa kuti atsogolere mtundu wa Israyeli. Numeri 27:18 ndi 22 amakamba kuti Mose anadzodza komanso kulamula Yoswa kugwira ntchito ya Ambuye.

Munthu amene amakonzekeretsa anthu ena amayenera kuyamba kudzodzedwa ndi kulamulidwa iyeyo. Pakuti ndi kudzodza kumeneko kumakonzekeretsa inu ku ntchito ya utumiki:

**Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika (Luka 4:18)**

Anakumana ndi ulemerero wa Mulungu: ulemerero wa Mulungu ndi wofunikira monga mmene mwaonera. Werengani Eksodo 24:13 ndi 17.

### **KUKHUDZA KWA WOKONZEKERETSA**

Moyo wa Yoswa unali ndi kukhudza kwa iwo amene anamuyandikira, kuti ngakhale atafa, atsogoleri komanso anthu amene anawaphunzitsa kutumikira Mulungu.

**Ndipo anthuwo anatumikira Yehova masiku onse a Yoswa ndi masiku onse a akulu akulu otsala atafa Yoswa, amene adaona nchito yaikuru yonse ya Yehova anaicitira Israyeli (Numeri 2:7)**

Kodi mukufunanso moyo wanu kukhala ndi kukhudza? Uwu ndi mtundu wa munthu umene Mulungu amafuna kugwiritsa ntchito ngati wokonzekeretsa. Kodi moyo wanu ukuchita bwanji molingana ndi Yoswa?

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Perekani chitsanzo cha munthu mu Chipangano Chatsopano amene Mulungu anamugwiritsa ntchito yomemeza anthu ena.

---

---

3. Lembani zomuyenereza munthu kukhala womemeza.

---

---

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Werengani buku la Yoswa kuti mudziwe zambiri pa maphunziro anayiwa.
2. Mupeza munthu mmodzi wofunika mu buku la Yoswa wotchedwa Kalebi. Anali munthu wokonzekeretsedwa. Amalimbikitsdwa kutenga phiri la Mulungu.

Kalebi anapita ku Kanani pansi pa utsogoleri wa Mose koma analibe malangizo panthawi imene amatenga phiri. Anakonzekera mmaganizo komanso ku uzimu.

## CHAPUTALA CHA 15

### WOKONZEKERETSEDWA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalach muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kufotokoza zitsanzo zinayi za kudziko za choonadi cha kuuzimu zofunika pa kukonzekeretsa.
- Kulemba zifukwa zitatatu zomwe okhulupirira sachita bwino kuchoka ku mkaka kupita ku nyama ya Mau a Mulungu.
- Kulongosola mmene wokhulupirira angachokere ku mkaka kupita ku nyama ya Mau a Mulungu.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Mwa ici, polekana nao mau a ciyambidwe ca Kristu, tipitirire kutsata ukulu msinkhu; osaikanso maziko a kutembenuka mtima kusiyana nazo nchito zakufa, ndi a cikhulupiriro ca pa Mulungu (Ahebri 6:1)**

### MAWU OYAMBA

Mu chaputala chathachi mwaphunzira zomuyenereza munthu amene akufuna kukhala womemeza anthu a Mulungu. Si onse amene ayitanidwa kukhala atsogoleri, koma aliyense akhoza kukhala Yoswa mu mzimu woonetsera makhilaidwe amene anali nawo. Mtsogoleri aliyense ayenera kukhala ndi otsatira.

Anthu a Mulungu ayenera kumemezedwa kuti atsatire atsogoleri a Mulungu kupanda kutero pamakhala chisokonezo. Muphunziro ili muphunzira mmene mungamemezera anthu kwa Mulungu.

### ANTHU OKONZEKERETSEDWA

Zinthu zinayi zinachita pomemeza Israyeli kuti agonjetse Kanani. Zinthu zinayizi zimene ndi zitsanzo ziziwika ku choonadi cha uzimu, zitha kukonzekeretsani ndi kukupangitsani kumemeza anthu ena. Werengani chaputala cha 5 cha Yoswa musanayambe kupitiliza.

Zinthuzi ndi monga:

1. Mwazi. Werengani Yoswa 5:10, iyi ndi nkhani ya pasaka amene amakamba za kuwaza mwazi. Ndi mwazi umene Yesu anakhetsa pamtanda kuombola ife ku machimo.

2. Lupanga: Onaninso Yoswa 5:2-9. Ndi lupanga la chizindikiro cha mdulidwe. Monga Abrahamu anachita kwanthawi mu chipululu ngati chizindikiro. Anthu amene akukonzekeretsedwa ayenera kukhala ndi chizindikiro pamoyo wawo. Werengani Akolose 2:11.

3. Chipatso. Werengani Yoswa 5:9-12. Mana amene Israyeli amya mu chipululu anasiya kugwa ndipo anthu anayamba kudya zipatso cha ku Kanani. Mana amachokera kwa Mulungu ndipo anali ofunika mu nthawi imeneyo popeza amakwaniritsa zosowa zawo mu chipululu. Koma io ndi nthawi ya chipatso cha mmunda. Chipatsochi chimalankhula za kukhwima ku uzimu. Werengani Ahebri 6:1 komanso I Petro 2:2. Koyamba munthu sakhala ndi luso la Mau a Mulungu. Onani Ahebri 5:13. Kachiwiri samagwiritsa ntchito zimene aphunzira. Onani Ahebri 5:12.

Mulungu adzkupatsani chidziwitso chatsopano ku Mau ake kufikira mudzayamba kuwagwiritsa mmoyo wanu.

Kachitatu, ndi athupi, Paulo anawauza a kumpingo wa akorinto. Werengani pa I Akorinto 3:13. Kodi mungachoke bwanji ku mkaka kupital ku nyama ya Mau a Mulungu?

Koyamba khumbirani mkhaka wa Mau kuti mukulu (I Petro 2:2. Kachiwiri ziperekeni kukufuna nyama, onani Miyambo 2:1-5.

4. Lupanga: Werengani Yoswa 5:13-15. Pamene nthawi ya nkhondo yayandikira, ndi pamene Yoswa anatenga udindo womenya nkhondo. Pamene Yoswa anaona munthu atatenga lupanga mmanja ake, anafunsa ngati anali wa adani kapena ayi.

Zimenezi ndi maziko anayi a kumemeza anthu a Mulungu.



## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.

---

---

---

2. Fotokoza zitsanzo zinayi za ku uzimu zimene ndi zofunikira pokonzekeretsa anthu.

---

---

---

---

3. Fotokozani zifukwa ziwiri zimene zimapangitsa okhulupirira kuti asachoke ku mkaka kupita ku nyama ya Mau a Mulungu.

---

---

---

4. longosolani mmene wokhulupirira angachokere ku mkaka kupita ku nyama ya Mau a Mulungu.

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kweikweni kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Miyambo 2:1-5 amaulula za ndondomeko yozindikira nyama ya Mau a Mulungu. Werengani ndimeyi ndi kulemba chidule chake mmawu anu:

---

---

---

---

---

---

2. Kodi zimenezi mungazigwiritse ntchito bwanji mmoyo wanu?

---

---

---

---

---

---

## CHAPUTALA CHA 16

### MFUNDO ZA KULOWERA

ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalach muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kulemba chidule cha mfundo za kulowera zopezeka mbuku la Yoswa.
- Kukonzekeretsa ena kugwiritsa ntchito mfundozi.

**VESI LOTSOGOLERA:**

**ngati zikwi makumi anai ankhondo okonzeka anaoloka pamaso pa Yehova kuthira nkhondo ku zidikha za Yeriko. (Yoswa 4:13)**

### MAWU OYAMBA

Anthu okwana 40,000 anakonzekeretsedwa ndi Yoswa. Anadutsa mtsinje wa Yordano kukonzekera nkhondo. Anthu sanasiye ulendo wawo wochoka ku Aigupto, anaoloka kufika ku dziko la malonjezano. Kutuluka ku uchimo ndi dongosolo la Mulungu pa inu. Akufuna akubweretseni ku dziko la malonjezano ndi madalitso. Akufuna akupangeni kukhala khristu wogonjetsa adani ndi kutengera mizinda ndi maiko kwa Ambuye.

Werengani chidulw cha Mose pa dongosolo la Mulungu pa Deuteronomo 6:23. Nkhondo imene Israyeli anakumana nawo ndi zitsanzo za nkhondo zimene timakumana nazo mu uzimu.

**Pakuti zonse zinalembedwa kale zinalembedwa kutilangiza, kuti mwa cipiriro ndi citonthozo ca malembo, tikhale ndi ciyembekezo (Aroma 15:4)**

Muphunziro ili muphunzira mfundo za kulowera zimene Israyeli anagwiritsa ntchito kugonjetsa Kanani. Mfundozi zikhoza kugwiritsidwa ntchito mmudzi wanu, mzinda kapena mtundu kwa Mulungu.

### KUFIKA POSABWERERA MMBUYO

Werengani Numeri chaputala 13 ndi 14. Pamene Israyeli anali pa malire a Kanani. Ndi pamene mumakonzekeretsedwa kapena kubwerera mbuyo pa moyo wanu wa uzimu. Atafika ananena kuti sakwanitsa kugonjetsa dziko (Numeri 13:31). Kusakhulupirira kudzakupangitsani kukhala pamodzi pa malonjezo a Mulungu.

## MFUNDO ZA KULOWERA

Izi ndi zina mwa mfundo za zimene ana a Israyeli anagwiritsa ntchito pamene amafuna kugonjetsa dziko la Kanani.

Kukonzekera nkondo: Iyi ndi mfundo yoyamba asanalowe mdziko. Werengani Yoswa 1:3, pamene Mulungu amamuuza Yoswa kuti akonzeka.

Kudziwa mdani wako: Kwas Yoswa mdani wake anali akanani. Mulungu anadziwa njira zothana ndi iwo. Werengani Levitiko 18. Mau a Mulungu amadziwa adani anu a dziko, thupi ndi mdierekezi. Baibulo lili ndi malangizo ambiri a mmene tingagonetsere adani athu.

Kudziwa mbali imene Mdani wanu ali: Ngati mukufuna kudziwa mdani wanu, mukuyenera kukumana naye mason di maso, osati mwamantha ayi. Musaope usinkhu wawo ayi. Pamene muyendabe mu chikhulupiriro.

Funani chitsimikizo cha kupezeka kwa Mulungu: Pakuti Likasa linali ngati chizindikiro cha kupezeka kwa Mulungu pakati pa Israyeli ku nkondo. Pamene Israyeli, anachimwa kupezeka kwa Mulungu kudachoka. Mukuyenera kuonetsetsa kuti pamene mukukonzekeretsedwa pa dongosolo la Mulungu onani kuti kupezeka kwa Mulungu kuli pa inu.

Dziwani kuti nkondo ndi ya Mulungu: Mobwerezabwereza, Mulungu amauza Yoswa ndi Israyeli kuti nkondo ndi ya Mulungu. Sanayenera kutenga dziko mwa nzeru, luso la iwo okha koma nkondo inali ya Mulungu.

Musadalire maganizo a umunthu: Yoswa akanakhala kuti amadalira maganizo a umunthu, sakanakwanitsa kutenga Yeriko pozungulira kapena pofuula. Pamene mukukonzekera zida za uzimu. Kaya nyengo itha kumaoneka yonyozeka, mukuyenera kudalirabe Mulungu.

**Pakuti maganizo anga sali maganizo anu, ngakhale njira zanu siziri njira zanga, ati Yehova (Yesaya 55:8)**

**Werenganinso I Akorinto 1:25,27,29**

Pamene Yoswa anadalira mphamvu ndi nzeru zake anakumana ndi mavuto. Werengani Yoswa 9:1-27.

Kuthana ndi zokhumudwisa osati kuteteza nkondo: Yoswa sanadikire adani kuti azawapute. Anamenya nkondoyo osati kungoteteza chabe nkondoyo. Okhulupirira ambiri amatenga nthawi yawo yambiri kulimbana ndi mmene mdani akubwerera osati kumenya kumene nkondoyo ndi kutenga dziko la malonjezano.

Mukhale ndi ndondomeko yoyenda bwino: Pamene munthu ali ndi dongosolo loyenda bwino, ndiye kuti mumayendabe. Sumakodwa ndi zinthu zina kapena ku zakale. Yoswa amayenda nwadongosolo mu Kanani. Ndipo amayendabe, mkumachita zimene Mulungu amamuza. Momwenso mpingo ukuyenera uziyenda bwino, pofalisa uthenga wabwino.

Limbanani ndi malinga ofunika: Njira imene Yoswa amamenyera nkondo inali inali yadongosolo. Onani Yoswa 9 ndi 10:28-43. Yoswa amalimbana malinga ofunika kwambiri a adani. Mukuyeneranso kulimbana ndi malinga enieni a moyo wanu.

Musadalire thupi: Mulungu samafuna Israyeli kuti adalire akavalo ndi magareta pa chogonjetso chawo. Kodi mwakhala mukudalira makavalo kapena magareta pofuna kugonjetsa adani, kumachita zinthu mmene dziko limachitira pomenya nkondo.

Limbanani ndi mizu yeniyeni osati pamwamba pa vuto: Israyeli anagonjetsa adani onse mpaka atatha onse. Dzikolo analilowa adani onse atathamo. Zikanakhala kuti anasiya adani mdzikomo, muzu wa tchimo ukanabuka mkuyamba kuwazunzanso. Musasiye ndi kulimbana ndi pamwamba pa nkondo. Musakhutitsidwe ndi chigonjetso chochepa, pitilizani kukonzekeretsa mphamvu zanu za uzimu kufikira mutalowa dziko la adani mkuligonjetsa kotheratu.

Mverani Mulungu: Chimodzi mwa zinthu zofunikira pa mfundo zolowera ndi kumvera. Baibulo limatiuza kuti...

**Monga Yehova adalamulira Mose mtumiki wace, momwemo Mose analamulira Yoswa; momwemonso anacita Yoswa; sanacotsapo mau amodzi pa zonse Yehova adalamulira Mose (Yoswa 11:15)**

Kuthekera kwanu kokonzeretsa ndi kulowa kumagwirizana ndi kumvera kwanu kwa Mulungu.

Pilirani ku nkondo: Ziginjetso zonse za Yoswa sanaginjetse mwachangu ngato Yeriko. Werengani Yoswa 11. Iye anamenya nkondo ndi mafumu a dzikomo kwa zaka 6 (onani Yoswa 11:18). Kupilira ndi kofunikira pogonjetsa malinga akulu, kuthamangitsa adani ndi kutenga zonse zimene Mulungu analonjeza kwa inu.

Khazikikani pa mgonjetsi osati chigonjetso: Yoswa anatsogolera Israyeli kulambira Mulungu atagonjetsa (Onani Yoswa 8:29-32). Nthawi zina timalakwisa pokamba zambiri za kupambana nkondo mmalo mwa iye amene wapereka chigonjetso.

Phunzirani kusintha kulephera mkukhala kupambana: Ana a Israyeli anagonjetsedwa ndi mzinda waung'ono wa Ai. Izi zikupezeka pa Yoswa 7-8. Chifukwa cha kufunika kwa mfundoyi, chaputala chonsechi chakhazikika pa mutuwu.

## **DZIKO LIMENE LASALA**

Werengani Yoswa 13:1-7. Pamene Yoswa amayandikira imfa panasalabe dziko limene limayenera kutengedwa ndi Israyeli. Israyeli amayenera kutsiriza zimene Yoswa anawatsogolera kuyamba.

Anthu amene amemezedwa amapitiliza kulowa kwa adani ngakhale mtsogoleri wawo wachotsedwa. Pofuna kukonzekeretsa anthu mukuyenera kuwachotsa chidaliro pa inu. Pamene Yoswa anafa, fuko lililonse la Israyeli linayenera kukamenya nkondo mdziko mmene munali adani. Chimene chikuchitika ndi gulu chikhalenso pa munthu mmodzi.

Mulungu analonjeza kuchotsa adani pang'onopang'ono (Eksodo 23:29-30). Simuchotsa adani anu a ku uzimu mu kanthawi kochepe. Mulungu amachotsa adani pang'onopang'ono mmoyo wanu. Izi zimapuna kudalira kwa Mulungu kopitilira.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Lembani chidule cha mfundo za kulowa mdziko zopezeka mbuka la Yoswa.

---

---

---

---

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Buku la Yoswa ndi buku la malangizo a mmene tingakhalire mmoyo wa nkondo ya uzimu.
2. Werengani Yoswa 12:7-24. Ndimeyi ili ndi zigonjetso zokwana 31 zimene Yoswa anagonjetsa adani. Kodi inu muli ndi zigonjetso zingati chaka chimenechi? Kodi mwagonjetsa bwanji adani anu?
3. Kukonzekeretsa ndi kulowa kwa ku Kanani kopezeka mbuku la Yoswa kumatsatira mlozo wa maphunziro a Harvestime International Institute.
4. Yoswa anayenera kupangitsa Israyeli kulowa mdziko la Kanani. Inunso mwaitanidwa ndi cholinga chomemeza anthu kuti alandire malonjezo a Mulungu.
5. Werenganinso buku la Yoswa kawiri ndi kuona mfundo za kulowa mdziko.



## CHAPUTALA CHA 17

### ATATHA KUGONJETA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kudziwa zifukwa zinayi za kugonjetsa mu uzimu.
- Kulemba chidule cha zotsatira za kugonjetsa ku uzimu.
- Kulongosola njira za kubwenzeretsa.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**ndipo akadzipulumutse ku msampha wa mdierekezi, m'mene anagwidwa naye, ku cifuniro cace (II Timoteo 2:26)**

#### MAWU OYAMBA

Mu phunziro ili muphunzira za mmene Israyeli anagonjetsera. Pamene mwakonzereketsedwa ndi Mulungu ndi kuyamba kutenga malo anu mu dzina lake, mumakumana ndi mavuto. Nthawi zina kugonjetsedwa kumene. Muphunzira zimene muchita mutagonjetsa.

#### NKHONDO YA YERIKO

Werengani zimene zinachita pa nkondo ya Yeriko pa Yoswa 6:16. Pamene mukuoloka mtsinje wa Yordani ku moyo wanu wa uzimu ndi kuyamba kutenga malo anu a Mulungu, mosakayikira mudzakumana ndi Yeriko, koma Mulungu adzakupatsani. Pamene timakhala ndi mavuto ndi pamene tagonjetsedwa.

#### CHIGWA CHA MAVUTO

Israyeli anakumana ndi mavuto pamene amafuna kugonjetsa mzinda wa Ai. Nkhani ya Ai ndi chigwa cha mavuto ikuyamba pa Yoswa 7:1 amene mawu ake otsogolera ndi “Koma” chaputala cha 8 anapezeka ali muvuto. Tisanthula zifukwa zimene zinapangitsa kuti agonjetsedwe ndi zimene anapanga kuti apulumuke. Tiona zifukwa zakugonjetsedwa zimenenso timakumana nazo.

#### 1. Mfundo:

Kuphwanja malamulo a Mulungu (Tchimo) kumabweretsa kulephera. Mulungu anauza Israyeli kuti asatengengo za ku Yeriko. Zimayenera kuperekedwa kwa Ambuye. Analamulidwa kuti asatenge zotembereredwa pakati pawo.

**Ndipo inu, musakhudze coperekedwaco, mungadziononge konse, potapa coperekedwaco; ndi kuononga konse cigono ca Israyeli ndi kucisautsa. Koma siliva yense, ndi golidi yense, ndi zotengera za mkuwa ndi citsulo zikhala copatulikira Yehova; zilowe m'mosungira cuma ca Yehova (Yoswa 6:18-19, 7:21)**

Tchimo nthawi zonse limayamba mmaganizo. Malingaliro atchimo amabwera pambuyo pa tchimo. Monga Akani amene anadzifunsa kuti “adzaona ndi ndani, adzadziwa ndi ndani? Monga mmene limakhalira tchimo, amangoona ubwino wake basi, osati kuipa kwake kosatha. Akani akanayang’ana ndi maso a chikhulupiriro osati a chilakolako, akanaona kuti zinthuzo zinali zodetsedwa, koma anazona ndi maso a kuthupi.

Adani anu a ku uzimu ndi dziko, thupi, ndi mdierekezi. Izi zimagwira ntchito limodzi kukuyesani ndi zilakolako za thupi, mason di matama a moyo uno. Mukayang’ana yesero ndi maso a chikhulupiriro osati a chilakolako, muzaona kuti zoletsdwazo ndi zotembereredwa.

## **2. Matama/kunyada**

Akani sanangokhala iye chokhumudwitsa mu nkhaniya vuto lawo. Pamene Yoswa anatuma kupita ku Ai kukaona mzinda, iwo anabwerera mkumuza Yoswa. Werengani Yoswa 7:3. Mu nkondo zimene timakumana nazo, timaona ngati tingakwanitse kuthana ndi mavuto aochepa tokha. Koma palibe kanthu kochepe ngati ili nkhani yolimbana ndi mdani, posafuna kudalira Mulungu. Pamene tayamba kudziona tokha ngati akutha, timaona kuti pali vuto ngakhale tikupita koopsa.

## **3. Mmene tikuzionera zinthu:**

Anthu amene anapita kukaona Ai, samaona zinthu ndi maso a uzimu. Amazona zinthu ndi maso a kuthupi. Werengani Yoswa 8:25. Pamene mukhala ndi anthu a kuthupi ku nkondo, mumaona zinthu molingana ndi umunthu wanu. Malangizo ake amakhala a umunthu ndipo mumagonjetsedwa.

## **4. Kupanda pemphero:**

Yoswa nayenso analakwisa kuti Israyeli agonjetsedwe. Anamvetsera pa lipoti lawo koma sanapemphere chifukwa cha lipotilo. Mwachangu anamemeza anthu okwana 3,000 kukathira nkondo ndi Ai. Molingananso ndi nkhani ya Gibiyoni kuti Mulungu anawachepetsa omenya nkondo. Pa Ai Mulungu akanachulukitsa ochepa kwamiri. Simungampatse malire Mulungu ndi kuganiza kuti Mulungu amayendera zakale. Ndi Mulungu watsopano, ndipo amachita zatsopano.

## **ZOTSATIRA:**

Werengani Yoswa 7:12, monganso mmene pamakhalira zikwakwa za kugonjetsa, pamakhalanso zotsatira za kulephera. Kuphwanya malangizo a Mulungu monga kunyada, kukhala kuthupi, kusapemphera kumakupangitsani kukhala kakasi mmaso mwa adani.

## **POPOLUMUKIRA:**

Pamakhala pothawira utatha kulephera. Ngakhale Satana akuikeni mu ukapolo, muzatuluka. Werengani II Timoteo 2:26. Pali njira zinayi zobwereranso pamene mwagonjetsedwa ndi mdani:

**1. Vumbulutso:** werengani Yoswa 7:10-11. Uku ndi kudziwa za vuto lako. Pamene Yoswa anakapemphera, Mulungu anamuululira za vuto lake, tchimo la Israyeli. Timakhala achangu kuona za vuto la mpingo koma sitidziwa udindo wathu pa vutolo. Aliyense ali gawo la thupi mwa Khristu. Tchimo la munthu mmodzi limakhudza thupi lonse.

**2. Kulapa:** Werengani Yoswa 7:10, Mulungu sanangoululu za vutolo komanso anamuuzza za mmene angathanirano nawo. Kudziwa za vuto sikukwanira kuthesa koma mukuyenera kuthana nawo vutolo. Ilipo nthawi yosiya kaye pemphero ndi kuyamba kuchita zimene Mulungu wanena kuti muchite. Werengani I Yohane 1:9

### **3. Kubwenzeretsa:**

Zitaonongedwa zodetsedwa, chiyero chinabweranso pakati pa anthu. Zimene zinawabweretsera mavuto zinakonzedwa. Pamene Mulungu wakuonetsani vuto lanu lanani, ndipo bwererani ndi kuchotsa zoletsedwa mmoyo wanu.

### **4. Kubwerera:**

Pamene ubale ndi Mulungu watha chifukwa cha tchimo, kukonzeka kumabwera pamene mwabwerera kumalo osiyana ndi a kugonjetsa mdani. Mayendedwe anu ndi Mulungu ayenera kukonzedwa. Mukuyenera kubwereranso ku malo a nkhondo ndi kuthana ndi vuto lanu.

## **KHOMO LA CHIYEMBEKEZO**

Pamene mwatsatira njira za Mulungu zokonzanso zinthu, iye amakutengerani ku chigwa cha vuto ndipo amachisinthira kukhala khomo la chiyembekezo. Onani Hoseya 2:15.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

2. Lembani zifukwa zinayi zimene zinapangitsa Israyeli kugonjetsedwa ndi mzinda wa Ai.

---

---

---

---

---

3. Lembani chidule cha kugonjetsedwa kwa Israyeli pa Ai.

---

---

4. Lembani njira zinayi za kukonzanso kuti mubwerere.

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## **KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Zifukwa zimene zinapangitsa Israyeli kogonjetsedwa ndi:

Kuchimwa

Kunyada

Maonedwe a zinthu

Kusapemphera.

Ganizirani zikukwa zina za kugonjetsedwa ku moyo wanu wa uzimu.

2. Werengani kuyankhula kwa Mulungu ndi Yoswa mwatsatanetsatane.

3. Santhulani za mmene munagonjetsedwera kale lanu.

## CHAPUTALA CHA 18

### NTHANO YA MIZINDA ITATU

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba Vesi Lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kufotokoza chifukwa ndiyani ndi kofunika kugonjetsa ziwanga za uzimu mmoyo wanu.
- Kudziwa mizinda itatu imene kwasala ziwanga zochepa za uzimu.
- Kulongosola zotsatira za kuzusiya ziwangazi mu mizindayi.
- Kulemba njira 7 zophera ziwanga za ku uzimu.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Panalibe Aanaki otsala m'dziko la ana a Israyeli; koma m'Gaza, ndi m'Gati ndi m'Asidodo anatsalamo ena (Yoswa 11:22)**

#### MAWU OYAMBA

Pamene Israyeli analowa mu Kanani, anapeza adani mdzikomo.

**Tinaonakonso Anefili, ana a Anaki, obadwa ndi Anefili; ndipo tinaoneka m'maso mwathu ngati zinsidzi; momwemonso tinaoneka m'maso mwao (Nomeri 13:33)**

Ku uzimu, adaniwa akuimira zovuta zazikulu zimene mumakumana nazo mu mpingo, mbanja, mu utumiki, ku ntchito komanso mumtima mwanu.

#### KUONONGA ZIWANGA

Mulungu anauza Israyeli kuononga zonse zopezeka mu Kanani kuphatikizapo ziwanga. Koma Israyeli sanamvere lamulo la Mulungu:

**...Koma simunamvera mau anga; mwacicita ici cifukwa ninji? Cifukwa cacenso ndinati, Sindidzawapitikitsa kuwacotsa pamaso panu; koma adzakhala ngati minga m'nthiti zanu, ndi milungu yao idzakhaira inu msampha (Oweruza 2:1-3)**

Ngati ziwanga mmoyo wanu sizinachokebe, zidzakhala misampha ndi minga ku uzimu wanu. Chifukwa cha ichi, phunziro ili likulongosola za njira zophera ziwanga zimene mumakumana nazo mmoyo wanu.

## NTHANO YA MIZINDA ITATU

### **Panalibe Aanaki otsala m'dziko la ana a Israyeli; koma m'Gaza, ndi m'Gati ndi m'Asidodo anatsalamo ena (Yoswa 11:22)**

A Anaki analoledwa kutsala mdziko amene ziwanga komanso a Kanani amene Mulungu analamula kuti aphedwe. Ku Gaza ndi Ashidodi, ndi kumene Israyeli anawatsatira mkukakhala. Pakuti ndi ku malo kumeneku kumene mavuto a Aisrayeli anachokera, ndipo nthano ya mizinda itatu. Gaza (Oweruza 16), Ashidodi (I Samueli 4-5) ndipo Gati (I Samueli 17)

Ziwanga zosagonjetsedwa mmoyo wanu zimabweretsa ziwanga zambiri. Ndipo mukaziyang'anira zimakhala zambiri ndipo mudzakhala ndi mantha aakulu. Mukhoza kukhala ndi zida za nkondo ndi kuphunzira nkondo ya uzimu, koma muzakhala malo amodzi kufikira mutapita malo a nkondo mkulimbana nawo.

## NJIRA ZOPHERA ZIWANGA

Zina mwa njira zimene mungagonjetsere ziwanga ndi izi:

### **Koyamba: kukonzekera:**

Kuti mukumane nawo mason di maso mmoyo wanu, mukuyenera kukonzekera mu nkondo zazing'ono zimene mumakumana nazo. Werengani I Samueli 17:34-36). Pamene mwakonzeka kukumana ndi adani, konzekani kukantha kochokera kwina. Zina zimachokera ku banja. Utsogoleri kumaoneka osatheka. Adaniwa amdzuka mkumakutonzani. Koma ngati mwakonzeka ku uzimu muzagonjetsa.

### **Kachiwiri: vomerezani:**

Davide anavomereza kuti kulimbika mtima kwake kunali mwa Mulungu. Werengani I Samueli 17:26,32,37 ndi 45-46.

### **Kachitatu: tsimikizirani:**

Werengani I Samueli 38:40, ngati mwakonzeka kupambana ndi adani mukuyenera kutsimikizira zida zanu. Mukuyenera kuvala zida zonse za nkondo (Aefeso 6:10).

### **Kachinayi: kulowa:**

Kukonzekera kwanu kutha kukhala bwino, ndipo zida zanu poambananso, ndipo chikhulupiriro chanu chabwino mwa Mulungu. Koma ngati muthawa mdani simungagonjetse. Palibe chigonjetso chotheke ngati mwangokhala pa malo amodzi mukmapereka zifukwa.

**Kachisanu: malingaliro abwino:**

Mukakumana ndi adani a mmoyo wanu, mukuyenera kukumana nawo ndi malingaliro abwino.

**Lero lino Yehova adzakupereka iwe m'dzanja langa, ndipo ndidzakukantha, ndi kukucotsera mutu wako. Ndipo lero ndidzapatsa mitembo ya makamu a Afilisti kwa mbalame za mlengalenga, ndi kwa zirombo za dziko lapansi; kuti dziko lonse likazindikire kuti kwa Israyeli kuli Mulungu. Ndi msonkhano wonse uno udzazindikira kuti Yehova sapulumutsa ndi lupanga, kapena ndi mkondo; pakuti Yehova ndiye mwini nkondo, ndipo iye adzakuperekani inu m'manja athu (I Samueli 17:46-47)**

Malingaliro a Davide sanali ofuna ulemerero kwa iye yekha kapena kuti mmene analili ndi mphamvu. Malingaliro ake anali wobweretsa ulemerero kwa Mulungu.

**Kachisanu ndi chimodzi: dongosolo la ngwiro:**

Mulungu anali ndi malingaliro angwiro pa chigonjetso cha Davide. Mdani wanu ndi wa mulungunso, choncho mungamugonjetse ndi zida zake basi osati zida za ku thupi. Werengani Aefeso chaputala cha 6.

**Kachisanu ndi chiwiri: kugonjetsa:**

Mukuyenera kugonjetsa mdani wanu. Izi zikutanthauza kuti mukuyenera kumuononga motheratu. Pamene muchita nkondo munjira ya Mulungu, muzagwiritsa ntchito njira zomwezo zimene mdani amagwiritsa ntchito kukuopsezani. Choncho mukuyenera kugonjetsa mdani kupanda kutero adzabweretsa mavuto kwa inu.



## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

---

2. Kodi ndi mizinda iti itatu imene Yoswa anasiyako ziwanga zochepa?

---

---

---

3. Kodi zotsatira za kusiya ziwanga zochepa mu mzinda zinali zotani?

---

---

---

4. Kodi chimachitika ndi chiyani pamene musiya adani wosagonjetsa mmoyo wanu?

---

---

---

5. Lembani njira 7 zophera ziwanga.

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## KUPITLIZA KUPHUNZIRA

1. Kodi muli ndi ziwanga zina zosagonjetsedwa mmoyo wanu? Ngati ndi choncho ndi ati? Alembeni.

---

---

---

Ganizirani za mmene mungagwiritsire ntchito njirazi pokupha ziwanga mmoyo wanu: Kukonzekera, kuvomereza, kutsimikiza, kulowa, malingaliro abwino, ungwiro, kupambana.

## CHAPUTALA CHA 19

### KUKONZEKERA KWA MPHATSO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa chaputalachi muyenera:

- Kulemba vesi lotsogolera kuchokera pamtima.
- Kufotokoza tanthauzo la kukonzekera kwa mphatso.
- Kukonzekeretsa mpingo wanu ndi mphatso za uzimu.
- Kulongosola mmene kawuniwuni amaululira ngati munthu ali malo oyenera mu utumiki.
- Kudziwa zofunika pogwiritsa ntchito mphatso za uzimu.

#### VESI LOTSOGOLERA

**Koma za mphatso zauzimu, abale, sindifuna kuti mukhale osadziwa (I Akorinto 12:1)**

#### MAWU OYAMBA

Phunziro lomaliza la ndondomeko ya kukonzekeretsedwa limakhudza za kukonzekeretsedwa kwa mphatso. Ngati muli mtsogoleri wa ena, ndiye kuti phunziroli ndi lofunika kwa inu. Pakuti lili ndi maphunziro amen endo ofunika a pamoyo watsiku ndi tsiku mu utumiki komanso ku uzimu.

#### KUKONZEKERETSEDWA KWA MPHATSO

Mpingo ukhonza kupangidwa mu njira zambiri molingana ndi khumbo la mpingowo ndi akulu ampingo. Komanso molingana ndi mmene mbusa mmene akufunira. Mipingo ina ilibe dongosolo ndipo zotsatira zake umagwa.

Kuti mukhale oona mtima, wamphamvu wa Mulungu, mpingo ukuyenera kukhala ndi dongosolo molingana ndi mphatso za mzimu woyera. Mphatsozi zimakonzekeretsa ntchito ya utumiki.

Utumiki uliwonse ukuyenera kukhala ndi dongosolo ndi kukonzekeretsedwa molingana ndi kuthekera kopatsidwa ndi Mulungu.

Kukonzekeretsedwa kwa mphatso ndi njira yokhala ndi dongosolo la anthu pa ntchito ya utumiki molingana ndi mphatso za mzimu woyera.

Pali magawo atatu a njirayi:

1. kutsogolera anthu kuzindikira mphatso zawo za uzimu.
2. kudziwa zosowa za utumiki

3. kuika anthu molingana ndi mphatso zawo.

**Gawo loyamba: kuzindikira mphatso za uzimu:**

Ngati mukufuna kutsogolera anthu kudziwa mphatso zawo za uzimu, ndiye kuti inu komanso anthuwo mukuyenera kutsogolera kuti anthu adziwe mphatso zawo.

Mwapemphero atsogolereni mamembala a mpingo wanu kudzera mu izi kuti adziwe mphatso zawo zimene zikupezeka mbukuli:

Kubadwa mwatsopano  
Kulandira mzimu woyera  
Kukhala ndi nzeru za mphatso za mzimu  
Kuonetsetsa magwiritsidwe ake  
Kufuna mphatso posala ndi kupemphera  
Kusanjika manja pa iwo kuti Mulungu aulure mphatso zawo  
Kuzisanthula okha pa chidwi chawo cha zauzimu  
Kusanthula kwa inu mtsogoleri  
Kusanthula mu mpingo  
Kuyankha mafunso a mphatso za uzimu.  
Kuzindikira mphatso zimene ali nazo  
Kuwapatsa zosowa za utumiki  
Kuwashandiza kuti mphatso zawo zigwirizane ndi zosowa za utumiki  
Kuchita kalondolondo pa utumiki wawo mderalo.

**Gawo lachiwiri: Kuzindikira zosowa za utumiki:** izi ndi zina zimene ndi zosowa za mu utumiki:

Kuyendera odwala, mamembala atsopano, okalamba, osauka, amundende.  
Ulaliki: wakhomo ndi khomo, misonkhano ya pamtetete  
Kalondolondo pa utumiki kwa anthu atsopano  
Tandizo lochokera kwa akuluakulu.  
Kuchereza alendo  
Utumiki kwa anthu osauka.  
Kuimba nyimbo  
Kupereka ulangizi.

**Gawo lachitatu: Ikani anthu molingana ndi mphatso.**

Ngati mwachita gawo loyamba ndi lachitatu, ndiye kuti mwachita...

1. ndandanda wa anthu a mumpingo ndi mphatso zawo.
2. ndandanda wa maudindo amene akuyenera kukhala ndi anthu, udindo wawo molingana ndi mautumiki komanso mphatso zawo.

Gwiritsani ntchito chigawo chimene chikupezeka popitiliza kuphunzira. Anthu ambiri amafuna apemphere kaye asanavomereze utumiki. Onetsetani kuti mwalemba zonse zokhudza utumiki ndi kuwapatsa. Ena amene akukana kumana nawoni nthawi ina ngati angavomerenso.

Ngati pali maundindo ena a utumiki amene alibe munthu, mukhodza kuchita ziwiri izi:

1. pempherani zokhudza kusiya utumikiwo kapena kulepheretsa moyenera kufikira munthu atapezeka
2. ngati utumikiwo ndi wofunika, ikanipo munthu amene ali ndi utsogoleri moyembekezera.

### **ZOFUNIKA POGWIRITSA NTCHITO MPHATSO**

Zimatenga nthawi kuti mukhale ndi dongosolo mu mpingo wanu ndi kuyamba kukonzekeretsa anthu molingana ndi mphatso za uzimu. Musakhumudwe pamene muona kuti anthu sakusantha, kumakhala ngati mmene analili zaka 40 zapitazo. Mu nyengo imeneyi, kumbukirani kuti chofunika ndi chokondi kwambiri. Werengani I Akorinto 12:31 ndi chaputala 13.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera kuchokera pantima.

---

---

---

2. Kodi kukonzekeretsa kofuna mphatso mkotani?

---

---

---

3. Lembani magawo atatu okonzekeretsa mpingo molingana ndi mphatso za uzimu.

---

---

---

4. Kodi mungadziwe bwanji kuti munthu ali malo oyenera mu utumiki?

---

---

---

5. Kodi nd zinthu ziti zofunika pogwiritsa ntchito mphamvu za uzimu?

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa akupezeka kumapeto kwenikweni kwa bukuli)

## MAYANKHO A MAFUNSO ODZIYETSA NOKHA

### CHAPUTALA CHA 1:

1. Koma Yesu anawaitana, nati, Mudziwa kuti mafumu a anthu amadziyesa okha ambuye ao, ndipo akuru ao amacita ufumu pa iwo.  
Sikudzakhala comweco kwa inu ai; koma amene ali yense akafuna kukhala warnkuru mwa inu, adzakhala mtumiki wanu (Mateyu 20:26)
2. Kupusisa mwa nzeru, kapena mwa ukadaulo.
3. Kukonzekeretsa ndi pamene munthu akukonzekera ntchito yomwe wapatsidwa. Mwa njira ina ndi zochita zimene anthu a Mulungu adzutsidwa ndi kuyamba kumgwirira ntchito Mulungu pofalisa uthenga wabwino.
4. Kukonzekeretsedwa ku uzimu kumasiya ndi kupusisa chifukwa kumapezeka mu mfundo za Mbaibulo ndipo kumasindika cholinga chake pa Mulungu osati pa munthu.  
Sikumakhazikika pa thupi kapena undekha, koma pa utumiki ndi lamulo.
5. Onaninso zokambirana zopezeka mu chaputala cha 1.
6. Tikuyenera kuika chidwi pa kukonzekeretsa kwa ku uzimu chifukwa ndi njira yokhayo yobweretsa zokolola mu uzimu ku dziko lapansi.

### CHAPUTALA CHA 2:

- 1 Pamenepo ndipo iwo akubalalitsidwa anapitapita nalalikira mauwo (Machitidwe 8:4).
2. Aefeso 4:11-16 amakamba za chifukwa chimene Ambuye anapereka mphatso za utsogoleri ku mpingo kuti akonzekeretse thupi la Khristu ku ntchito ya utumiki.  
Chifukwa chakuti Mzimu Woyera amakhala ndi kupereka mphatso za uzimu amatsimikiziranso za kukonzekeretsa thupi lonse la Khristu. Werengani Aroma 12:3-8 ndi I Akorinto 12:1-31.
3. Fanizirani mayankho anu ndi zomwe mwakambirana za kukonzekeretsedwa mu chaputala cha 2.
4. Fanizirani mayankho anu ndi omwe mwakambirana mu chaputala cha 2.
5. Fanizirani mayankho anu ndi omwe mwakambirana mu chaputala cha 2.

6. Fanizirani mndandanda wa zitsanzo zomwe mwakambirana mu chaputala cha 2.
7. Fanizirani chidule chomwe mwakambirana mu chaputala cha 2.

### **CHAPUTALA CHA 3:**

1. Atatha tsono Solomo kupemphera, moto unatsika kumwamba, nunyeketsa nsembe yopsereza, ndi nsembe zophera; ndipo ulemerero wa Yehova unadzaza nyumbayi. Ndipo ansembe sanakhoza kulowa m'nyumba ya Yehova, popeza ulemerero wa Yehova unadzaza nyumba ya Yehova. Ndi ana onse a Israyeli anapenyera potsika motowo, ndi pokhala ulemerero wa Yehova panyumbayi; nawerama nkhope zao pansi poyalidwa miyala, nalambira, nayamika Yehova, nati, Pakuti Iye ndiye wabwino, pakuti cifundo cace cikhala cikhali (II Mbiri 7:1-3).
2. Pali zabwino zokhudza moto wa kudziko lapansi. Monga kupatsa mphamvu komanso kutentha, kukonzera chakudya. Komanso phuluza ku nthaka limene limapereka manyowa. Moto umaononga zoipa, komanso kukopa anthu. Moto umayatsa moto unzake, koma umazima ngati suyasidwa mopitilira.
3. Moto wa Mulungu ndi umene unali pa tsiku la pentekosite. Ndi moto umene umamasula lilime lanu kuti muzilankhula mwamphamvu ndi kukwaniritsa lamulo lotumidwa.
4. Onani zomwe zikupezeka mu chaputala cha 3.
5. Onani zolinga za moto wa Mulungu mu chaputala cha 3.
6. Kubadwa mwatsopano, kulandira mzimu woyera, lorani moto ukonze moyo wanu, yatsani moto wina, pitilizani kuyatsa moto.

### **CHAPUTALA CHA 4:**

1. Nyamuka, wala, pakuti kuunika kwake kwafika, ndi ulemerero wa Yehova wakuturukira. 2 Pakuti taona, mdima udzaphimba dziko lapansi, ndi mdima wa bii mitundu ya anthu; koma Yehova adzakuturukira, ndi ulemerero wace udzaoneka pa iwe (Yesaya 60:1-2)



2. Ulemerero ndi mawu amene ali ndi matanthauzo ambiri mu chingerezi. Choncho amatanthauza kukongola, ulemu, kuwala, matamando, kuyenera. Pamene mawu a ulemerero akugwiritsidwa ntchito kwa Mulungu amakamba za umulungu wake, mphamvu yake, kukongola kwake ndi ungwiro.
3. Mulungu ndiye maziko a ulemerero.
4. Fananisani ndi zimene mwakambirana mu chaputala cha 4.
5. Fananisani ndi zimene mwakambirana mu chaputala cha 4.
6. Chiganizo ndi chonama. Ulemerero ndi mphatso yochokera kwa Mulungu.

#### **CHAPUTALA CHA 5:**

1. ndipo ulemerero wa Yehova udzabvumbulutsidwa, ndipo anthu onse adzauona pamodzi, pakuti pakamwa pa Yehova panena comweco (Yesaya 40:5)
2. Onaninso zokambirana mu chaputala cha 5.

#### **CHAPUTALA CHA 6:**

1. Yesu ananena naye, Kodi sindinati kwa iwe, kuti, ngati ukhulupira, udzaona ulemerero wa Mulungu? (Yohane 11:40).
2. Fananizani mayankho anu mu chaputala cha 6.
3. Pamene mukulemekeza Mulungu, Iye amaulula ulemerero wake kwa inu. Pamene mupereka ulemerero pa zimene wachita mumalandira ulemerero wokonzekeretsa utumiki wanu.

#### **CHAPUTALA CHA 7:**

1. Momwemo Aisrayeli onse anakwera nalo likasa la cipangano la Yehova ndi kupfuula, ndi kumveka kwa lipenga, ndi mphalasa, ndi nsanje zomveketsa, ndi zisakasa, ndi azeze (I Mbiri 15:28).
2. Monga chihema cha Mose, inunso ndi chihema cha Mulungu. Ngati mumanga moyo wanu wa uzimu moyenera ulemerero udzakhala pa inu. Mukachita mosiyana, ulemerero udzachoka.
3. Ebenezara, Afeki, Asidodi, Gati, Ekironi, Betisemesi, Kiriya-Yeromu ndi Yerusalemu.
4. Zokhuma, kustimikizika, chitsogozo, dongosolo.

### **CHAPUTALA CHA 8:**

1. Zikatha izo ndidzabwera, Ndidzamanganso chihema ca Davine, cimene cinagwa; Ndidzamanganso zopasuka zace, Ndipo ndidzaciimikanso (Machitidwe 15:16).
2. Kubwenzeretsedwa kwa chihema cha Davide ndi kubwenzeretsedwa kwa chihema cha moyo wanu wa uzimu, imene ndi nyumba ya Mulungu.
3. Lembani zomwe mwakambirana mu chaputala cha 8.
4. Chihema cha Davide chidzamangidwanso pamene nyengo zizafanana panthawi imene zimabwenzeretsedwa mmasiku akale.
5. Chidzabwenzeretsedwa mu ndondomeko.
6. Fanizirani zomwe mwaphunzira mu chaputala cha 8.

### **CHAPUTALA CHA 9:**

1. Koma ikudza nthawi, ndipo tsopano iripo, imene olambira oona adzalambira Atate mumzimu ndi m'coonadi; pakuti Atate afuna otere akhale olambira ace. Mulungu ndiye mzimu; ndipo omlambira iye ayenera kumlambira mumzimu ndi m'coonadi (Yohane 4:23-24)

2. Kulambira kumatanthauza kupereka ulemu, kuima mwa mantha, kugwada, kuwerama. Kulambira ndi kuzindikira Mulungu, chikhalidwe chake, njira zake pomtamanda pa zimene amachita.
3. Onani zomwe mwakambirana za kulambira mu uzimu mu chaputala cha 9.
4. Onani zomwe mwakambirana za kulambira mu choonadi mu chaputala cha 9.
5. Timalambira chifukwa cha chitsanzo cha kulimbikitsa ndi umuyaya wa tsogolo.
6. Ndongomeko ya kulambira ndi kukweza (Mulungu), kulemekeza (Thupi la Khristu) ndi kutumikira (Otayika).
7. Lembani zotsatira zisanu zopezeka mu chaputala cha 9
8. Mitundu isanu ya kulambira; kulambira kwa kulapa, kuvomereza, kupembedza, kudzipereka ndi kuchita nkhondo.
9. Ahebri 10:22
10. Onani zomwe mwakambirana mu chaputala cha 9.
11. Onani zomwe mwakambirana mu chaputala cha 9.

### **CHAPUTALA CHA 10:**

1. Mlemekezeni ndi lingaka ndi kuthira mang'ombe: Mlemekezeni ndi zoyimbira za zingwe ndi citoliro (Masalmo 150:4)
2. Chitsitsimutso ndi ntchito ya ulamuliro wa Mulungu mmalo mwa anthu ake amene aphunzira ndi kugwiritsa ntchito mfundo zopezeka Mbaibulo.
3. Tikuyenera kukonzekera potsatira mfundo zimene zikupezeka Mbaibulo. Chitsitsimutso ndi kugwira ntchito limodzi ndi Mzimu wa Mulungu ndi mmene anthu amachitira.

4. Chitsitsimutso nthawi zonse chimafunika, koma osati kwa amene anagwa.
5. Onani zimene mwaphunzira pa nyengo yakugwa mu chaputala cha 11.
6. Yohane Mbatizi mu Chipangano Chatsopano ndi chitsanzo cha anthu amene Mulungu anawapatsa chitsitsimutso.
7. Onani zomwe mwakambirana mu chaputala cha 11.

### **CHAPUTALA CHA 12:**

Palibe mafunso odziyetsa nokha.

### **CHAPUTALA CHA 13:**

1. ndipo anthu anga ochedwa dzina langa akadzicepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zao zoipa; pamene ndidzamvera m'Mwamba, ndi kukhulukira coipa cao, ndi kuciritsa dziko lao (II Mbiri 7:14)
2. onani mfundo 7 zomwe zikupezeka mu chaputala cha 13.
3. II Mbiri 7:14
4. Dzichepetseni, pempherani, funani Mulungu, siyani njira zanu zoipa.
5. Zinthu zitatu zimene Mulungu adzachita: kumva, kukhulukira machimo ndi kuchiritsa dziko lawo.

### **CHAPUTALA CHA 14:**

1. Koma abale anga amene anakwera nane anasungunutsa mitima ya anthu; koma ine ndinamtsata Yehova Mulungu wanga ndi mtima wanga wonse (Yoswa 14:8)
2. Yoswa

3. Anali munthu amene amamvetsera kwa Mulungu, kuiwala zakale, amadziwa magawo ake, wamphamvu komanso wolimba mtima komanso anakumana ndi Mulungu.

#### **CHAPUTALA CHA 15:**

1. Mwa ici, polekana nao mau a ciyambidwe ca Kristu, tipitirire kutsata ukulu msinkhu; osaikanso maziko a kutembenuka mtima kusiyana nazo nchito zakufa, ndi a cikhulupiriro ca pa Mulungu (Ahebri 6:1).
2. Onani zokhudza mwazi, mpeni, chipatso, ndi lupanga mu chaputala cha 15.
3. Zifukwa zimene okhulupirira zachoka ku mkaka kupita ku nyama ya mau a Mulungu ndi: kupanda luso la mau a Mulungu, samagwiritsa ntchito mau a Mulungu ndipo amakhala ku thupi.
4. Wokhulupirira angachoke ku mkaka kupita ku nyama ya mau a Mulungu pokhala okhumbira mkaka wa mau Mulungu, kudzipatsa mwambo omvera mau, ndi kudzipereka okha kufunafuna nyama ya mau a Mulungu.

#### **CHAPUTALA CHA 16:**

1. ngati zikwi makumi anai ankhondo okonzeka anaoloka pamaso pa Yehova kuthira nkhondo ku zidikha za Yeriko (Yoswa 14:3).
2. Onani zomwe mwakambirana mu chaputala cha 16.

#### **CHAPUTALA CHA 17:**

1. ndipo akadzipulumutse ku msampha wa mdierekezi, m'mene anagwidwa naye, ku cifuniro cace (II Timoteo 2:26).
2. Mfundo, kunyada, maonedwe a zinthu ndi kusapemphera.
3. Fanizirani ndi zomwe zikupezeka mu chaputala cha 17.

4. Vumbulutso, kulapa, kubwenzeretsa ndi kubwerera.

### **CHAPUTALA CHA 18:**

1. Panalibe Aanaki otsala m'dziko la ana a Israyeli; koma m'Gaza, ndi m'Gati ndi m'Asidodo anatsalamo ena (Yoswa 11:22).
2. Gaza, Gadi, Ashididi.
3. Onani chaputala cha 17.
4. Ngati ziwanga za moyo wanu zachotsedwa, zimakhala msampha ndi minga ku uzimu wanu.
5. Konzekani, vomerezani, tsimikizirani, lowani, malingaliro abwino, ungwiro, kupambana.

### **CHAPUTALA CHA 19:**

1. Koma za mphatso zauzimu, abale, sindifuna kuti mukhale osadziwa (I Akorinto 12:1)
2. Kukonzekeretsa akwa mphatso ndi njira yopanga dongosolo la gulu la anthu ku ntchito ya mulungu mogwirizana ndi mphatso za mzimu woyera.
3. Dziwani mpahtso zanu za uzimu, zosowa za utumiki, kuika anthu moyenera mphatso ndi zosowa.
4. Mwa nthawi pangani kawuniwuni wa mamembala a mpingo wanu. Muzaona kuti munthu wapezeka pamalo molingana ndi mphatso yake.
5. Chikondi.